


# IWO ODZOZEDWAWO

## PA NTHAWI YOTSIRIZA

 Moni, omvetsera. Tiyeni ife tiyankhule kwa Ambuye wathu tsopano. Mulungu Wamkulu, Mulengi wa miyamba ndi dziko lapansi, Yemwe Mwaumulungu wachita kutisankha ife nthawi ino mmawa uno, ya kupembedza kwa Inu. Ndipo mulole ife, Ambuye, mu mitima yathu tidzipereke tokha mwathunthu ku chifuniro Chanu Chaumulungu ndi kugwira ntchito kwa Mzimu Woyera mwa ife, kuti tibweretse icho chimene Inu mukanakhala nacho kuti ife tichidziwe. Chokhumba chathu ndi kuti tikhale Akhristu abwinoko ndi nthumwi zabwinoko za Inu. Inu mutapereka izi kwa ife mmawa uno, pamene ife tikuyembekezera pa Inu, mu Dzina la Yesu Khristu. Amenii.

Khalani pansii. [Winawake akuti, “Inu mukufuna kuchotsa zovala za pemphero?”—Mkonzi.] Inde.

<sup>2</sup> Ife tiri okondwa kwambiri kukhala tiri pano mmawa uno kachiwiri, mu—mu msonkhano wa Mfumu yaikulu. Ndipo ndife opepesa, ife, kachiwiri, kuti ife tiribe malo a anthu, koma ife tiri chabe. . . Ife tiyesa ndi kupanga zopambana zimene ife tingakhoze, pansii pa zochitika.

<sup>3</sup> Tsopano, ambiri ali nayo mipango ndi zopempha zayikidwa pamwamba pano kuti zipemphereredwe pa izo. Ndipo ine ndikungoziyika izo ku mbali imodzi; osati kuti ine ndikuzinyalanyaza izo, koma ine ndizipempherera izo ine nditatha pakulu. . . monga, ndi usikuuno. Ine nditero mmawa uno, ndiyeno usikuuno kachiwiri, pamene. . . Ndiye ine ndidzapemphera ndi kuyembekezera pa Mzimu wa Mulungu kwa machiritso, ndipo ndi pamene ine ndikanakonda kuti ndipempherere pa—mipango ndi zinthu.

<sup>4</sup> Ndipo pa zopempha zapadera, Billy anandipatsa izo, chimodzi chirichonse, kwa ine. Ziripo pafupi mazana atatu, ndipo ine ndinangochoka mu zipindazo ndiye. Inu mukuona, ine ndikumangotenga izo mofulumira basi, ndi mmodzi aliyense, yemwe ine ndingakhoze kufika kwa izo. Ndipo ine ndifika kwa izo mwamsanga basi momwe ine ndingakhozere kutero. Ine sindidzakhoza kutha kuwatenga iwo onse. Kungofikira mkati ndi kumutenga mmodzi, nkuti, “Ambuye, ndipo kodi akhala mmodzi *uyu*, ndi kukhala mmodzi *uyu*?” Basi monga choncho, chfukwa iwo ali, mmodzi aliyense, osowa, zopempha zenizeni; chinachake, mosakaika, zimene ife tiyenera kuzikamba palimodzi za izo. Ndipo ine. . . Mochepe, inu mukudziwa, nthawizina Mzimu Woyera ukhoza kunena chimodzi china

chimene ine ndinachiwerenga, chimene chimangokhala pa mtima wanga; ine ndimapita mmbuyo kwa icho kachiwiri, ndi kukasaka kupyola mmenemo mpaka ine nditachipeza icho. Ngati sichoncho, mwawamba chabe nkuzitenga izo.

<sup>5</sup> Tsopano, ife ndiponso tikufuna kunena, mmawa uno, ndi kuwalonjera iwo amene ali kunja mu zigawo zina za dziko. Ife tikufuna kuwalonjera anthu mmawa uno mwa njira ya kulumikiza kwa lamyu uku, ku Mzinda wa New York; Beaumont, Texas; Prescott, Arizona; Tucson, Arizona; San Jose, California; Connecticut; Gainesville, Georgia; ndi New Albany, Indiana; ku fuko lonse. Ife tikukulonjerani inu mu Dzina la Ambuye Yesu.

<sup>6</sup> Mmawa uno, mu Indiana, iwo uli mmawa wabwinoko. Ife tinali ndi mvula usiku watha imene inaziritsa nyengo. Ndipo ndife. . . Kachisi wadzaza, ndipo aliyense akuyembekeza, ndi ziyembekezero zazikulu, ku phunziro la Sande sukulu. Ndipo ine ndikudalira kuti madalitso olemeretsetsa a Mulungu akhala pa inu kunja uko.

<sup>7</sup> Ndipo ife tikuyembekeza, posachedwa momwe kungathekere, kuti tipange—njira imene ife tingakhoze kukhala nayo, pamene ife tingakhoze kubweretsa onse a ife palimodzi, mwinamwake pansi pa hema wamkulu, pamene ine ndikumverera kutsogozedwa kwenikweni kuti ndilalikire pa Mbale Zisanu ndi ziwiri zotsiriza izi mu Baibulo.

<sup>8</sup> Kotero tsopano, kotero kuti ife tisakhale motalika kwambiri pa phunziro lalikulu ili mmawa uno. . . Ine ndinafunafuna Ambuye, kuganiza, “Ine ndikanakhoza kunena chiyani?” podziwa kuti uwu ukhoza kukhala msonkhano wathu wotsiriza umene ife titi tidzakhale nawo konse. Kudza kwa Ambuye kuli pafupi kwambiri poyandikira!

<sup>9</sup> Ine ndikuwona, kutachitika kuneneratu kuja kunapangidwa mu California, kuli nyumba kunja uko, ndi malo, zikumira pa muyezo wa mainchesi makumi atatu pa ora, matabwa akuwazika ndi kuswekera mkati. Ndipo iwo sakudziwa chimene chikuchita izo. Ife tiri pamapeto. Nyumba za madola zikwi-zana, zikumira. Ine ndiri nazo zizembo zazikulu mu pepala, zithunzi, zimene ine ndikuyembekeza kuzibweretsa usikuuno, pamene ine ndikufuna kuyankhula pa chinachake pa izo usikuuno.

<sup>10</sup> Ndipo, ndiye, usikuuno ife tiri ndi pemphero la odwala. Pobwera mkati madzulo ano, faifi, sikisi koloko, kapena iliyonse imene iyo ili. Ife tati tiyambe molawirira, ine ndikuganiza, kotero anthu akhoze kupita molawirira, ndi kulandira makadi anu a pemphero. Ndipo ife tikhala tikupempherera odwala usikuuno, Ambuye akalola.

<sup>11</sup> Tsopano, nditatha kuganiza mwapemphero, “Ine ndiyenera kuchita chiyani?” podziwa kuti tsiku lina ine ndiyenera kuyankha chifukwa cha zimene ine ndinena pano. . . Ndipo ine ndasankha, kapena ndamverera kutsogozedwa ndi

Mzimu Woyera kuti ndiyankhule mmawa uno pa uneneri, kukhala ngati kutidziwitsa ife. Mwaona? Ndicho chinachake chimene ife. . . Ngati ife sitiri odziwitsidwa, ndipo chirichonse chimachitika mwawamba chabe, ife tiyenera kumadziwa zokhudza ichi. Mzimu Woyera wapereka izo kwa ife, kuti tiwachenjeze anthu za zobwera. Inu mukudziwa, Baibulo linati, kuti, “Mulungu sadzachita kanthu kupatula poyamba Iye atawawonetsa antchito Ake, aneneri.” Ndi—ndi momwe kuti Yesu anawachenjezera anthu, zomwe zikanati zidzachitike; momwe aneneri anawachenjezera anthu, zomwe zikanati zidzachitike. Ndipo icho chikutikakamiza ife tsopano, mu ora lalikulu limene ife tikukhalamo, kuti tiwone m’badwo umene ife tiri kukhalamo, ndi chimene chikuchitika, chimene chiti chidzachitike mu m’badwo uno. Kotero amodzi mwa maphunziro achirendo awa amene mwina ife tawawerenga nthawi zambiri, icho chinagwera pa mtima wanga kuti—kuti ndiyankhule kwa anthu zokhudza izo mmawa uno.

<sup>12</sup> Tsopano tiyeni ife titembenezire mu Mabaibulo athu ku Mateyu mutu wa 24 ndi kuwerenga gawo la Mawu. [M’bale Branham akuyeretisa ku mmero kwawo—Mkonzi.] Mundikhululukire ine. Ngati njira yo—yopezera nkhani yathu ya zokamba zathu ndi phunziro.

<sup>13</sup> Tsopano, kumbukirani ife tikuti tiphunzitse izi monga kalasi la Baibulo, mosafulumira. Tengani mapensulo anu ndi pepala. Ine ndiri nawo Malemba ochuluka ndawalemba pansi apa, amene—amene inu mungati mukhoze kuti muwalembe awa pamenepo. Ndiye nkupita kunyumba ndi kukawawerenga iwo, pakuti iyi ili ngati kalasi ya Sande sukulu, kuti ife tikakhoze kudziwa, ndi kukhala ochenjezedwa ndi kukonzekera maora amene ife tikukhalamo.

<sup>14</sup> Mu Bukhu la Mateyu Woyera. [M’bale Branham akuyeretisa kummero kwawo—Mkonzi.] Mundikhululukire ine. Ndime ya 24. . . Kapena, mutu wa 24, kani, kuyambira ndi ndime ya 15, ine ndikukhumba kuti ndiwerenge gawo la Mawu Ake.

*Ndipo pamene inu chotero muti mudzawone chotembereredwa chopululutsa, choyankhulidwa ndi Daniele mneneri, chitayima mu malo oyera, (yense yemwe awerenga, msiyeni iye amvetse:)*

*Ndiye asiyeni iwo amene ali mu Yudea athawire mu mapiri:*

*Msiyeni iye amene ali pa tsindwi la nyumba—tsindwi la nyumba asati abwere pansi kuti atenge chirichonse kuchokera mnyumba yake:*

*Ngakhale musati mumulole iye amene ali mmunda kuti abwerere mmbuyo kuti akatenge zovala zake.*

*Ndipo tsoka kwa iwo amene ali ndi mwana, ndi kwa iwo amene akuyamwitsa mu masiku amenewo!*

*Koma pempherani inu kuti kuthawa kwanu kusati kudzakhale mu chisanu, ngakhale pa tsiku la sabata:*

*Pakuti ndiye kudzakhala chisautso chachikulu, chonga chimene sichinakhalepo chiyambireni chake cha dziko mpaka ku nthawi iyi, ayi, ndipo sichidzakhalepo konse.*

*Ndipo kupatula masiku amenewo atafupikitsidwa, sipadzakhala mnofu uti udzapulumutsidwe: koma chifukwa cha osankhidwa masiku amenewo adzafupikitsidwa.*

*Ndiye ngati munthu aliyense adzanena kwa inu, Onani, kuno kuli Khristu, kapena uko; musakhulupirire izo ayi.*

*Pakuti pamenepo kudzawuka a Khristu abodza, ndi aneneri abodza, ndipo adzawonetsa zizindikiro zazikulu ndi zodabwitsa; mochuluka chotero kuti, ngati kukanakhala kotheke, iwo akanadzanyenga osankhidwa amene.*

*Taonani, ine ndakuuzani inu kale.*

*Chotero ngati iwo ati adzanene kwa inu, Taonani, iye ali mu chipululu; musati mupite kumeneko: onani, iye ali mu chipinda chobisika; musakhulupirire izo ayi.*

*Pakuti monga mphenzi imabwera kuchokera kummawa, ndi kuwalira ngakhale mpaka kumadzulo; koteru kudzakhala nakonso kudza kwa Mwana wa munthu kuli.*

*Pakuti kulikonse kumene kwafa nyama, kumeneko mphungu zidzasonkhanirako. . .*

<sup>15</sup> Tsopano, kwa phunziro, ine ndikanafuna kuti nditenge ndime ya 24, kuti ndigomezere pa ndime iyi mwa phunziro lathu la Sande sukulu mmawa uno. Ndipo mvetserani mwatcheru pamene ine ndikuwerenganso iyi, kachiwiri.

*Pakuti pamenepo kudzawuka a Khristu abodza, ndi aneneri abodza, ndipo adzawonetsa zizindikiro zazikulu ndi zodabwitsa; mochuluka chotero kuti, ngati kukanakhala kotheke, iwo akanadzanyenga osankhidwa amene.*

<sup>16</sup> Tsopano kwa phunziro mmawa uno, kapena mutu, kani, ine ndikufuna kuti nditenge: *Iwo Odzozedwawo Pa Nthawi Yotsiriza*. Ndilo phunziro limene ine ndikukhumba kuti ndiyankhulepo, kapena mutu: *Iwo Odzozedwawo Pa Nthawi Yotsiriza*.

<sup>17</sup> Ine ndikukhulupirira kuti ife tiri kukhala mu nthawi yotsiriza. Ine ndikuganiza pafupi aliyense yemwe. . . Wowerenga Lemba, kapena ngakhale wo—wokhulupirira,

akudziwa kuti ife tiri tsopano pa mapeto a mbiriyakale ya dziko. Sipadzakhala ntchito yolembera iyo, chifukwa sipadzakhala aliyense kuti aiwerenge iyo. Ndi pa mapeto a nthawi. Ndi liti, ine sindiri kudziwa. Basi ndi motalika chotani izo ziti zidzakhale, palibe ngakhale Angelo a Kumwamba akudziwa miniti imeneyo kapena ora. Koma ife tawuzidwa kale ndi Ambuye Yesu, kuti, pamene zinthu izi zimene ife tikuziwona tsopano zikuyamba kufika pomachitika, ndiye kuti titukulire mmwamba mitu yathu chifukwa chiwombolo chathu chiri kuyandikira pafupi. Tsopano, chimene “kuyandikira pafupi” amatanthawuza, ine sindiri kudziwa. Kukhoza kutanthawuza . . .

<sup>18</sup> Monga azasayansi ananena tsiku lina, pa televizioni, akuyankhula za zikwi zazikulu-za-mamailosi zikuswekera mkati mu dziko lapansi zimene ziti zidzatitimire. Iye anali atafunsidwa funso, “Ilo likanakhoza kutitimira kumeneko?” Ndiye Los Angeles, Gombe la Kumadzulo. Ndipo ambiri a inu munawona momwe iwo anatsatira izo ndi zopimira, ndipo anapita mmwamba kupyola . . . nzoswekera mkati pansi pa San Jose, zinapita kuwoloka mpaka ku Alaska, kupita kupyola Zilumba za Aleutian, pafupi mailosi mazana awiri kunja mpaka ku nyanja, ndi kubwerera mmbuyo zinapita ku San Diego, kunapita mozungulira kuseri kwa Los Angeles, ndi kubwera mpaka kumeneko, thumba lalikulu.

Ndipo zivomezi zonse izi zimene ife takhala tiri nazo ndi phala lamoto likugunda chidzenje chakuya chachikulu ichi, monga, mmenemo. Ine sindingakhoze kutchula dzina limene iwo—iwo amazitcha izo. Komabe, pamene ilo ligwedezeka, ilo limapereka zivomezi izi zimene ife takhala tiri nazo kwa zaka ku Gombe la Kumadzulo. Tsopano ilo lang’aluka njira yonse mozungulira. Ndipo asayansi anati, chimodzi . . .

<sup>19</sup> Munthuyo anati kwa mzake, “Ilo likanakhoza kugwera mkati?”

Iye anati, “Osati ‘likanakhoza,’ koma ilo lidzatero.”

Anati, “Koma osati mu m’badwo wathu, mwinamwake?”

Anati, “Mu maminiti asanu otsatira, kapena zaka zisanu zotsatira. Ife sitikudziwa kungoti liti.”

<sup>20</sup> Sabata lino, ananditumizira ine zolembe zazikulu mu pepala, za manyumba aakulu a madola chikwi-zana akuchita timaphokoso ndi kung’aluka, anthu akusunthira kutali. Ndipo iwo sakudziwa momwe angaziyimitsire izo. Palibe njira yoti nkuyimitsira izo. Mwaona, Mulungu akhoza kuchita chirichonse chimene Iye akufuna kutero, ndipo palibe aliyense angakhoze kumuuzza Iye momwe angachitire izo.

<sup>21</sup> Inu mumamanga manyumba, inu mukhoza kupanga zinthu zasayansi, ndipo Mulungu ndi mlengi wa sayansi. Inu mumuletsa motani Iye? Iye akhoza kuwononga dziko lapansi mmawa uno ndi utitiri ngati Iye akufuna kutero. Inu mukuzindikira, Iye

akhoza kuyankhula utitiri kuti ukhalepo, ndipo iwo kuti ukhale mailosi makumi anai kuya mu nthawi ya theka la ora, mwaona, palibe ayi. . . ndi kuwadyera anthu pa nthaka. Iye ndi Mulungu. Iye amangochita momwe Iye afunira. Iye ali wochitamwayekha, mwa Iyemwini.

<sup>22</sup> Tsopano, powona kuunjikizana konse uku kwa umboni, kuti ora limene ife tiri kukhalamo tsopano, ine ndikuganiza ndi chinthu chabwino kuti tibwereze zinthu izi ndi kuti tizijambule izo apa, pakuti Zisindikizo zatsegulidwa kale, ndi kuti tipeze choonadi cha zinthu izi, monga Mulungu wakhala waulemu chotero kwa ife, ndi chisomo Chake, kuti atiwonetse ife zinthu izi.

<sup>23</sup> Ine ndikufuna inu kuti muzindikire apa mu Mateyu 24, Yesu anagwiritsa mawu a “aKhristu,” a-K-h-r-i-s-t-u, “aKhristu.” Osati Khristu, koma “aKhristu,” ambiri, osati mmodzi. “aKhristu.” Chotero, mawu *Khristu* amatanthauza “Iye Wodzozedwayo.” Ndiyeno ngati ndiwo “odzozedwa,” sipadzakhala osati yekha, koma ambiri, odzozedwa, “Iwo odzozedwawo.” Mwaona?

<sup>24</sup> Mwina awake, ngati Iye akufuna kuti aziswe izo kotero ife tikanati mochuluka kapena mwapang’ono timvetse bwinoko izo, Iye akanati, “Mu masiku otsiriza pamenepo kudzauka iwo odzozedwa, mwabodzawo.” Tsopano, izo zikuwoneka pafupifupi zosatheka, mwaona, mawu a “odzozedwa.” Koma zindikirani mawu otsatira omwe, “ndi aneneri abodza,” a-n-e-n-e-r-i, ambiri.

<sup>25</sup> Tsopano, *iye wodzozedwayo*, ndi, “yemwe ali ndi uthenga.” Ndipo njira yokhayo imene uthenga ungakhoze kuti ubweretsedwe ndi mwa yemwe ali *wodzozedwa*, ndipo ameneyo akanakhala ali mneneri, wodzozedwa. “Pamenepo padzauka aphunzitsi odzozedwa mwabodza.” Mneneri amaphunzitsa chimene uthenga wake uli. Aphunzitsi odzozedwa, koma anthu odzozedwa okhala ndi kuphunzitsa kwabodza. Iwo odzozedwawo, “aKhristu,” ambiri; “aneneri,” ambiri. Ndipo ngati pamenepo pali chinthu chotero monga k—Khristu, mmodzi, ndiye awa akanayenera kuti akhale “iwo odzozedwawo,” amene uneneri wawo wa zomwe iwo anali kuphunzitsa ukanakhala kusiyanako, chifukwa iwo ali iwo odzozedwawo, odzozedwa.

<sup>26</sup> Tsopano, ndi phunziro la Sande sukulu, ife tikufuna kuti—kutiyese kubweretsa izi ku chiwonetsero chenicheni, mwa Malemba, osati mwa zimene winawake wanena za izo, koma kuwerenga Malemba kokha.

Inu mukhoza kunena, “Izi zingakhoze kukhala motani? Akanakhala iwo odzozedwawo. . .”

27 Kodi iwo anali chiyani? “aKhristu,” a-K-h-r-i-s-t-u, odzozedwa. “aKhristu, ndi aneneri abodza.” Iwo odzozedwawo, koma aneneri abodza!

Yesu ananena, kuti, “Mvula imavumbira pa olungama ndi osalungama.”

28 Tsopano, winawake akhoza kunena kwa ine, “Kodi inu mukukhulupirira kuti kudzoza uko pa anthu amenewo kukutanthauza kuti iko ndi kudzoza kwa Mzimu Woyera?” Inde, bwana, Mzimu Woyera weniweni wa Mulungu pa munthu, ndipo komabe iwo ndi abodza.

Tsopano mveterani mwatcheru ndi kuwona zimene Iye ananena. “Ndipo iwo adzasonyeza zizindikiro ndi zodabwitsa, mochulukwa chotero kuti izo zikanadzanyenga Osankhidwa amene ngati kukanakhala kotheka.” Ndipo iwo ali odzozedwa ndi Mzimu Woyera weniweni. Ine ndikudziwa kuti izi zikumveka mopusa kwambiri, koma ife titenga nthawi ndi kufotokoza izo mwa Mawu, kuti ndizo mwamtheradi PAKUTI ATERO AMBUYE, Choonadi.

29 Tsopano tiyeni titembenezire mu Mabaibulo athu, miniti yokha, ku Mateyu mutu wa 5, ndipo kuyambira ndi—ndime ya 45, ndi kuwona tsopano pamene ife tikuwerenga kwa mphindi zingapo pa Malemba awa. Ndiyeno, titatha ife kufika apa, chifukwa, ife tikupatsani inu...Kotero inu, ngati ife tilephera kuti tiwerenge zonse za izo, ndiye inu mutenge Baibulo lanu; ndi—ndipo aponso inu mukhoza kukawerenga izo titatha kuchoka kuno ndipo inu mutapita kwanu, ndipo—ndipo inu mukawerenge zimene Baibulo likunena zokhudza izo.

30 Tsopano kuti titenge nthawi yathu, kuti titenge—mfundo yokhazikitsirapo, chifukwa ine ndikupanga neno pano limene liri lonyumwitsa. Mzimu Woyera ungakhoze bwanji kumudzoza mphunzitsi wabodza? Koma ndizo zimene Yesu anati zikanadzachitika.

Tsopano, Mateyu, mutu wa 5, ndime ya 45, tiyeni tiwerenge tsopano. Tiyeni titenge, kuyambira m—mmbuyo pang’ono mwa iyo, ya 44.

*Koma Ine ndinena kwa inu, Kondani adani anu, dalitsani iwo amene akutembererani inu, chitirani zabwino kwa iwo amene amakudani inu, . . . apempherereni iwo amene amakugwiritsani inu ntchito monyoka, ndi kukuzunzani inu;*

*Kuti inu mukakhoze kukhala ana a Atate wanu amene ali kumwamba: pakuti iye amapangitsa dzuwa lake kuti litulukire pa oyipa ndi. . . abwino, ndipo amatumiza mvula pa olungama ndi. . .osalungama. (Mvula imabwera pa oyipa mofanana monga pa abwino.)*

<sup>31</sup> Tsopano kuti tizitsatire izi, ku uneneri wina wogwirizana ndi uwu, mulole ife titembenuzire tsopano ku Ahebri mutu wa 6, kwa ndime yina yotsatira pa iyi, pamene Paulo akubweretsanso ku malingaliro chinthu chomwecho chimene Yesu ananena. Paulo, akuyankhula tsopano. Pamene inu muli kusaka izo. . . Ndi inu kunjā mu kuwulutsa, tengani Mabaibulo anu pafupi ndi inu ndi chidutswa cha pepala, ndipo yang'anani pa izi tsopano. Ahebri mutu wa 6, Paulo akulembera kwa Ahebri, kuwasonyeza iwo mithunzi ndi zoyimira, kuwabweretsa iwo kuchokera pansu pa Chiyuda kupita mu Chikhristu, kuwasonyeza iwo momwe zinthu zakale zonse zinkangochitira mthunzi zinthu zimene zinali kuti zibwere. Paulo akuyankhula tsopano, Ahebri 6.

*Chotero posiya chiyambi cha chiphunzitso cha Khristu (K-h-r-i-s-t-u, mmodzi), tiyeni ife tipitirire patsogolo mpaka ku ungwiro; osati kuyika kachiwiri maziko a kulapa. . . ntchito zakufa, ndi za chikhulupiriro cha kwa Mulungu.*

*Za. . . chiphunzitso cha maubatizo, ndi za kusanjika manja, ndi za kuwuka kwa akufa, ndi za chiweruzo chamuyaya.*

*Ndipo izi ife tidzazichita, ngati Mulungu alola.*

*Pakuti kuli kosatheka kwa iwo amene anali nthawi yina atawunikiridwa, ndipo analawa za mphatso ya kumwamba, ndipo anapangidwa kukhala ogawana nawo za Mzimu Woyera,*

Ine ndikufuna kuyitana tcheru chanu miniti yokha. Kodi inu munazindikira, iyo ndi “mphatso”; ndipo osati “zimphatso,” ogawana nawo a “zimphatso zakumwamba”? Koma, “mphatso yakumwamba,” imodzi; “Khristu,” mmodzi; “mphatso,” imodzi.

*. . . mphatso yakumwamba, ndipo. . . anapangidwa kukhala ogawana nawo a Mzimu Woyera,*

*Ndipo analawa za. . . mawu a Mulungu, . . . (analawa za chiyani?). . . mawu a Mulungu, ndi mphamvu ya dziko liri kudza,*

*Ngati iwo ati adzagwere kunjā, kuti akadzikonze okha kachiwiri mwa kulapa; powona kuti iwo akudzipachikira kwa iwo okha Mwana wa Mulungu katsopano, ndi kumuyika iye ku manyazi apoyera.*

*Pakuti, (mvetserani) nthaka. . . imamwa mu mvula imene imabwera mowirikiza pa iyo, kuti ibalepo therere lokwanira iwo amene alirimira, imalandira madalitso kuchokera kwa Mulungu:*

*Koma izo zimene zimabala minga. . . mitungwi ndi zokanidwa, ndipo ziri zoyandikira ku kutemberera; zimene mapeto ake ali oti zikawotchedwe.*



<sup>32</sup> Tsopano fanizirani izo ndi Mateyu 5:24 kachiwiri. Zindikirani, Yesu anati mvula ndi dzuwa zimabwera pa dziko lapansi, zimene Mulungu amazitumiza izo kuti zikonzere chakudya ndi zinthu kwa anthu a dziko lapansi. Ndipo mvula imatumizidwa chifukwa cha chakudya, therere. Koma namsongole, maudzu, pokhala mmunda, zimalandira chinthu chomwecho. Mvula yomweyo imene imapangitsa tirigu kukula ndi mvula yomweyo imene imapanga maudzu kukula.

<sup>33</sup> Ndinali nalo phunziro lotero pa zimenezo nthawi yina, pamene ine ndinakomana nawo koyamba anthu Achipentekoste! Ndipo ilo linali phunziro lalikulu kwa ine. Ine ndinawawona amuna awiri, mmodzi . . . Ndisanayambe ndamvapo kuyankhula mmalirime kale. Mmodzi anayankhula mu malirime, winayo anatanthauzira iwo, mosinthanitsana. Ndipo amakhoza kunena zoono, ananena kuti, “Alipo ambiri muno amene ayenera kulapa usikuuno. Alipo akazi ndi amuna, limodzi.” Ndipo anthu ankawuka apo ndi kupita ku guwa.

Ine ndinaganiza, “Nzaulemerero bwanji!”

<sup>34</sup> Ndiyeno ndi mphatso yaying’ono ya Mzimu Woyera, ine ndinayankhula kwa amuna amenewo, basi, inu mukudziwa momwe, mu kuzindikira za mumtima, njira yaing’ono chabe yopezera izo. Ndipo mmodzi wa iwo anali Mkristu weniweni, ndipo iye anali wantchito weniweni wa Khristu, ndipo mmodzi winayo anali wachinyengo. Ndipo mmodzi wa iwo, mmodzi yemwe anali wachinyengo, anali akukhala ndi mkazi wa mutu wakuda, akuthamangathamanga ndi wa labulauni ndipo anali nawo ana ndi iye. Chabwino, izo zinali apo pomwe mu masomphenya; sizikanakhoza kukanidwa. Ndipo ine ndinayankhula kwa iye za izo. Iye anayang’ana pa ine ndipo anayenda mozungulira nyumbayo.

<sup>35</sup> Tsopano ine ndinasokonezeka, mokwanira ndithu. Ine ndinaganiza ine ndinali nditabwera kwa angelo, ndiye ine ndinadabwa ngati ine sindinali pakati pa adierekezi. Izi zikanakhoza kukhala motani? Ine sindikanakhoza kuzimvetsa izo. Ndipo kwa zaka ine ndinasunga manja anga kutali ndi izo, mpaka tsiku limodzi pamene . . .

George Smith, mnyamata yemwe akuyenda ndi mwana wanga wamkazi, ife tinapita dzulo, uko ku malo a chigayo chakale kumene ine ndimapita kukapemphera.

Ndipo nditatha kukhala mkati mmenemo masiku angapo, Mzimu Woyera unabweretsa Lemba ili mmbuyo kwa ine. “Pakuti mvula imabwera mowirikiza pa dziko lapansi kuti ikaliveke ilo ndi therere, koma minga ndi nthula zimakhala moyo mwa mvula yomweyo, ndi zimene mathero ake ali oti zikawotchedwe.” Kukhala moyo mwa gwero lomwelo lopereka moyo la Mulungu. Ndiye ine ndinamvetsa izo. “Mwa . . .” Yesu anati, “Ndi zipatso zawo iwo amadziwika.”

<sup>36</sup> Tsopano, chotero, mvula kugwera pansi pa zomera zachirengedwe za padziko lapansi, ndi choyimira cha mvula Yauzimu imene imapereka Moyo Wamuyaya, ikugwera pansi pa Mpingo, pakuti ife timayitcha iyo mvula ya nyundo ndi mvula ya masika. Ndipo ndiyo mvula, ikutsanulira apo kuchokera mu Mzimu wa Mulungu, pa Mpingo Wake.

<sup>37</sup> Zindikirani, ndi chinthu chachirendo kwambiri pano. Mwaona? Pamene mbewu izo zinapita mu nthaka, mulimonse izo zinafikira mmenemo, izo zinali minga kuyamba ndi kuyamba. Koma kumeneko tirigu amene anapita mu nthaka, ndi therere, linali therere kuyamba ndi kuyamba. Ndipo therere lililonse kumadzibala lokha, mobwerezza kachiwiri, zikusonyeza kuti ilo linali mu kuyamba kwapachiyambi.

<sup>38</sup> “Ndipo iwo akanadzanyenga Osankhidwa ngati izo zikanakhala zotheke,” chifukwa iwo akulandira mvula yomweyo, dalitso lomwelo, kusonyeza zizindikiro zomwezo, zodabwitsa zomwezo. Mukuona? “Iwo adzanyenga, kapena akanadzanyenga Osankhidwa ngati izi zikanakhala zotheke.” Tsopano, minga siyingakhoze kudzithandiza kukhala minga, ndipo ngakhalenso tirigu sangadzithandize kukhala tirigu; ndicho chimene Mlengi wa chimodzi chirichonse analinga pa chiyambi. Ndiwo Osankhidwa. Mvula yomweyo!

<sup>39</sup> Dzuwa limatuluka cha mmawa ndi kudzifalikitsira pa dziko lonse, monga ilo linali nalo dziko lapansi ili ndi tsiku limene ife tikukhalamo. Ndipo dzuwa, dzuwa lomwelo limene limatulukira kummawa ndi dzuwa lomwelo limene limakalowa kumadzulo. Ndipo dzuwa limenelo limatumizidwa kuti likakhwimitse njere pa dziko lapansi, zimene matupi athu amapangidwa kuchokerako.

<sup>40</sup> Ife tiri kukhala moyo ndi zinthu zakufa. Ndiyo njira yokha imene inu mungakhoze kukhala nayo moyo. Ndipo ngati chinachake chiyenera kuti chife tsiku lililonse kotero kuti inu mukhale moyo, mwachibadwa, ndiye kodi siziri izo zoono kuti ngati lako. . . Thupi lako liyenera kuti likhale moyo ndi zinthu zakufa, kwa moyo wachibadwa, ndiye iwe uyenera kukhala ndi Chinachake chitafa, mwauzimu, kuti chipulumutse moyo wako wauzimu. Ndipo Mulungu, anakhala chogwirika, mnofu, ndipo anafa kuti ife tikakhoze kukhala moyo. Palibe mpingo, palibe chinthu china mu dziko chingakhoze kukupulumutsani inu koma Mulungu. Ndi cho chinthu chokha chimene iwo amakhala moyo nacho.

<sup>41</sup> Tsopano yendetsani Malemba. Yesu ali Mawu. “Mu chiyambi panali Mawu. Ndipo Mawu anapangidwa thupi ndipo anakhala pakati pathu. Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali ndi Mulungu. Ndipo Mawu anapangidwa thupi, ndipo ndi Amene anakhala moyo, anakhala pakati pathu.” “Ndipo munthu sadzakhala moyo ndi mkate wokha,” kwa zathupi, “koma ndi

Mawu onse amene atuluka kuchokera mkamwa ya Mulungu.” Ndiye, inu mukuona, ife timakhala moyo ndi Mawu, ndipo ameneyo ndi Mulungu.

<sup>42</sup> Tsopano dzuwa limabwera modutsapo ndi kukhwimitsa njerezo. Tsopano, ilo silingakhoze kuzikhwimitsa izo zonse mwakamodzi. Pamene izo zikupitirirabe, kumakhwima, izo mowirikiza zimacha mpaka izo zimabwera ku khutu lathunthu.

Chotero izo ziri, lero, ndi Mpingo. Izo zinayamba mu ubwana wake, kumbuyo mu m’badwo wa mdima, pamene iwo unali pansu pa nthaka. Iwo wakula tsopano kufika mu kukhwima. Ndipo ife tikhoza kuziwona izo, mwangwirowo, momwe kuti Mulungu kupyolera mu chirengedwe nthawizonse. . .

<sup>43</sup> Inu simungakhoze kusokoneza chirengedwe. Ndilo lomwe liri vuto lero. Ife tikuwulutsa mabomba, ndi kunja uko mu nyanja imeneyo, kuziswa izo ndi kuziphulitsa izo mozungulira ndi mabomba a atomiki. Inu mukungoswa zochulukira zadothi limenelo nthawi zonse, kugwetsera mkati mwa ilo. Inu mukamadulira pansu mitengo; mikuntho idzakutengani inu. Kupanga dziwe pa mtsinje; iwo udzasefukira.

Inu muyenera kupeza njira ya Mulungu yochitira zinthu ndi kumakhala mwa iyo. Ife tawapanga anthu chipembedzo mu mipingo ndi mabungwe; tapenyani zimene ife tiri nazo! Khalani mu njira yoperekedwa ndi Mulungu ya izo.

<sup>44</sup> Koma, inu mukuona, “Iye amatumiza mvula,” kubwerera ku phunziro lathu, “pa olungama ndi osalungama.” Yesu akukuuzani inu apa tsopano, mu Mateyu 24, icho chidzakhala chizindikiro pa nthawi yotsiriza.

Tsopano, ngati chizindikiro ichi chiri kokha choti chikadziwike pa nthawi yotsiriza, ndiye izo zidzayenera kuti zikhale kutachitika kutsegula kwa Zisindikizo zimenezo. Mwaona? Ndi chizindikiro cha mapeto. Icho chikanadzakhala, pamene zinthu izi zikuchitika, icho chidzakhala pa nthawi yotsiriza. Ndipo icho chidzakhala chizindikiro, tsopano, kotero kuti Osankhidwa asadzakhale ali osokonezedwa mu zinthu zimenezi. Inu mukuziona izo? Ndiye, izo ziyenera kuwululidwa, kuyalutsidwa.

<sup>45</sup> Zindikirani, zonse tirigu ndi maudzu zimakhala moyo mwa Kudzoza komweko kuchokera Kumwamba. Zonse za izo zimasangalala pa Iko.

Ine ndikukumbukira izi, polozero mmbuyo ku chochitika ichi kumtunda uko tsiku lija ku Ntchini wa a Green. Ine—ine ndinawona masomphenya aja akubwera uko. Ndipo apo panali dziko lalikulu, ndipo ilo linali lonse litalimidwa. Ndipo apo panapita Wofesa, choyamba. Ine ndikufuna kuziyika izo pamaso panu. Penyani amene akupita apo choyamba, ndiye ndi chiyani chikutsatira izo. Ndipo pamene Munthu uyu atavala choyera anabwera apo kuzungulira dziko lapansi, akufesa mbewu,

ndiye kumbuyo kwa Iye kunabwera mwamuna, wovala zovala zakuda, ankawoneka akuzembera kwambiri, akunyang'amira motsatira kumbuyo kwa Iye, akufesa maudzu. Ndipo pamene izi zinachitika, ndiye ine ndinawona mbewu zonse zitatulukira. Ndipo pamene izo zinatulukira, zimodzi zinali tirigu ndipo zimzakezo zinali maudzu.

Ndipo apo panabwera chilala, mwakuti pamenepo, zinkawoneka monga, zonse za izo zinali ndi mitu yawo pansi ziri kumangolirira mvula. Ndiye apo panadza mtambo wawukulu pamwamba pa dziko lapansi, ndi iyo inavumba. Ndipo tirigu anawuka ndipo anati, "Ambuye alemekezeke! Ambuye alemekezeke!" Ndipo maudzu anawuka ndipo anafuula, "Ambuye alemekezeke! Ambuye alemekezeke!" Zotsatira zofanana. Zonse za izo zikupsyerera, zonse za izo zikupita. Ndiyeno tirigu akuwuka ndipo akumva ludzu. Ndipo chifukwa izo zinali mmunda womwewo, dimba lomwelo, malo omwewo, pansi pa kutsanulira kofanana, apo panatulukira tirigu ndipo apo panatulukira namsongole mwa chinthu chofanana chomwecho. Zindikirani, madzi omwewo odzozera akumeretsa tirigu, akumeretsa udzu.

<sup>46</sup> Mzimu Woyera womwewo umene umadzoza Mpingo, umene umawapatsa iwo chikhumbo kuti azipulumutsa miyoyo, umene umawapatsa iwo mphamvu kuti azichita zozizwitsa, Iwo umagwera pa osalungama mofanana monga olungama. Mzimu womwe womwewo! Tsopano, inu simungakhoze kuwupanga iwo mwa njira yina iliyonse ndi kumvetisa Mateyu 24:24. Iye anati, "Apo padzawuka aKhristu abodza," iwo odzozedwa, mwabodzawo. Odzozedwa ndi Chinthu chenicheni, koma nkukhala aneneri abodza a Ichu, aphunzitsi abodza a Ichu.

Nchiyani chimene chikanati chimupange munthu kufuna kuti akhale mphunzitsi wabodza wa chinachake chimene chiri Choonadi? Tsopano ife tifika mmusi ku chilemba cha chirombo mu maminiti pang'ono, ndipo inu mudzawona chipembedzo chake. Mwaona? Aphunzitsi abodza; abodza, odzozedwa. A Khristu odzozedwa, koma aphunzitsi abodza. Ndiyo njira yokha imene inu mungakhoze kuwonera izo.

<sup>47</sup> Monga ngati kuno nthawi yina kale, ine ndabwerezapo izi. Ine ndikhoza kubwereza izo chifukwa ife talumikizidwa kudutsa fukoli. Tsiku lina ine ndinali kuyankhula kwa mzanga wa ine, kumene izo zikufikirako mmawa uno, mu Arizona. Ndipo iye anali ndi—munda wa citrus. Ndipo iye anali nawo mtengo kumeneko umene unali mtengo wa lalanje umene unali kubala zipatso za manyumwa, ndi ndimu, nanchesi, tanjelo. Ndipo ine ndayiwala kuti ndi zipatso zosiyana zingati zimene zinali pa mtengo umodzi umenewo. Ndipo ine ndinati kwa b—b—bamboyo, ine ndinati, "Zikutheka motani izo? Ndi mtengo wa mtundu wanji umenewo?"

Iye anati, “Mtengowo, pawokha, ndi mtengo wa lalanje.”

Ine ndinati, “Bwanji iwo uli ndi zipatso za manyumwa pa iwo? Nchifukwa chiyani iwo uli ndi mandimu pa iwo?”

Iye anati, “Izo ndi zomezanitsidwa mwa iwo.”

Ine ndinati, “Ine ndikuona. Chabwino, tsopano,” Ine ndinati, “tsopano, chaka chamawa pamene mtengo umenewo uti udzabwere ndi mbewu yina ya chipatso,” chimene izo zonse zimacha pafupi nthawi yofanana, ine ndinati, “ndiye iwo udzabala wonse palimodzi malalanje. Ngati uli mtengo wa lalanje lanchombo, iwo udzabala malalanje anchombo, sichoncho izo, bwana?”

Iye anati, “Ayi, bwana. Nthambi iliyonse yomezanitsidwa idzabala za mtundu wake.”

Ine ndinati, “Inu mukutanthauza kuti nthambi ya ndimu idzabala ndimu kuchokera mu mtengo wa lalanje uwo?”

Iye anati, “Inde, bwana.”

“Kodi chipatso cha manyumwa chidzabala chipatso cha manyumwa kuchokera mu mtengo wa lalanje uwo?”

Iye anati, “Inde, bwana. Ndicho chikhalidwe cha nthambi imene yamezetsanidwa mwa iwo.”

Ine ndinati, “Malemekezo akhale kwa Mulungu!”

Iye anati, “Inu mukutanthauza chiyani?”

Ine ndinati, “Funso limodzi linanso. Tsopano, kodi mtengo wa lalanje umenewo udzabalaponso malalanje kachiwiri?”

Iye anati, “Pamene iwo uti udzatulutse nthambi yina.” Pamene iwo uti udzatulutse nthambi yina, osati pamene ina yamezanitsidwa mwa iwo. Koma, iyo yonse ndi zipatso za citrus, ndipo iyo imakhala moyo wa citrus umene uli mu mtengo wa citrus.

<sup>48</sup> Ine ndinati, “Ndi pamenepo inu! Amethodisti adzabala Chimethodisti, nthawi iliyonse. Abaptisti adzabala Chibaptisti, nthawi iliyonse. Akatolika adzabala Chikatolika, nthawi iliyonse. Koma Mpungu wa Mulungu wamoyo udzabala Khristu kuchokera ku muzu, Mawu nthawi iliyonse, ngati iwo uti udzatulutse konse nthambi yina ya iyo Mwini.”

<sup>49</sup> Tsopano, inu mukhoza kumezanitsa iyo mkati mmenemo, inu mukuona. Chipatso cha manyumwa chirichonse, ndimu, tanjelo, nanchesi, zirizonse zimene zipatso za citrus ziri, chirichonse cha izo chikhoza kukhala moyo mu mtengo umenewo; koma chikubala mboni zabodza za mtengo, zikukhala moyo mwa mtengowo. Inu mukuwona izo? Iyo ikukhala moyo ndi kumapitirira pa moyo weniweni umene uli mu mtengo umenewo.

Tsopano, apo pali Mateyu 24:24, kukhala moyo ndi Moyo womwewo, koma iwo sanalipo kumene, pa chiyambi. Iwo

akubala umboni wabodza wa Mtengo umenewo! Ndi mtengo wa lalanje, komabe ndi mtengo wa citrus. Ndipo iwo amati, “Mpingo uwu, chipembedzo ichi chikubala umboni wa Khristu,” ndipo ali ndi ubatizo wabodza, umboni wabodza wa Mawu, kuyesa kumanena kuti mphamvu ya Mulungu inali kokha ya atumwi.

Yesu, Iyemwini, anati, “Pitani inu ku dziko lonse ndi kukalalikira Uthenga kwa nthambi iliyonse imene konse... mtengo umene uti udzabale konse, nthambi iliyonse imene iti idzakhale mu mtengowo. Ndipo zizindikiro izi zidzatsira nthambi zenizeni.” Kuti? Malingana ngati iwo uli Mtengo, malingana ngati Iwo ukutulutsa nthambi, mpaka ku mapeto a dziko. “Mu Dzina Langa iwo adzatulutsa ziwanda; kuyankhula ndi malirime atsopano; kunyamula njoka; kumwa zinthu zakupha; kuyika manja pa odwala ndipo iwo adzachiritsidwa.” Mukuona ora limene ife tiri kukhalamo? Mukuona zimene Yesu ananena?

<sup>50</sup> Kumbukirani, izi zinali pa nthawi yotsiriza, osati mmbuyo pansu pa Wesile ndi kumbuyo uko. Tsopano, pa nthawi yotsiriza, izi zinali zoti zikachitike.

Tsopano penyani Malemba; aloleni Iwo achitire umboni. Yesu anati, “Fufuzani Malemba, pakuti mwa Iwo inu mukuganiza, kapena mukukhulupirira, kuti inu muli nawo Moyo Wamuyaya, ndipo Iwo ali Amene amachitira umboni za Ine.” Mwa kuyankhula kwina, ngati mtengo uwu uti udzatulutse konse nthambi... “Ine ndine Mpesa, Mtengo; inu ndinu nthambi. Iye amene akhulupirira mwa Ine, ntchito zimene Ine ndizichita iye adzazichita nayenso,” Yohane Woyera 14:12.

<sup>51</sup> Tsopano, “Iye amene akhala mwa Ine, iye amene... iye amene anali mu muzu Wanga pa chiyambi.”

Ndicho chifukwa Yesu anali zonse Muzu ndi Mphukira ya Davide. Iye analipo asanakhalepo Davide, mwa Davide, ndi pambuyo pa Davide, zonse Muzu ndi Mphukira ya Davide; Nyenyezi Yammawa, Duwa la Sharon, Kakombo wa Mdambo, Alpha ndi Omega; Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera. “Mwa Iye mukukhala chidzalo cha Umulungu mwathupi.” Zonse Muzu ndi Mphukira ya Davide!

“Iye amene ali Moyo wosankhidwa, Moyo wokonzedweratu, umene uli mwa Ine,” Ndipo Iye ali Mawu, “kuchokera pachiyambi; pamene iye ati azibwera, iye adzabala zipatso Zanga.” Yohane Woyera 14:12.

Koma enawo adzakhala moyo ndi chinthu chomwecho, kumadzitcha okha Akhristu ndi okhulupirira. “Osati onse amene anena, ‘Ambuye, Ambuye,’ ati adzalowe mkati.”

Tsopano, ndipo izi ndi zoti zichitike ndi kuwonetseredwa mu masiku otsiriza, “pamene zinsinsi za Mulungu ziyenera kutsirizidwa,” monga ife titi tifikire kwa izo patso golo pang’ono.

<sup>52</sup> Mitengo iyi, mpesa woona ndi mpesa wabodza! Inu mwandimvapo ine ndikulalikira pa izo chiyambireni, kuchokera mu zaka zapitazo, momwe iyo yakulira limodzi. Kuyibweretsa iyo mwa yense payekha ndi kuwonetsa zimenezo, kuchokera kwa Kaini ndi Abele, mipesa iwiri imene inakomana pa guwa; onse a iwo achipembedzo, onse a iwo odzozedwa, onse a iwo akukhumba moyo, ndi kumapembedza Mulungu yemweyo. Ndipo mmodzi anakanidwa ndipo winayo analandiridwa.

Ndipo njira yokha imene mmodzi amene analandiridwayo akanachitira chirichonse chosiyana kwa m'bale wake, icho chinaluridwa kwa iye. Pakuti Baibulo linati, “Mwa chikhulupiriro...” Ahebri, mutu wa 11, “Mwa chikhulupiriro Abele anapereka kwa Mulungu nsembe yopambana kwambiri kuposa ija ya Kaini, imene Mulungu anachitira umboni kuti iye anali wolungama.”

Yesu, anati, vumbulutso lauzimu la Yemwe Iye anali! “Kodi anthu amati Ine Mwana wa munthu ndine yani?”

Iye anati, Petro anati, “Inu ndinu Khristu, Mwana wa Mulungu wamoyo.”

“Wodala uli iwe, Simoni—Simoni, mwana wa a Yonasi; thupi ndi magazi sizinaululire izi konse kwa iwe. Atate Anga amene ali Kumwamba awulula izo. Pa thanthwe ili Ine ndidzamangapo Mpingo Wanga,” (chiyani?) vumbulutso lowona la Mawu. Apo pali Mpesa woona kachiwiri. “Abele, mwa chikhulupiriro!”

Inu mukuti, “Ilo silinali vumbulutso.”

<sup>53</sup> Chikhulupiriro ndi chiyani? Chikhulupiriro ndi chinachake chimene chaululidwa kwa iwe; chimene sichinakhalepo, koma iwe ukukhulupirira kuti icho chidzakhalepo. Chikhulupiriro ndi vumbulutso la chifuniro cha Mulungu. Kotero, mwa vumbulutso!

<sup>54</sup> Ndipo mipingo lero sili kukhulupirira ngakhale mu vumbulutso lauzimu. Iwo amakhulupirira mu kuphunzitsa kwa mbalume za kachitidwe kena. “Mwa vumbulutso Abele anapereka kwa Mulungu nsembe yopambana kwambiri kuposa ija ya Kaini, imene Mulungu anachitira umboni kuti iye anali wolungama.” Amen. Ine ndikuyembekeza kuti inu mukuona zimenezo. Mukuona pamene ife tikukhala? Mukuliona oralo?

Ine ndinali kuyankhula kwa n—njonda osati kale lapitalo, sikolala wa Chikhristu ndi njonda. Iye anati, “Bambo Branham, ife timakana mavumbulutso onse.”

<sup>55</sup> Ine ndinati, “Ndiye inu muyenera kumukana Yesu Khristu, pakuti Iye ali vumbulutso la Mulungu, Mulungu anawululidwa mu thupi laumunthu.” Mukapanda inu kuziwona izo, inu mwatayika.

Yesu anati, “Mukapanda inu kukhulupirira kuti Ine ndine Iye, inu mudzafa mu machimo anu.” Iye ali

vumbulutso la Mulungu, Mzimu wa Mulungu utawululidwa mwa mawonekedwe aumunthu. Ngati inu simungakhoze kukhulupirira izo, inu mwatayika. Inu mukamuyika Iye pa munthu wachitatu, munthu wachiwiri, kapena munthu wina aliyense pambali pa Mulungu, inu mwatayika. “Mukapanda inu kukhulupirira kuti Ine ndine Iye, inu mudzafa mu machimo anu.” Vumbulutso!

<sup>56</sup> Ndi zosadabwitsa kuti iwo sakanakhoza kumuwona Iye. “Palibe munthu angakhoze kubwera kwa Ine kupatula Atate Anga akamukoka iye. Ndipo onse amene Atate andipatsa Ine,” mu mizu, “adzadza kwa Ine.” Mukuona? Inu mukumvetsa zimenezo? O, momwe ife tiyenera kumukonda Iye, kumunyadira Iye, kumutamanda Iye; kuwona chipatso cha Mzimu mu masiku otsiriza, ndipo Mtengo wa Mkwatibwi ukucha pamwamba pa nthawi!

<sup>57</sup> Mpesa woona ndi mpesa wabodza, yonse inali nako kudzoza kofanana. Madzi anagwera pa yonse ya iyo. Nzosadabwitsa kuti Iye anatichenjeza ife, “Izo zikanadzanyenga Osankhidwa omwe ngati izo zikanakhala zotheka.”

<sup>58</sup> Zindikirani, iyo imawoneka yofanana. Iyo imadzozedwa mofanana. Koma zindikirani, “Ndi zipatso zawo...” Inu mumayidziwa motani iyo?

Inu mumadziwa bwanji kuti sindiro lalanje? Chifukwa ilo likubala chipatso cha manyumwa. Nthambi imeneyo ndi yabwino, iyo ikukhala mu mtengowo, koma iyo ikubala chipatso cha manyumwa. Iyo siili monga yoyambayo.

Ndipo ngati mpingo unena kuti iwo “amamukhulupirira Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi nthawizonse,” ndi kumakana Mphamvu Yake, kukana ntchito Zake, kukana Mawu Ake; ngati—ngati. . . Mpingo umene umakhulupirira mwa Yesu Khristu, uti udzachite ntchito za Yesu Khristu, iwo udzakhala nawo moyo wa Yesu Khristu. Ndipo ngati iwo siuli, ziribe kanthu ngati Moyo ukutsanulira mwa iwo; ngati iwo siuli wokonzedweratu, kuchokera ku mizu, iwo udzabala chipatso cha manyumwa nthawi iliyonse, kapena chinachake chosiyana. Koma ngati uli Moyo wokonzedweratu, mu mizu, iwo udzabala Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi nthawizonse, ngati ali Mawu amene akubwera kupyolera mu Muzu. Chimene, Iye ali Muzu, chiyambi cha nthawi.

<sup>59</sup> Zindikirani, koma ndi chimene iwo amabala chimene chimakuuza iwe kusiyana. “Ndi chipatso chawo,” Yesu anati, “Inu mudzawadziwa iwo.” “Munthu samasonkhanitsa manyumwa kuchokera pa nthula,” ngakhale nthula zitakhala ziri mmunda wa mpesa womwe. Izo zikanakhoza kukhala zotheka, koma chipatso chidzafotokoza izo.

Chipatso ndi chiyani? Mawu, a chipatso cha nyengoyo, Ndicho chimene icho chiri, kuphunzitsa kwawo. Kuphunzitsa



kwa chiyani? Kuphunzitsa kwa nyengoyo, nthawi imene iyo ili. Chiphunzitso cha munthu, chiphunzitso cha chipembedzo, koma, kapena Mawu a Mulungu a nyengoyo?

Tsopano, nthawi ikupita patali mwamsanga kwambiri, kuti ife tikanapirira pa izo nthawi yayitali. Koma ine ndikutsimikiza kuti inu amene muli pano, ndipo ine ndikutsimikiza kuti inu mu fuko lonseli, mukhoza kuwona zimene ine ndikuyesa kukuuzani inu, pakuti ife tiribe kutalikira kochuluka kwambiri kuti tikhale pa izo.

<sup>60</sup> Koma inu mukhoza kuwona kuti Kudzoza kumafika pa osalungama, aphunzitsi abodza, ndi kumawapangitsa iwo kuti achite chimodzimodzi zimene Mulungu anawauza iwo kuti asamachite; koma iwo amadzachita izo, mulimonse. Chifukwa chiyani? Iwo sangakhoze kudziletsa izo. Nthula zingakhoze bwanji kukhala chinthu china chirichonse koma nthula? Ziribe kanthu kaya ndi mvula yochuluka bwanji imene yakonkhedwera pa izo, izo ziyenera kukhala nthula. Ndicho chifukwa Yesu anati, “Izo zidzakhala zoyandikana kwambiri izo zikanadzanyenga Osankhidwa omwe,” amene ali mu mizu, “ngati izo zikanakhala zotheka,” koma izo nzosatheka. Tirigu sangakhoze kuchita kanthu koma kubala tirigu; ndizo zonse zimene iye angakhoze kubala.

<sup>61</sup> Zindikirani. Kumbukirani, Mulungu sali woyambitsa wa bungwe. Mdierekezi ndiye woyambitsa wa bungwe. Ine ndatsimikizira izo mwa Mawu, mmbuyo ndi mtsogolo, ndi mobwereza bwereza; sitisowa kuti tipite mu izo mmawa uno. Ife tikudziwa kuti Mulungu sanawapangepo anthu bungwe limodzi monga chomwecho, kupanga bungwe. Mazana a zaka itachitika imfa ya wophunzira wotsiriza, iwo nkuti asanayambe akhalapo nalo bungwe loyamba. Izo nthawizonse zatsimikizira zolephera. Ngati izo siziri, nchifukwa chiyani ife sitiri palimodzi mu chikondi lero, Amethodisti, Abaptisti, Apresbateria, Akatolika ndi onse? Nchifukwa chiyani ntchito za Mulungu sizikutitsatira ife, ndiye, mpingo uliwonse uli pa chinthu chomwecho, Mawu? Zinthu izo zimene zimawalekanitsa anthu, ubale. . . Ife tiri otalikira kwa Mulungu kuposa momwe ife tinayamba takhalirapo, mipingo, imene tikuyikamba.

<sup>62</sup> Tsopano, ife tawuzidwa, kuti, “Zinthu zonse zakale zinkachitika mwa zitsanzo, kwa kutiphunzitsa kwathu, zidzudzulo, kulimbikitsa.” Kuti, zinthu zonse zakale za Chipangano Chakale zinkachitika, mochitiratu mthunzi, kuti tiwone zimene zikanati zidzakhale mu Chipangano Chatsopano, mu tsiku lathu.

Basi monga ngati inu simunayambe mwawonapo dzanja lanu, ndipo inu nkuyang’ana apo ndipo inu nkuwona mthunzi pa khoma, monga dzanja langa lingakhalire kuchokera mu kuwala, ngati ilo liri ndi zala zisanu pano mu mthunzi, pamene

chiri chithunzi; ndipo inu mukasuntha manja anu moyandikiza, pokhala lenileni, cha ku—cha ku chithunzi, icho chiyenera kubwera ku zala zisanu.

Monga Baibulo limatiuza ife, kuti, “Chipangano Chakale pokhala mthunzi, choyimira cha zinthu zatsopano, kapena zinthu zimene zinali zoti zibwere; osati zinthu zimene zomwe ziripo, koma iwo ndi mthunzi, choyimira cha zinthu zimene ziri kudza.”

<sup>63</sup> Tiyeni ife tibwerere mmbuyo ndi kuwona ngati chinthu ichi chinayamba chakhalapo mu m’badwo wina uliwonse. Kodi inu mukulolera? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Kotero ife tidziwa, kuti titsimikizire izi, mmbuyo ndi mtsogolo, mwa Mawu; osati mwa malingaliro a munthu wina, mbalume zina.

Ine sindikusamala yemwe iye ali; munthu wina aliyense, inemwini kapena wina aliyense, “Ngati iye sayankhula molingana ndi lamulo ndi aneneri, mulibe Kuwala mwa iye.” Mukuona? Ndizo zimene Baibulo linanena. “Mulole mawu a munthu aliyense akhale bodza, ndipo Anga akhale owona,” mosasamala yemwe iye ali.

<sup>64</sup> Tsopano tiyeni tibwerere mmbuyo ndi kukapeza ngati izi zinayamba zachitikapo, kuti zitisonyeze ife chitsanzo.

Ife tikhoza kubwereranso kachiwiri tsopano mu Bukhu la Eksodo ndi kuyankhula za khalidwe lotchedwa Mose, yemwe anali mneneri wodzozedwa wotumidwa ndi Mulungu, ndi Mawu a Mulungu ndi chifuniro cha Mulungu kwa m’badwo wake. Monga Mawu a Mulungu nthawizonse amayenda mwa kupitiriza, Iye anati, “Iye sanali kuchita kanthu mpaka Iye ataululira Izo kwa aneneri Ake poyamba.” Ndiye Iye amachita izo. Mwaona?

Tsopano, Iye sangakhoze kunama. Iye sangakhoze kunama ndi kukhala Mulungu. Ayi, bwana. Iye ayenera kukhalabe woona. Mulibe bodza mwa Iye. Iye ali. . .

Ndipo Iye sangakhoze kusintha Izo. Ngati Iye atero, ndiye Iye sali Mulungu; Iye analakwitsa. Iye ayenera kukhala wopandamalire. Ndipo wopandamalire sangakhoze kupanga kulakwitsa. Mukuona? Kotero chirichonse chimene Mulungu ayankhula konse, ndicho cholondola Mwamuyaya. Mwaona? Ndipo Iye analonjeza zimenezo. Kotero, penyani, palibe paliponse mu Baibulo kupatula izo zitatsatira kupitiriza molondola mpaka kwa izo.

<sup>65</sup> Tsopano, Mulungu anamulonjeza Abrahamu kuti mbewu yake ikanadzakhala mlendo mu—mu dziko lachirendo kwa zaka mazana anai, ndiye Iye akadzayitulutsa iyo kunja ndi dzanja lalikulu la nyonga ndi mphamvu, kuwonetsa zizindikiro Zake ndi zodabwitsa pakati pa anthu amene iwo ankakhala nawo. Nthawi ya lonjezo inayandikira pafupi. Anthu anali atayiwala za izo. Iwo anali ndi Afarisi ndi Asaduki, ndi ena otero,

zipembedzo. Koma, zonse mwadzidzidzi, apo kunadza Mulungu mwini ndipo anatenga kuchokerako, kupita, kutali ndi aliyense wa iwo.

Mulungu palibe, mu tsiku lirilonse kapena pa nthawi iliyonse, anayamba wamuyitanapo mneneri kuchokera ku chipembedzo. Ayi, bwana. Iwo wasokonezeka kwambiri, iye sangakhoze kuchita izo; iye akanayenera kukhala ndi chipembedzo chimenecho.

<sup>66</sup> Mose, munthu wotumidwa kuchokera kwa Mulungu, ali ndi Mawu a Mulungu, ndipo pa ulendo wake akuwatengera Israeli kukalowa mu dziko lolonjezedwa, mosamalitsa ali ndi lamulo la Mulungu, iye anakomana ndi mneneri wina, wodzozedwa mmodzi wina amene anali nako kudzoza kowona kwa Mzimu Woyera womwewo umene unali pa Mose. Ndiko kulondola. Iye anali mneneri. Mzimu Woyera unali pa munthu uyu. Dzina lake linali Balaamu. Ndife tonse omudziwa iye. Chabwino, zinthu zomwe, zofanana, zinthu—zinthu zimene munthuyo ananena, zikanali kuchitikabe, pafupi zaka mazana makumi awiri ndi asanu ndi atatu apitazo. “Iwe uli ngati chipembere, O Israeli. Aliyense amene adalitsa iwe adzadalitsidwa. Aliyense amene atemberera iwe adzatembereredwa. Nyonga zako, ndi mwamphamvu, ndi odala bwanji mahema ako, O Yakobo!” Onani, iye sakanakhoza kudzithandiza yekha. Iye anabwera kumeneko akulinga mu mtima mwake kuti awatemberere anthu.

<sup>67</sup> O, inu aphunzitsi abodza amene mukumvetsera kwa matepi awa zaka zonse izi, ndi kumawona Mulungu akutsimikizira chimodzimodzi zimene Iye ananena, ndipo inu mumakhala mowerenga mwanu ndi kumadziwa kuti ndicho Choonadi; ndipo chifukwa cha kusiyana kwanu kwa chipembedzo, inu mumawatsutsa iwo ndi kumawauza anthu anu kuti siziri chomwecho. Tsoka kwa inu! Nthawi yanu yayandikira pafupi.

<sup>68</sup> Balaamu, atadzozedwa ndi Mzimu womwewo umene unali pa Mose. Ndi chiyani chinali chosiyana? Kuphunzitsa kwa Mose kunali kwangwiro. Baibulo linanena apa mu Petro Wachiwiri, kuti kunali “kuphunzitsa kwa Balaamu” kumene Israeli anakulandira, kumene Mulungu sanakukhulukire konse. Tchimo losakhulukika! Palibe mmodzi wa iwo amene anapulumsidwa, ngakhale iwo anali atabwera pansi pa madalitso a Mulungu, ndipo anawona dzanja la Mulungu likusuntha ndi mneneri wamphamvu uyu, ndipo analiwona ilo likutsimikiziridwa chimodzimodzi ndi Mulungu. Ndipo, chifukwa, mneneri wina anabwera mkati ndi kuphunzitsa, kosiyana, ndipo anatsutsana naye Mose, ndi kuyesa kuti atsimikizire kwa anthu kuti Mose anali kulakwitsa. Ndipo Datani, Kora, ndi ambiri a iwo, anagwirizana naye iye ndipo anawaphunzitsa ana a Israeli kuti achite ziwere, kuti atsatre bungwe lake, kuti, “Ndife tonse ofanana.”

“Ziribe kanthu kuti ndife Amethodisti, Abaptisti, Apresbateria, kapena Apentekoste, ndipo chinanso nchiyani, ndife tonse ofanana.”

<sup>69</sup> Ife sitiri ofanana! Inu ndinu anthu opatulidwa, oyera kwa Ambuye, odzipereka ku Mawu ndi Mzimu wa Mulungu, kuti mubale chipatso cha lonjezo Lake la tsiku lino. Ndipo inu simuli a iwo! Ine ndikudziwa kuti ndizo zamphamvu mwaukali, koma ndicho Choonadi chimodzimidzi basi. Odzipereka ku utumiki mu masiku otsiriza awa! “Tulukani kuchokera pakati pa izo.”

<sup>70</sup> Tsopano, “kuphunzitsa kwa Balaamu,” osati uneneri wa Balaamu. Iwo unali wabwino. Ameneyo anali Mulungu. Ndi angati akukhulupirira zimenezo? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Uneneri wa Balaamu unali wolondola chimodzimidzi, chifukwa Iye sakanakhoza kuyankhula kanthu kena kalikonse. Kudzoza kwa Mulungu sikukanakhoza kuyankhula kanthu kena kalikonse, ndipo Mulungu anavomerezera izo pa kutsimikizira kuti izo zinali Choonadi. Koma kunali “kuphunzitsa kwa Balaamu.”

<sup>71</sup> Tsopano fanizitsani izo ndi Mateyu 24:24. Iwo odzozedwawo, koma kuphunzitsa kwawo ndi kwabodza. Utatu, ndi zinthu zonse monga choncho; zolakwika, otsutsakhristu!

Ine ndikuyembekeza kumverera kwanu sikufika popwetekedwa. Ndipo musati mutembenuze izo, mafoni amenewo kuwatseka. Ndipo musati muwukepo ndi kutuluka kunjja. Ingokhazikikani bata, ndipo tiyeni tiwone ngati Mzimu Woyera siwuwulula izo kwa ife, ndi kutsimikizira izo kwa ife. Inu mukuti, “Koma izo. . .” Basi chirichonse chimene inu mumakhulupirira, ingokhazikikani bata ndi kumvetsera. Ndipo mumufunse Mulungu kuti atsegule mtima wanu, ndiye inu mupeza ngati ndinu mtungwi, kapena nthula, kapena paliponse pamene inu mukuyima. Mukuona?

<sup>72</sup> Tsopano, ngakhale Yudasi, “okonzedweratu ku chiweruzo iye anali,” atakhala pamenepo pamaso pa Yesu. Ndipo Yesu anamuwuza iye, “Iwe ndiwe ameneyo. Chirichonse chimene iwe ukuti uchichite, ndi chirichonse chimene iwe ukuyenera kuti uchite, pita ukachichite icho mwamsanga.” Iye akudziwa chimene iye anali kuchita, koma, chifukwa cha zidutswa makumi atatu izo za siliva, ndi kutchuka, anamugulitsa Ambuye Yesu Khristu. Mmodzi wa ophunzira Ake, msungichuma wa mpingo, Yesu anamutcha iye “bwenzi” Lake. Mwaona? Baibulo linati, “Iye anabadwa ali mwana wa chitayiko,” basi mofanana monga Yesu anabadwa Mwana wa Mulungu. “Kunyenga Osankhidwa omwe ngati izo zikanakhala zotheka.”

<sup>73</sup> Zindikirani mwatcheru pamene ife tikuwerenga mopitirira. Ife titenga chochitika china, uko mu Bukhu la Mafumu. Uko kunali m—mneneri, ndipo dzina lake linali Mikaya. Iye

anali mwana wamwamuna wa Imlah, ndipo iye anali mneneri. Iye anali.

Ndipo uko kunali mneneri wina, mkulu wa bungwe la aneneri, iwo odzozedwawo. Baibulo linati iwo anali “aneneri,” mofanana basi monga Iye anati Balaamu anali mneneri, iwo odzozedwawo.

Ndipo uko kunali mmodzi wa iwo dzina lake Mikaya, yemwe anali wodzozedwa ndi Mulungu ndipo atatamidwa ndi Mulungu, ndi Mawu a Mulungu.

Uko kunali mmodzi, Zedekia, yemwe ankaganiza kuti iye anali wotumidwa ndi Mulungu. Iye anali wodzozedwa ndi Mulungu, koma kuphunzitsa kwake kunali kosiyanana ndi Mawu a Mulungu. “Adzauka, aKhristu abodza, kumawonetsa zizindikiro zazikulu, akanati adzawanyenge Osankhidwa ngati kukanatheka.”

<sup>74</sup> Zindikirani, onse a iwo, onse a iwo odzozedwa. Tsopano, iwe ukanakhoza kudziwa bwanji yemwe anali wolondola, ndi wolakwitsa? Penyani chimene Mawu anamulonjeza Ahabu. Mneneri yemwe analipo asanakhalepo iye, yemwe anali Eliya, mmodzi wa aneneri aakulu a m’badwowo, yemwe anali mneneri wotsimikiziridwa. Mneneri wotsimikiziridwa uyo ananena, kuti, “Chifukwa Ahabu anali atachita choyipa ichi, kuti agaru akanadzanyambita magazi ake; atatenga moyo wa Naboti. Ndi kuti agaru akanati adzamudye Yezebeli, ndipo. . . thupi lake likanadzakhala ndowe pa minda.” Tsopano, ungakhoze motani iwe kudalitsa chimene Mulungu wachitemberera? Kapena ungakhoze motani iwe kutemberera, monga Balaamu ananena, chimene Mulungu wachidalitsa? Mwaona?

Koma aneneri awa anali odzipereka. Panalibe kukayikira ayi koma chimene iwo anali anthu abwino, anthu olemekkezeka. Pakuti, kuti ukhale mneneri mu Israeli, iwe uyenera kukhala wolemekkezeka, kapena ngakhale Wachiisraeli. Iwe unali kugendewa, ngati sichoncho. Iwo anali amuna olemekkezeka. Iwo anali amuna anzeru. Iwo anali amuna ophunzira. Iwo anali osankhidwa ndi Ahabu, a fukolo. (Mukuona zimenezo, Mlongo Wright?) Osankhidwa a fukolo, okwanira bwino a zime- . . .

<sup>75</sup> Ndipo tsopano, pamene Mikaya anawona masomphenya ake, iye ankadziwa mu mtima wake chimene Mawu anali atanena, koma iye ankafuna kuti uwone chimene Mzimu umene unali mwa iye ukanati unene.

Kotero iwo anamuuzwa iye, iwo anati, “Iwe unene chinthu chomwecho chimene aneneri ena awa akunena. Ndipo pamene iwe utero, bwanji, iwe udzakhala, ife tikutengera iwe mu chiyanjano, mopanda kukayika, kachiwiri. Mukuona? Ife tikupanga iwe mmodzi wa ife. Ife tikutenga iwe kubwerera ku chipembedzo cha ife. Ndiwe. . . Ife tikudziwa kuti ndiwe mneneri, koma iwe nthawizonse ukumanena zinthu

zotemberera. Iwe nthawizonse ukumamutemberera Ahabu. Tsopano, Zedekia, munthu wamkulu, papa, kapena..." chirichonse chimene iye anali. "Tsopano iye wamudalitsa Ahabu, ndipo wati, 'Pitani mukachite izo.' Tsopano iwe unene chinthu chomwecho, Imlah. Bwanji, ndiwe munthu wosauka chabe. Iwe ulibe gulu, nkomwe, mpang'ono pomwe. Ndipo anyamata awa ali nawo mamilioni. Fuko lonse ndi la iwo. Tsopano iwe unene mofanana monga iwo akuchitira, ukuwona zimene iwe uti uchite, iwe udza—iwe udzadya zolemera za dziko." Iye akuyankhula kwa munthu wolakwika pamenepo!

<sup>76</sup> Bwanji ngati izo zikananenedwa kuti, "Kodi iwe ungakhoze kupeza cholakwitsa chirichonse mwa Zedekia, Mikaya?" "Ayi." "Kodi iwe unayamba wamugwirapo iye mu tchimo?" "Ayi." "Kodi iwe unayamba wamumvapo iye akumutukwana aliyense?" "Ayi." "Kodi iwe unayamba wamugwirapo iye ataledzera?" "Ayi." "Kodi iwe ungakhoze kutsutsa maphunziro ake?" "Ayi." "Kodi iwe ukukhulupirira kuti digirii yake ya udokotala ndi yabodza?" "Ayi." "Iwe ukukhulupirira Ph.D. yake—yake ndi yolondola?"

"Zedi. Mwa bungwe la Sanhedrin; ine ndikuganiza ndizo zonse bungwe, ine ndikuganiza izo ndi zabwino."

"Chabwino, ndiye, bwanji iwe sulikujowinana ndi iye?"

"Chifukwa iye wachoka pa Mawu!"

<sup>77</sup> Chabwino, ife tikhala nacho chiwonetsero cha izo, ndiye, monga Eliya mneneri zisanachitike izo. Ndipo ngati ndiwe mwana wa Mulungu, iwe udzakhala ndi mneneri wa Baibulo ili. Ndi Mawu. Zindikira ora, nyengo.

<sup>78</sup> Chabwino, bwanji ngati Zedekia akanati, "O, ine ndikumudziwa mneneri yemwe ananena zimenezo, koma ndizo za m'badwo wa mtsogolo. Ndi za nthawi yaitali kuchokera pano?"

Iye anati, "Dikirani mpaka ine nditawona masomphenya ochokera kwa Mulungu, ndiyeno ine ndidzakuuzani inu."

Anati, "Ndiye iwe unena chinthu chomwecho?"

Iye anati, "Ine ndingonena chimene Mulungu anena; palibe chinanso, palibe chowonjezera. Ine sindingakhoze kuwonjezera mawu amodzi kwa Iwo, kapena kuchotsapo Mawu amodzi kwa Iwo."

Kotero usiku umenewo, mu pemphero, Ambuye anadza kwa iye mu masomphenya. Iye anapita kunja mmawa wotsatira, iye anati...

Apo pali aneneri awiri!

<sup>79</sup> Munthu wamkulu kwambiri mu fuko, mu nkondo ndi kupenya kwa fuko, anali Zedekia. Iye anali mkulu wa aneneri, kwa mfumu. Iye anali mkulu wa aneneri ena onsewo, mwa

bungwe. Iye anapangidwa, ndi bungwe lake, mutu wa iwo onse; mwinamwake wowerenga bwino kwambiri, wophunzira bwino kwambiri, woyenera mochulukwa pa ntchitoyo. Ndipo iye anali atadzozedwa ndi Mzimu Woyera, pakuti iye akutchedwa “mneneri.” Zedi, osati mneneri wamba chabe, iye anali mneneri wa Chihebrei. Tsopano mpenyeni iye.

<sup>80</sup> Zedekia anati, “Ambuye anayankhula kwa ine, ‘Ndipangire Ine nyanga ziwiri izi za chitsulo,’ chophiphiritsa.” Mneneri kawirikawiri amapereka zophiphiritsa. “Iye anati, ‘Panga nyanga izi za chitsulo.’ Mzimu Woyera unanena kwa ine, ‘Tenga izi,’ Kudzoza kumene kunandidalitsa ine.” Musati muganize izo ngati mwansembe, koma kuti tifike pa nsonga. “Mzimu Woyera umene umayankhula mu malirime kupyolera mwa ine, Iwo umene wanditsimikizira ine, Iye anati, ‘Tenga nyanga izi, ndipo, mwa izi, muuze mfumu kuti iye akakankha Siriya mpaka kutuluka mu dzikolo. Ndipo ine ndidzamupatsanso iye dziko limene liri molondola la Israeli, mpingo.”

M’bale, ndizo zachikhazikitso kwambiri, basi pafupifupi monga Balaamu anali kumtunda kuno. Balaamu anali wachikhazikitso basi kunena monga Mose analiri. Mose... Chiwerengero cholondola cha Mulungu ndi zisanu ndi ziwiri. Ndipo Balaamu anati, “Ndimangireni ine maguwa asanu ndi awiri; nsembe zisanu ndi ziwiri zoyera, ng’ombe, ndi nkhosa zisanu ndi ziwiri.” Ndiko kuyankhula za kudza kwa Mwana wa Mulungu. Mwachikhazikitso, iye anali basi wolondola monga aliyense wa iwo.

<sup>81</sup> Ndipo pano pali Zedekia, basi wolondola mwachikhazikitso, “Pakuti dziko ili ndi la ife. Bwanji, Asiriya amenewo ndi Afilisti kumeneko akudzazitsa mimba zawo, za ana awo ndi zina zotero, adani athu, ndi chakudya chimene ana athu akukhala opanda! Pamene, Mulungu anatipatsa ife dziko ili!”

M’bale, ndiwo mtsutso wabwino. Ine ndikuganiza iye akanakhoza kukuwira izo pamaso pa Israeli, ndipo iwo akanakhoza kufuula molimba monga iwo akanakhozera. Tsopano, ine ndikuyankhula za lero tsopano. Ine ndikuyembekeza inu mukunditsatira ine. Kukuwa konse, kufuula!

<sup>82</sup> Inu mukukumbukira Davide Lamlungu latha? Mukuona? Inu kunja uko mu dziko la wailesi, kapena dziko la kulumikizana kwa lamya uku; inu simunamvere Uthenga wa Lamlungu lapita, khalani otsimikiza kuti muupeze iwo. *Kuyesa Kuti Umuchitire Mulungu Ntchito Mopanda Kukhala Okonzedwera Kuti Uyichite Iyo*, ziribe kanthu modzipereka chotani, wabwino, ziri mwamtheradi zosalandiridwa ndi Mulungu. Mwaona?

Tsopano, apa panali Zedekia, akuganiza kuti iye akulondola.

<sup>83</sup> Mikaya anati, “Ndiroleni ine ndikamufunse Mulungu.” Koteri iye anabwera uko mmawa wotsatira ndi PAKUTI ATERO AMBUYE. Iye anafufuza masomphenya ake ndi Mawu.

<sup>84</sup> Tsopano ngati iye akanati anene kwa Zedekia, “Kodi iwe ukudziwa zimene mneneri wa Baibulo apa anati zikanati zidzamuchitikire munthu uyu?”

<sup>85</sup> “Koma osati pa nthawi iyi, chifukwa munthu uyu ndi munthu wolemekezeka. Iye akuyesera.” Musati mulephere kumvetsa izi. “Iye akuyesera kuti aperekenso kwa mpingo zinthu zimene ziri za mpingo. Iye akuyesera kuti aperekenso chuma chake chibwerere,” osati zinthu Zauzimu; ngati izo zikanakhala, iye akanagwedeza fuko lonse ilo monga Eliya anachitira. Koma, kuyesa kuwapatsa iwo zinthu za katundu. “Ife tiri ndi chuma. Ndife bungwe lalikulu. Ife ndife a ilo. Ife tonse, inu nonse anthu, inu Achiprotestanti, muyenera nonse kulumikizana ndi ife.” U-nhu.

Tiri kubwera ku izo mwa pang’ono pokha. “Ndiwo onse abale ndi alongo, mulimonse.” Iwo sali! Sanakhalepo konse ndipo sadzakhala ali konse, ndi Mpingo weniweni woona wa Mulungu. Sangakhoze kukhala!

<sup>86</sup> Zindikirani, iye anawona masomphenya. Ndipo chotero iye anati, “Mulungu anayankhula kwa ine.” Tsopano, penyani, munthuyo anali wodzipereka. Iye anati, “Iye anati, ‘Panga nyanga izi, ndipo upite kumeneko pamaso pa mfumu ndi kukakankhira chakumadzulo,’” kapena dera lirilonse kumene dzikolo linali kuchokera pamene iwo anali atayima. “‘Ukakankhe, ndipo zimenezo zikakhala PAKUTI ATERO AMBUYE, kuti iye akupita kukapambana chigonjetso ndi kukabwererako, chigonjetso cha mpingo.’ Akawathamangitsira iwo kunja!” Ndizo zapafupi kwenikweni, sichoncho izo? Ndi chiyani chinali vuto?

Apa panadza Mikaya uko. Anati, “Tsopano iwe upereke uneneri wako.”

<sup>87</sup> Anati, “Pitani kumeneko! Koma ine ndinawona Israeli monga nkghosa, atabalalika, ali opanda m’busa.” Psyii! Chimodzimidzi mosiyana.

<sup>88</sup> Tsopano, ndinu osonkhana. Tsopano ndi utiyo ali kulondola? Onse a iwo, aneneri. Njira yokha imene inu mungakhoze kudziwa kusiyana mwa iwo, ndi, kufufuza izo mwa Mawu.

Anati, “Iwe ukuzipeza chotani izi?”

Iye anati, “Ine ndinamuwona Mulungu atakhala pa Mpandowachifumu.” Anati, “Ine ndinawona uphungu wonse pomuzungulira Iye.”

<sup>89</sup> Tsopano kumbukirani, Zedekia anali atanena kumene kuti iye anawona Mulungu, nayenso, ndipo Mzimu womwewo. “Ine ndinamuwona Mulungu. Iye anandiuza ine kuti ndipange



nyanga izi kuchokera ku—kuchokera ku chitsulo. Kupita kunja uko ndi kukankhira mafukowo achoke kuno, pakuti ili ndi la ife. Enawo alibe ufulu wokhala mu ilo.” Iwo akanatero ngati iwo akanakhala moyanjana ndi Mulungu. Iwo akanakhala nalo ilo, koma iwo anali atapita kutali ndi Mulungu.

Ndimomomwe bungwe lirili, mpingo. Ilo liri nawo ufulu kwa zinthu izi, koma inu mwanamizidwa nkuchoka ku izo, chifukwa inu mwapita kutali kwa Mawu a Mulungu ndi Mzimu wa Mulungu, kudzoza, kuti kutsimikizire Mawu a nyengo. Musati inu mulephere kuwumvetsa Uthenga uwu.

<sup>90</sup> Zindikirani zimene zinachitika tsopano. Iye anati, “Ine ndinamuwona Mulungu,” Mikaya anatero, “atakhalala pa Mpandowachifumu Kumwamba. Uphungu wake unali utasonkhana momuzungulira Iye. Iye anati, ‘Ndi ndani yemwe ife tingakhoze kumupeza kuti apite pansu ndi kukamunyenga Ahabu, kuti tipangitse mawu a Eliya kubwera mowona; mneneri Wanga yemwe anali wotsimikiziridwa. Ine ndinayankhula kuti iye akanadzabwera. Ndipo Eliya anali nawo Mawu Anga. Ndipo miyamba ndi dziko zidzapita, koma Mawu Anga sadzalephera ayi. Ine sindikusamala kaya iwo akhala amakono chotani, kapena kaya iwo akhala abwino motani, kapena kaya akhala ophunzira chotani, kapena kaya iwo ali aakulu chotani, Mawu Anga sadzalephera konse.’

Ndipo mzimu wabodza unatulukira kuchokera ku gehena, unagwa pansu pa maondo ake, ndipo unati, ‘Ngati Inu mutati mungondiroleza ine, ine ndikhoza kuwapatsa iwo kudzoza kwanga, kuwapangitsa iwo kumachita mtundu uliwonse wa chizindikiro kapena chodabwitsa, malingana ngati ine nditi ndiwachotse iwo pa Mawu. Iye sadzadziwa ngakhale konse kuti Awo ndi Mawu Anu. Iye adzawanyalanyaza Iwo, pofuna kutchuka.’” M’bale, nthawi sizinasinthe. M’bale Neville, ndizo zooni. Inu mukumbukire, ndizo zooni. “ ‘Ine ndidzafika pa iye, kumupanga iye kuti achite zinthu zomwezo zimene ena onse a iwo amachita. Ine ndidzamupangitsa iye kunenera, ndi kunena bodza.’” Ilo lingakhoze kukhala bodza chotani? Chifukwa izo zinali zosiyana ndi Mawu.

<sup>91</sup> Inu mukatenga uliwonse wa maubatizo abodza awa, zabodza *zakuti-ndi-zakuti-ndi-zakuti*, ine sindikusamala kaya izo zikumveka kwenikweni chotani, mochuluka chotani iwo ali kuyesera kukopera izo, ndi bodza ngati ziri zosiyana ndi Mawu a Mulungu a ora lino. Ndizo chimodzimidzi.

Inu mukuti, “Chabwino, lathu, chabwino, ife tinachita *izi*, ndipo ife tikuchita *izi*, ndipo mpingo wathu uli mwanjira *iyi* ndi *iyi*.”

Ine sindikusamala chimene icho chiri. Ngati chiri chosiyana ndi Mawu olembedwera kwa ora lino, ndi bodza. Mulungu sadzakhala nako kanthu kochita ndi izo, ziribe kanthu

modzipereka chotani, ophunzira chotani, aluntha chotani, momwe zikumvekera moonana, momwe izo zikumvekera zoganzika, ngati ziri zosiyana kwa Mawu a ora lino. [M'bale agogoda kawiri pa guwa—Mkonzi.] Ife tifika mu izo mwakuya pang'ono mu maminiti angapo, nthawi ikatilola ife. Ngati ife sititero, ife tidzazitenganso izo usikuuno.

<sup>92</sup> Zindikirani, iye anali wodzipereka, munthu wabwino mopanda, kukayika. Ndipo iye anati. . . Ndiye, mwinamwake, Mikaya ananena kwa iye, osati pa nkhope yake yomwe, koma mwakuyankhula kwina, “Iwe wadzozedwa ndi mzimu wabodza.” Kodi icho sichikanakhala chinachake choti umuwuze bishopo? Koma iye anachita izo.

<sup>93</sup> Ndipo kotero bishopo uyu anayenda kubwera apo ndipo anati, “Iwe siudzakhala nane chiyanjano konse kenanso,” ndipo amamumenya iye mu nkhope. Anati, “Iwe ukudziwa kuti ine ndine munthu wotsimikiziridwa. Mpingo wanga unandipanga ine mutu wa iwo, chinthu ichi. Voti yotchuka ya anthu a Mulungu inandipanga ine ichi. Bungwe langa linandipanga ine ichi. Ndipo Mulungu anatipatsa ife dziko ili, ndipo Iye akulinga kuti ilo likhale la ife. Ndipo ine ndiri naye PAKUTI ATERO AMBUYE.” Anamumenya iye, ndi kunena, “Ndi njira iti imene Mzimu wa Mulungu unapita pamene Iwo unandichokera ine?”

<sup>94</sup> Mikaya anati, “Iwe udzayipeza iyo, limodzi la masiku awa,” pamene California ali pansa pa nyanja kutali uko, ndi zinthu zonse izi. Mwaona? “Iwe udzawona njira imene Iwo unapita, pamene iwe ukakhala mu ndende zamkati.”

<sup>95</sup> Tsopano, Ahabu, kodi iwe unena kuti chiyani? “Ine ndikumukhulupirira mneneri wanga,” iye anatero. Bwanji ngati iye akanangofufuza Mawu? Mwaona, iye sanafune kuti adziwone yekha akutembereredwa. Ndimvereni ine! Iye sanafune kudziwona yekha akutembereredwa. Palibe munthu amene amatero.

Ndipo bungwe langa- . . . m'bale wachibungwe, ndilo limene liri vuto ndi inu. Inu mumafuna kuganiza kuti inu muli kulondola, pamene, iwe mukudziwa mu mtima mwanu, pamene inu mukubatiza kugwiritsa dzina la “Atate, Mwana, Mzimu Woyera,” inu mukunama. Inu mukudziwa pamene inu mu- . . . kunena zinthu zimenezo zimene inu mukuchita, ndi kutenga maumboni oyambirira, ndi zinthu zonse monga choncho, inu mukulakwitsa. Ungakhoze bwanji umboni weniweni kukhala kuyankhula mu malirime, ndiyeno nkumayankhula mosiyana ndi lonjezo la Mulungu mu ora lino? Izo zingakhoze kukhala motani? Inu simukufuna themberero, sichoncho inu? Koma *Pano* izo zalembedwa, kotero izo zidzakhala ziri. Ndicho chilemba cha chirombo, zapafupi kwambiri kuti zikanadzanyenga ngakhale Osankhidwa ngati izo zikanakhala zotheka.

<sup>96</sup> Chizindikiro chirichonse, chodabwitsa chirichonse, munthu wodzozedwa, uneneri, mtundu uliwonse wa zinthu uli nkuchitika; mitundu iliyonse ya zizindikiro, mitundu iliyonse ya zodabwitsa, iwe ungadziwe motani kusiyanitsa kwake? Penyani Mawu a ora lino. Ndi momwe iwe umatenga . . .

<sup>97</sup> Penyani Mose, momwe iye akanakhozera kumuuza Balaamu. Penyani Mikaya pano, ife tinali kudziwa bwanji kuti iye anali kulondola? Mawu, asanakhalepo iye, anali atalosera izo kwa Ahabu. [M'bale Branham akugogoda pa guwa kangapo—Mkonzi.]

Ndipo Mawu, tisanakhalepo ife, analosera mabungwe awa a tsiku lino, ndi themberero ili pa iwo. Ndi zinthu zimene zikanati zidzachitike ndi Mpingo Wake wodzozedwa moona, udzakhala nawo Mawu, Mkwatibwi wa Mawu. Pano ife tiri. Ndi izi pano, lero, basi monga izo zinaliri pamenepo.

<sup>98</sup> Baibulo linati, “Mkamwa mwa mboni ziwiri kapena zitatu mulole mawu aliwonse akhale okhazikitsidwa.” Ine ndinayankhula za Balaamu, ine ndinayankhula za Balaamu ndi za Mose. Ndipo ine ndayankhula tsopano za Mikaya ndi Zedekia. Tsopano ine ndikuti ndipereke mmodzi winanso. Chimene, alipo mazana a iwo, koma umodzi winanso, kuti tipange mboni zitatu. Ine ndiri nacho chingwe chathunthu cha iwo ndawalemba apa; koma kuti tisunge nthawi.

<sup>99</sup> Yeremia yemwe anali mneneri wotsimikiziridwa, wokanidwa, koma mneneri wotsimikiziridwa wa Mulungu. Iwo ankamuda munthuyo. Iwo anaponyera chosa- . . . chipatso chakucha kwambiri pa iye, ndi china chirichonse. Ndipo iye anayika themberero pa iwo. Ndi zinthu zimene iye anachita, ndipo anagona pamenepo pa mbali zake, ndi zinthu, ndi kupereka zizindikiro kuti Israeli anali kulakwitsa.

Mneneri aliyense, mneneri woona yemwe anayamba waukapo mu dziko, ankatemberera mabungwe achipembedzo awo a mpingo. Izo zikanakhoza kusintha motani, ndi Mulungu wosasintha?

<sup>100</sup> Mzimu Woyera ndiwo Mneneri wa ora lino; Iye akuvomerezera Mawu Ake, kuwatsimikizira Iwo. Mzimu Woyera unali Mneneri wa ora la Mose. Mzimu Woyera unali Mneneri wa ora la Mikaya. Mzimu Woyera, umene unalemba Mawu, umabwera ndipo umawatsimikizira Mawu.

<sup>101</sup> Tsopano nchiyani chinachitika mu nthawi ya Mikaya? Ahabu anaphedwa, ndipo agaru ananyambita magazi ake, molingana ndi Mawu a Mulungu.

Nonse inu aphunzitsi abodza, chotero anena Mulungu, tsiku lina inu mudzakolola zimene inu muli kufesa, inu atsogoleri akhungu a akhungu! Ine sindinakwiye. Ine ndikungokuuzani inu Choonadi. Ndipo ine sindikananena izi ngati kumtunda uko, mu chipinda chija, ngati Mzimu Woyera ukanati usati, “Kanene

izo mwa njira imeneyo.” Kodi ine ndinayamba ndakuuzanipo inu chirichonse cholakwika kupatula chimene Mulungu watsimikizira icho kukhala chiri cholondola? Galamukani, abale anga, nthawi isanathe kwambiri!

<sup>102</sup> Koma ndiroleni ine ndinene izi. Minga ikanawuka motani ndi kukhala nthula, pamene iyo inakonzedweratu ku chimenecho? Osankhidwa akanadziletsa motani kuti asaziwone izo? Chifukwa, iwo ali osankhidwa kuti aziwone izo. “Onse amene Atate andipatsa Ine adzabwera,” anatero Yesu, “koma palibe mmodzi wa iwo angakhoze kubwera kupatula Iye atawapereka kwa Ine maziko adziko asanakhazikitsidwe, pamene maina awo anayikidwa pa Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa,” osati pa wotsogolera wa mpingo, koma pa Bukhu, Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa.

<sup>103</sup> Zindikirani, Yereimiya anaimirira apo, wotsimikiziridwa pamaso pa anthu, komabe iwo ankamuda iye.

<sup>104</sup> Ndipo kotero iwo anapita uko ndipo anakapanga joko, iye anatero, ndipo analiyika ilo pa khosi lake, ndipo anapita pamaso pa anthu. Iwo anati, “O, ife ndife anthu aakulu a Mulungu. Bwanji, ife ndife Israeli. Ife tiri odzipereka kwambiri pa sunagoge wathu! Ife timabwera Lamlungu lirilonse, ife, ife timapereka nsembe, ndipo ife timapereka umo ndalama zathu. Nebukadinezara angakhoze bwanji kuletsa zinthu zoyera za Mulungu?” Ha! Machimo anu anali atachita izo.

Mulungu anati, “Ngati inu muti musunge malamulo Anga, Ine sindidzachita izi. Koma, ngati inu simutero, izo zikubwera kwa inu.” Ndiko kulondola chimodzimodzi. Zofanana basibe. Kusunga malamulo Ake, Mawu Ake a ora, chimene Iye analonjeza.

<sup>105</sup> Tsopano zindikirani. Tsopano, Yereimia, mwa chifuniro cha Mulungu, mneneri wotsimikiziridwa, ngakhale ankadedwa... Mmodzi aliyense wa iwo ankadedwa mu masiku awo. Iwo ankachita zinthu zachirendo chotero mosiyana kwa chipembedzo cha tsiku limenelo, mmodzi aliyense ankamuda iye, ngakhale mafumu ndi china chirichonse. Kotero iye anayika—joko pa khosi lake, ndipo anati, “**PAKUTI ATERO AMBUYE**. Inu mukakhala muli kumusi uko kwa zaka makumi asanu ndi awiri,” chifukwa iye anali nako kumvetsa kuchokera mu Mawu a Mulungu. “Zaka makumi asanu ndi awiri!”

<sup>106</sup> Ndiye Hanania, Hanania, ine ndikuganiza inu mumatchula chomwecho, H-a-n-a-n-i-a. Hanania, mneneri pakati pa anthu, anabwera apo, anatenga joko kulichotsa pa khosi la Yereimia, ndipo analiswa ilo. Ndipo anati, akhale wolemera wamkulu pakati pa anthu, onani, pamene izo zinali kuyankhula mosiyana kwa Mawu a Mulungu. Ndipo iye anati, “Zaka ziwiri iwo adzakhala atabwererako. **PAKUTI ATERO AMBUYE**.”

Aneneri awiri odzozedwa. Kusi yana kunali kotani pa iwo? Mmodzi anali nako kuyankhula kwa Mawu, ndipo mmodzi winayo analibe. Yeremia anati, “Ameni.”

<sup>107</sup> Pamaso pa akulu onse ndi osonkhana, Israeli yense, onani, iye ankafuna kuti awasonyeze kuti iye akanakhoza kukhala wamkulu basi monga Yeremia. “Iwe ukuziwa iwo samakukonda iwe, mulimonse. Kotero ndine mneneri, nanenso. Ndine mochulukwa mneneri kuposa iwe uliri, chifukwa iwe ukunenera bodza. Iwe ukundiiza ine kuti anthu a Mulungu akakhala pansu pa chinthu *chakuti-ndi-chakuti*?”

Ndizo zimene iwo amanena lero, koma inu mukakhala kumeneko momwemo basi, monga mpingo. Inu mwatembereredwa ndi themberero. Inu nonse mipingo, zipembedzo zikugwirira ku mwambo wawo wa munthu mmalo mwa Mawu a Mulungu, inu mwatembereredwa ndi Mulungu.

<sup>108</sup> Tsopano zindikirani, apa iye akubwera. Hanania akusomphola joko iyi kulichotsa pa khosi lake, chophiphiritsa cha Mulungu, analisiswa ilo, ndipo anati, “PAKUTI ATERO AMBUYE. Zaka ziwiri iwo adzakhala atabwerera.” Kungochita mwa chiwonetsero, “Ndine *Wakuti-ndi-wakuti*.” Chifukwa iye anayima mkati, iye anali mneneri wa mwabungwe.

<sup>109</sup> Yeremia anali munthu wa mchipululu yemwe ankakhala kwa yekha. Iye ankanenera choyipa mowatsutsa iwo nthawi zonse, chifukwa iwo anali oyipa.

Ndipo munthu uyu kuwauza iwo, “O, inu muli bwinobwino malingana ngati muliko. Malingana ngati ndinu Israeli, ndizo zonse zimene ziri zofunikira. Onani, inu, ife. . . Mulungu sikuti akachita zimenezo. Ine ndikuziwa pali chinachake chaching’ono chinachitika apa, koma musati mututumuke, musati muchite mantha.”

O, m’bale, iwo akukhalabe moyo lero. “Musati mudandaule, chirichonse chiri bwino. Ife tiri nacho chirichonse pansu pa ulamuliro. Ndife Mpingo.” Inu musati muziganiza zimenezo. Eya.

<sup>110</sup> Kotero iye anati, “Chirichonse chiri bwinobwino. Iwo adzabwerera mu zaka ziwiri. Ako ndi kanthu kakang’ono kamene kachitika. Sindicho chinthu chosazolowereka. Ife tinali nazo izo. Kungoti Nebukadineza wabwera kuno, koma Mulungu wathu asamalira zonse za izi.”

Koma Mawu ananena kuti iwo akanakakhala kumeneko zaka makumi asanu ndi awiri; mpaka m’badwo umenewo utazimirira nkutha, ndi m’badwo wina. Zaka makumi anai ndi m’badwo. “Iyi ndi pafupifupi mibadwo iwiri yomwe inu muti mukakhale kutali uko.” Ndipo Yeremia ananena izo molingana ndi Mawu a Mulungu.

<sup>111</sup> Hanania anaphwasula ilo! Yeremia anati, “Chabwino. Amen. Koma, Hanania, tiyeni ife tikumbukire izi, ife ndife tonse aneneri. Ndife atumiki.”

Ndipo ine ndikunena izi kwa inu, m’bale wanga. Tiyeni ife tikumbukire pakhalala pali aneneri ife tisanakhalepo, ndipo iwo analosera motsutsa mafumu, ndipo iwo analosera motsutsa zinthu zina zake. Koma, kumbukirani, pamene mneneri anena chirichonse, iye ayenera kunenera molingana ndi Mawu. Monga Mikaya, ndi Mose, ndi onse ena a iwo. Izo ziyenera kuti zikhale molingana ndi Mawu. Ngati izo siziri, ndiye kumbukirani zimene zimachitika.

<sup>112</sup> Ndiye, Hanania, ukali wa chilungamo chake unawuka. “Ine ndine Hanania” (mopanda kukaika), “mneneri wa Ambuye, ndipo ine ndikuti, ‘Zaka ziwiri.’” Mwa kuyankhula kwina, “Ine sindikusamala chimene Mawu akunena.” Kudzoza kwake, “Ine ndikuti, ‘Zaka ziwiri, iwo adzakhala atabwererako.’”

<sup>113</sup> Yeremia anayenda kuchoka pamaso pa iye, anapita kunja ndipo anati, “Ambuye, ine sindikusamala zimene iye wanena, ine ndikanali kukhulupirira ndi kudziwa kuti Mawu ananena chomwecho. Ine ndikhala moona kwa Inu. Ine sindinyengedwa ndi iye.”

<sup>114</sup> Mulungu anati, “Pita ukamuuze Hanania, ‘Ine ndilipanga ilo la chitsulo, goli lotsatira.’” Ndipo chifukwa iye anachita icho, iye anatengedwa nachotsedwa pamaso a dziko lapansi, Hanania ameneyo, chaka icho chomwe.

Apo pali zitsanzo zathu, onse aneneri. Zochulukana zina zambiri zikanakhoza kunenedwa ndipo zikanakambidwa pa nthawi ino.

<sup>115</sup> Koma penyani. Yesu ananena, kuti, mu nthawi yotsiriza iyi, kachiwiri, mizimu iwiri idzakhala ili yoyandikana kwenikweni palimodzi kachiwiri. Ndi kulondola uko? [Osonkhana akuti, “Amen.”—Mkonzi.] Tsopano zindikirani. Iyo idzakhala ili yoyandikirana kwambiri kuposa iyo inaliri. Ino ndi nthawi yotsiriza. O, ana! Mulungu chitirani chifundo pa ife! Mpaka, “Iyo ikanakhoza ngakhale kukhala yeniyeni kwambiri mpaka iyo ikanadzanyenga Osankhidwa amene ngati nkotheke.” Tsopano inu mupita chotani, ife tinali kuyidziwa chotani iyo mu masiku amenewo? Inu muyidziwa chotani iyo lero? Njira yomweyo, kukhala ndi Mawu, “Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi nthawizonse.”

Tsopano samalani Uthenga wonse uwu. Ndipo pamene inu muti muzikamvetsera ku tepi, ngakhale mwina wake ine ndidzakhala nditapita tsiku lina pamene Ambuye atsiriza ndi ine pa dziko lapansi pano, inu mudzanene mobwerera ku izi. Mvetserani ku liwu langa, chimene ine ndikukuuzani inu. Ngati iye atanditenge ine kusanafike Kudza Kwake, ingokumbukirani,

ine ndayankhula kwa inu mu Dzina la Ambuye, mwa Mawu a Ambuye. Inde.

<sup>116</sup> Zindikirani, “Kukhala yoyandikana kwambiri limodzi mwakuti iyo ikanadzanyenga Osankhidwa ngati izo zikanakhala zotheka,” akanadzachita zizindikiro zomwezo, zozizwitsa zomwezo, mwa Mzimu womwewo. Ndi kulondola uko? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Monga ngati aneneri anali amene ife tangokamba za iwo, aneneri. Tsopano, ndiponso izo zinalembedwa . . .

<sup>117</sup> Tiyeni titembenuzire kwa izo, chifukwa cha ichi, ngati inu mukufuna kutero, Timoteo Wachiwiri 3. Tiyeni tisati tichisiye ichi. Ndipo ine sindikufuna kuti . . .

<sup>118</sup> Ine ndikuyang’ana pa koloko iyo apo, ndipo ine—ine ndikufuna kulumpha zochuluka za izi, ndipo ine sindikuganiza kuti ife tiyenera kuchita izo tsopano. Mukuona? Zindikirani. Basi . . . Ngati ine ndikuyima pano, kuchita thukuta monga ine ndikuchitira, onani, koma ine ndiri wokondwa. Ndipo ine ndikudziwa kuti izi ziri zooni. Timoteo Wachiwiri 3:8.

<sup>119</sup> Paulo, mwamuna yemwe anati, “Ngati Mngelo adza kuchokera Kumwamba ndi kumayankhula mawu ena aliwonse kwa inu osiyana ndi amene ine ndinawanena, msiyeni iye akhale wotembereredwa,” tsopano, Mngelo anabwera pansu. Ndiye Atesalonika Wachiwiri . . . O, ine ndikupepesa.

<sup>120</sup> Zindikirani mu Timoteo Wachiwiri 3:8. Penyani Paulo akuyankhula tsopano. Tiyeni tiyambire ndi pafupi . . . Tiyeni tiyambire poyambira pa ndime, ndipo mveterani tsopano mwatcheru kwenikweni. Inu amene muli nalo Baibulo lanu, werengani ndi ine. Inu amene mulibe Baibulo lanu, mveterani mwatcheru. A . . .

*Ichi dziwaninso, kuti mu masiku otsiriza . . .*

Lembani mzere pansu apo, “masiku otsiriza.” Ndi pamene izo ziti zidzachitike.

*. . . nthawi zowopsya zidzadza. (Ife tiri mu izo.)*

*Pakuti anthu adzakhala odzikonda iwo okha, osilira, odzitamandira, odzikuza, amwano, osamvera kwa akuwabala, osayamika, osayera,*

<sup>121</sup> Tapenyani pa gulu ili limene ife tiri nalo lero, lovunda. Ngakhale mwa amuna kunja pa msewu, anyamata, kukokera tsitsi lawo pansu pa mphumi zawo, monga lambiri ngati mkazi. Chisokonezeko! Chisodomu!

<sup>122</sup> Kodi inu munawerenga mu chaka chino, *Reader’s Digest* ya mwezi uno? Anati, “Anthu Achiamereka pa usinkhu,” umene ine ndikuganiza iwo unali, “pakati pa usinkhu wa zaka makumi awiri ndi makumi awiri ndi zisanu, ali kale mu chikhalidwe cha usinkhu wawo wapakati.” Iwo atha! Iwo avunda! Sayansi ikunena zimenezo, kuti mwamuna amakhala mu usinkhu wake

wapakati, ndi mkazi, pamene iwo anakali chabe koyambirira kwawo kwa makumi awiri. Thupi lawo ndi lovunda kwambiri ndi loperekedwa ku nyansi.

<sup>123</sup> O, Amereka, ndi mowirikiza kangati Mulungu akanati akufungatireni inu, koma tsopano ora lanu lafika! Inu mukutsogolera dziko mu nyansi.

*...amwano, osamvera kwa akuwabala, osayamika, osayera,*

*Opanda chikondi chachibadwidwe, . . .*

Opanda chikondi chowona ngakhale kwa wina ndi mzake, mwamuna kwa mkazi, mkazi kwa mwamuna. “Opanda nkomwe chikondi chachibadwidwe.” Nyansi, mwakugonana!

*...osagwirizanika, onenerana mwabodza, osadzigwira, aukali, ndi onyoza iwo amene ali abwino,*

Mwa kuyankhula kwina, kuti, “Inu gulu la oyera odzigudubuzi.” Winawake anafunsa funso tsiku lina za kubwera kuno ku mpingo. Anati, “Musati mupite uko. Zonse zimene izo ziri ndi chiphokoso chachikulu ndi kupitiriza.”

Onani, “onyoza a iwo.”

*owukira, a mmutu, odzikuza, okonda zosangalatsa kuposa kukonda Mulungu;*

Inu mukuti, “M’bale Branham, ndicho chikominisi.” Ndime yotsatirayo ikuti chiyani?”

*Okhala nawo mawonekedwe aumulungu, koma (chiyani?) kumakana mphamvu yakeyo: (Mawu, Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi nthawizonse, kuwonetseredwa, lonjezo la tsikuli) . . .*

Chimodzimodzi basi monga Hanania, chimodzimodzi basi monga Zedekia, chimodzimodzi basi monga Balaamu, kupita mmbuyo, aneneri ena abodza.

*Okhala nawo mawonekedwe aumulungu, odzozedwa . . . Mwaona?*

*Okhala nawo mawonekedwe, odzozedwa, atumiki oyikidwa . . .*

*Okhala nawo mawonekedwe aumulungu, koma kumakana kuti Iye ali yemweyo dzulo, lero . . . Kumakana Mawu Ake!*

Kodi iwo anamukana chotani Yesu mu tsiku lijalo? Kodi iwo anamukana ndani pamene iwo anamukana Yesu? Mawu. Iwo anali achipembedzo. Iwo ankaphunzitsa kuchokera mu Baibulo lawo, koma iwo anakana Mawu a tsiku liripoli.

Kodi iwo ali chiyani lero? Chinthu chomwecho, odzozedwa, akulalikira Ulaliki wa chipentekoste, koma kumakana lonjezo la tsiku liripoli la Mawu pokhala likutsimikiziridwa, “Yesu



Khristu yemweyo dzulo, lero ndi nthawizonse.” Kodi inu mukuona izo? [Osonkhana, “Ameni.”—Mkonzi.]

*Pakuti awa ali mtundu wa iwo amene amakwawira mu manyumba, ndi kutsogolera... akazi opusa olemedwa ndi tchimo, osocheretsedwa ndi zilakolako zosiyana,*

“Maphwando athu azosoka ndi *zakuti-ndi-zakuti* zathu.” Winawake kubwera mozungulira kuyesera kuti atanthauzire molakwika Mawu, ndi kumanena izi, “Zonse ndi zolondola, mlongo, kuti inu mukhale ndi tsitsi lalifupi. Musati mupereke chidwi kwa mbuli iyo. Mwaona? Kapena, ngati inu—inu muzivala izi; sizimenezo ayi, ‘ndi zimene zimatuluka kuchokera mu mtima wa munthu zimene zimamuyipitsa iye.’” Mwaona? Ndipo kodi inu mukuzindikira kuti inu mwadzozedwa ndi mzimu woyipa, wosilira, wauve? Samalani, inu mukhoza kumayimba mu kwayara, ndi tsitsi lalifupi, koma inu muli ndi mzimu woyipa. Ndizo zosiyana ndi Mawu. Ndiko kulondola. Ndizo zimene Baibulo linanena. Ndipo inu mukuti, “Chabwino, ine ndimavala akabudula. Izo sizimanditsutsa ine.”

“Aliyense amene, ngati mkazi avala chovala choyenera kwa mwamuna, ndi themberero pamaso pa Mulungu.” Mulungu wosasintha ananena zimenezo.

<sup>124</sup> O, zinthu zochulukira kwambiri, ife tingakhoze bwanji kungopyola mu zimenezo; nthawi yathu ingati ipite. Koma inu mukudziwa mokwanira kuti mudziwe chimene chiri cholondola ndi cholakwika. Ndipo ine ndingakhoze kuwapanga motani iwo kuchita izo? Ine ndingakhoze kuchita motani izo? Mukuti, “Chabwino, nanga iwe ukufuulira chiyani?” Ndine mboni yokutsutsani inu. Tsiku lina, mu Tsiku la Chiweruzo, inu simudzakhala nayo ngodya yoti inu mupiteko.

<sup>125</sup> Mikaya akanakhoza motani kuziletsa izo? Mose akanakhoza motani; akukuwa, kuyesa kuti ayimitse izo, ndipo Yoswa ndi iwo kuthamangira pakati pa anthu, ndipo Levi anasolola lupanga lake ndipo anawapha iwo, ngakhale? Iwo anapitirira patsogolo mofanana basi.

Izo zinanenedweratu kuti iwo akanati adzachite zimenezo. Ndipo iwo adzachita izo, chifukwa PAKUTI ATERO AMBUYE iwo adzachita izo. Inu mukuganiza kuti masankho amenewo adzasweka konse, chipembedzo chawo nkubwereranso ku Mawu? Ndi PAKUTI ATERO AMBUYE, iwo satero! Kodi iwo adzapita mu wotsutsakhristu? Chimodzimidzi. Ndizo PAKUTI ATERO AMBUYE, iwo adzatero! “Kotero kodi inu mukunena za chiyani?” Ine ndiyenera kuti ndikhale mboni, ndipo choteronso inu, okhulupirira onse. Penyani.

*... akazi opusa olemedwa ndi... zilakolako zosiyana,*

<sup>126</sup> “Chabwino, akazi ena onsewo amachita.” Aneneri abodza! Tsopano mvetserani. Aneneri abodza, amene ine ndikukamba za iwo. Tsopano iwo adzachita chiyani mu tsiku lotsiriza?

*...kutsogolera akazi opusa...osocheretsedwa ndi zilakolako zosiyana,*

“Chabwino, ine ndikudziwa akazi ena onse...” Chabwino, pitirirani.

<sup>127</sup> Ine ndinanena chiyani chisanachitike chochitika chachikulu ichi kuno mu California? “Inu anthu kuno mu Los Angeles, chaka chirichonse pamene ine ndibwerera kuno kuli ochulukira atsitsi lodula ndi amuna achikazi kuposa amene analipo poyambirira, alaliki ochulukira akupita mu bungwe. Inu muli opanda chowiringula! Ngati ntchito zamphamvu zikanakhala zitachitidwa mu Sodomu ndi Gomora zimene zachitidwa mwa inu, iye mwenzi akuyima lero. O, Kaperenao, iwe amene umadzitcha wekha ndi dzina la angelo, Los Angeles!” Mukuona zimene zikuchitika? Iye akupitirirabe kumene kupita pansu pa nyanja. Liti? Ine sindikudziwa pamene iye ati apite, koma iye akupita. Inu anthu aang’ono, ngati ine sindidzaziwona izo mu tsiku langa, inu mudzapenye. Iye wapita!

*Ophunzira nthawizonse, . . .osakhoza konse kubwera ku chidziwitso cha choonadi.*

Tsopano pano pali kunjenjemeretsa, pano pali gawo lonjenjemeretsa. Mvetserani kwa izi.

*Tsopano monga Yane ndi Yambre anamutsutsa Mose, chomwecho akuchita awa nawonso kukana choonadi: anthu a malingaliro ovunda, otayika pokamba za chikhulupiriro chimene chinaperekedwa kamodzi kwa oyera, ndithudi.*

“Pokamba za Chikhulupiriro.” “Ndipo iye adzatembenuzira Chikhulupiriro cha atate, kapena ana, kubwerera kwa atate.”

<sup>128</sup> “Otayika pokamba za Chikhulupiriro.” Um! Inu mukudziwa chimene otayika chimatanthauza? Ngati inu muli ndi Baibulo la Scofield, pali “h” pamenepo. Apo pomwe, akuti, “chinyengo.” Chinyengo, ndicho chimene icho chiri.

<sup>129</sup> Tsopano, miniti chabe. Ine ndikufuna kuti ndiyang’ane pa chinachake apa. Ine ndikuganiza ine ndinalimba izi molondola. Ine sindiri wotsimikiza, koma ine ndikufuna kuzinena izo, ndi kuyang’ana pa izo ndisanati ine—ine ndizinene izo. Tsopano, miniti imodzi yokha. [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.] “Otayika pokamba za Choonadi, pokamba za Chikhulupiriro.” “Chikhulupiriro”, pali Chikhulupiriro chimodzi chokha. Ndiko kulondola. “Pokamba za Chikhulupiriro, otayika!”

Tsopano ine ndikufuna kuti ndiwerenge Luka 18. Miniti yokha. Inu simukusowa...Inu mukhoza kulemba izo; inu simukusowa kuti muwerenge izo.

*Ndipo iye ananena fanizo kwa iwo mpaka kutsiriza uku, kuti anthu ayenera kuti nthawizonse azipemphera, ndipo osati. . . azifooka;*

*Kunena—kuti, Munali woweruza mu mzinda, yemwe sanali kuwopa Mulungu, ndipo sanali kulabadira munthu ayi:*

*Ndipo munali mkazi wamasiye mu mzinda womwewo; ndipo iye anadza kwa iye, kunena, Mundibwezerere ine kwa mdani wanga.*

*Ndipo iye sanati—ndipo iye sanafune ayi kwa kanthawi: koma patapita kanthawi iye ananena mwa iyeyekha, Ndingakhale sindiwopa Mulungu, kapena kusamala munthu;*

*Komabe chifukwa mkazi wamasiye uyu akundivuta ine, Ine ndimubwezerera iye, kuwopa mwa. . . kubwerabwera iye angandilemetse ine.*

*Ndipo Ambuye anati, Tamverani chimene woweruza wosalungama ananena.*

*Ndipo kodi Mulungu sadzawabwezerera ake. . . osankhidwa, amene alirira kwa iye usana ndi usiku kwa iye, ngakhale iye akupirira nawo motalika iwo?*

*Ine ndikukuuzani inu kuti iye adzawabwezerera iwo mwaliwiro. Komabe pamene Mwana wa munthu adzadza, kodi iye adzapeza chikhupiro pa dziko?*

<sup>130</sup> Tsopano ndilo funso. Apa ndi pamene ine ndimafuna kuti tifikapo, mu Chivumbulutsō 10. Ife tifika mu izo mu maminiti pang'ono, ndi ndime yina ya Lemba. Iye anati, “Mu masiku a Uthenga wa mngelo wachisanu ndi chiwiri, chinsinsi cha Mulungu chiyenera kuti chitsirizidwe.” Pano pali funso, ndilo, ngati inu mutsatira mu mzere umenewo mu ora lino, kodi icho chidzatsirizidwa? “Kodi ine ndidzachiyeza Chikhulupiro?” Kodi Malaki 4 adzakwaniritsidwa mu nthawi iyi, “Kubwezeretsa Chikhulupiro cha ana, kubwerera ku Chikhulupiro cha atate, apachiyambi, Mawu”? Mwaona?

<sup>131</sup> “Otayika, Yane ndi Yambre, monga iwo anatsutsira.” Tsopano, ndiponso, mvetsarani, Timoteo Wachiwiri 3:8. “Monga Yambu. . . anamutsutsa Mose, ndiponso mu masiku otsiriza otayika awa omwe akanadzadza,” tsopano onani pamene Ilo likunena apa, “okhala nawo mawonekedwe aumulungu,” iwo odzozedwawo. Tsopano tiyeni basi. . . Inu mubwerere ndi—ndi kukawerenga izo pamene inu mukafika kwanu, kotero kuti ine ndikhoze kutsirizitsa izi, mmawa uno, ngati ine ndingakhoze. “Otayika ponena. . .” Osati otayika mu—mu—mu kukhala moyo; iwo ndi abwino, anthu amakhalidwe.

<sup>132</sup> Tsopano zindikirani pamene Mose anapita kumusi ku Igupto, ndi uthenga wa PAKUTI ATERO AMBUYE, ndipo

unali wotsimikiziridwa; anayitana pa Israeli, amene anali anthu, osati mpingo. Israeli anali anthu; iwo sanali konse mpingo. Chifukwa, mawu akuti *mpingo* amatanthauza “iwo otulutsidwawo.” Iwo anali anthu a Mulungu. Ndiye pamene iwo anakhala odzozedwa pansi pa Mawu, ndipo natulutsidwa, iwo anakhala mpingo wa Mulungu. Ndiyeno anabwerera mmbuyo, chifukwa iwo sanakhulupirire Mawu a Mulungu, ndipo anamvetsera kwa mneneri wabodza. Ine ndikuyembekeza kuti zimenezo zikumira mkati.

Israeli, pokhala anthu a Mulungu, anatuluka pansi pa dzanja la Mulungu, odzozedwa ndi Mawu. . . ali nayo Mphamvu ya Mulungu, anawona zizindikiro ndi zodabwitsa za Mulungu. Ndiyeno pamene Mulungu anali kusunthira patsogolo ndi iwo, mneneri wabodza anabwera mkatimo, wodzozedwa, ndipo anaphunzitsa chinachake mosiyana kwa Mawu apachiyambi a Mulungu amene iwo anali atawamva; ndipo mmodzi aliyense wa iwo anawonongeka mu chipululu, kupatula anthu atatu. Tsopano gwirani izo.

<sup>133</sup> “Monga izo zinali mu masiku a Nowa, mmene miyoyo isanu ndi itatu inapulumuka ndi madzi, chotero izo zidzakhala mu kudza kwa Mwana wa munthu.” “Monga izo zinali mu masiku a Loti, mmene atatu anatuluka kuchokera mu Sodomu, chotero izo zidzakhala ziri mu nthawi pamene Mwana wa munthu ati adzaululidwe.” Ine ndikungobwereza Lemba, Mawu a Ambuye, amene, “Miyamba ndi dziko lapansi zidzachoka. . .” Iwo adzakhala apang’ono!

<sup>134</sup> Zindikirani apa. Mose akutsikira kwa Aroni. Mose anali woti akhale Mulungu. Mulungu anamuza iye kuti akhale Mulungu, anati, “Iwe ukhale Mulungu, ndipo umulole Aroni m’bale wako akhale mneneri wako. Iwe ukayike mawu mkamwa mwake ngati iwe sungakhoze kuyankhula bwino.” Anati, “Koma ndi ndani anamupanga munthu wosayankhula? Ndani anamupanga munthu kuti aziyankhula?” Ndi Ambuye.

Ndipo iye anayenda kupita kumusi kumeneko. Kodi iye anachita chiyani? Iye anachita chozizwitsa choona ndi cholungama chimene Mulungu anamuza iye kuti achichite. Mulungu anamuza iye kutero, “Pita ukaponyere ndodo yako pansi.” Anayinyamulapo iyo, ndipo iyo inali njoka. Iye anayinyamula iyo, ndipo inasandukanso kukhala ndodo. Anati, “Pita ukachite izo pamaso pa Farao, ndi kunena, ‘PAKUTI ATERO AMBUYE.’”

<sup>135</sup> Ndipo pamene Farao anawona izi, ife tikuti, “Motani, matsenga otchipa bwanji.” Anati, “Palibe kanthu kwa izo. Ndi zowerenga maganizo kapena chinthu chinachake, inu mukudziwa. Ife tiri nawo anyamata mu bungwe lathu amene angakhoze kuchita chinthu chomwecho. ‘Bwerani kuno, Abishopu *Akuti-ndi-akuti*. Ndipo, iwe, iwe ubwere kuno.’ Ife

tiri nawo iwo akhoza kuchita chinthu chomwecho.” Uyo anali Satana akuyankhula kupyolera mwa Farao.

Uja anali Mulungu akuyankhula kupyolera mwa Mose.

<sup>136</sup> Koma mpenyeni munthu uyu akutulukira. Yane ndi Yambre anayenda kubwera pamaso pa Mose, ndipo poyera pamaso pa anthu, ndipo anachita chozizwitsa chirichonse chimene Mose akanakhoza kuchita. “Iwo adzanyenga Osankhidwa omwe ngati ziri zotheka.” Kulondola kumeneko? Anachita chinthu chomwecho chimene Mose anachita. Inu mukumvetsa izo? Tsopano kumbukirani, ndi PAKUTI LIKUTERO LEMBA, kuti izo zidzabwereza kachiwiri mu masiku otsiriza.

Panali kusiyana kotani pakati pa Mose ndi Yambre?

Mose anati, “Siyani magazi abwere mu madzi.”

Ndipo aneneri abodza awa anati, “Zedi, ife tinayika magazi mu madzi, nafenso.” Ndipo izo zinachitika.

<sup>137</sup> Kotero Mose anati, “Siyani apo pabwere utitiri.” Kodi iye ankazitengera kuti izo? Molunjika kuchokera kwa Mulungu. Mwaona?

Ndipo kodi iye anachita chiyani? Iye anati, “Chabwino, zedi, ife tikhoza kubweretsa utitiri, nafenso.” Ndipo iwo anachita izo. Chozizwitsa chirichonse chimene Mose akanakhoza kuchichita, iwo amakhoza kuchichita, nawonso!

Kumbukirani, sungani zimenezo mu malingaliro, ife tikubwera ku izo, pakapita kanthawi. Iwo akhoza kuchita chirichonse chimene ena onsewo angakhoze kuchita, koma iwo sangakhoze kukhala ndi Mawu. Iwo sangakhoze kukhala ndi Mawu.

<sup>138</sup> Tsopano zindikirani, iwo anachita izo. Koma Mose, mneneri woona-wotumidwa kuchokera kwa Mulungu, wotumidwa ndi Mulungu, iye sanakangane nawo iwo, kuti, “Pano, inu simungakhoze kuchita zimenezo! Inu simungakhoze!” Iye anangowasiya iwo okha, kungowalola iwo kumapitirirabe. Iwo ali aneneri achibungwe, koma pitirirani nazo.

Mose anangopitirira patsogolo choncho, kumvetsera kwa Mulungu. Chirichonse chimene Mulungu ananena, “Tsopano iwe uchite *izi*,” Mose anapita ndipo anakachichita icho. Iye anachita chinthu chatsopano. Pamene iwo anatero, mmodzi aliyense wa iwo anali nako kutengeka kapena chinachake, apa iwo anabwera. Iwo anachita izo, nawonso, chimodzimodzi basi monga Mose anachitira.

<sup>139</sup> Tsopano zindikirani. Anyamata awa anawonekera...O, inu anthu, musati inu muphonye izi! Okopera awa, osanzira, anawonekera pambuyo pa mmodzi woonayo atapita poyamba. Mwaona? Iwo anabwera kuti adzasanzire. Onani, iwo ayenera kutero. Mdierekezi sangakhoze kulenga chirichonse; iye ali chabe wopotoza wa chapachiyambi.

Ndipo kodi tchimo ndi chiyani? Ndi chilungamo chitapotozedwa. Chigololo ndi chiyani? Kachitidwe kolondola katapotozedwa. Bodza ndi chiyani? Choonadi chitaperekedwa molakwika. Kupotoza!

Yang'anani pa Hanania, kupotoza kwa Mawu apachiyambi.  
Yang'anani pa Balaamu, kupotoza kwa Mawu apachiyambi.  
Yang'anani pa Zedekia, kupotoza kwa Mawu apachiyambi.

Ndipo Baibulo linanena kuti anyamata awa adzatulukira, pambuyo pake, kupotoza...kapena kuti adzapotoze Mawu apachiyambi ovomerezedwa ndi otsimikiziridwa kuti ali Choonadi.

<sup>140</sup> “Chita ntchito ya mlaliki,” mu ngodya ija uko, “panga kutsimikizira kwathunthu kwa utumiki wako. Pakuti nthawi idzabwera pamene iwo sadzapirira Chiphunzitso cholama, koma potsatira zilakolako zawo zomwe adzaziunjkira kwa iwo okha aphunzitsi, pokhala nawo makutu oyabwa; ndi kumapita patsogolo ndi kumachita chirichonse chimene iwo akufuna kuchita, ndipo, ‘Ziri bwino, ife tiri nazo zizindikiro zomwezo ndi zodabwitsa.’ Ndipo adzatembenezidwa kuchoka ku Choonadi, ndi kubweretsedwa mu nthano, mbalume.”

<sup>141</sup> O, kuzindikira kuti pali Mzimu Woyera, mantha amene amagwira moyo wa munthu pamene iye ayima kuti aganize momwe ziriri zenizeni ndi zomveka pamaso pathu pomwe! Kakumbeni mwalawapangodya uja kunja uko ndipo mukawerenge kachidutswa ka pepala kamene kanayikidwa mmenemo, zaka makumi atatu ndi zitatu zapitazo. Mukawone zimene Iye ananena uko pa—pa Msewu wa Chisanu ndi chiwiri, mmawa umenewo pamene mwalawapangodya uwu unkayikidwa. Tsopano penyani izo. Penyani pamusi apa pa mtsinje, pamene Mngelo wa Ambuye anabwera pansu mwa mawonekedwe a Lawi la Moto, mazana a mipingo, kapena anthu a mpingo, atayima mozungulira pa gombe; zimene Iye ananena, onani ngati izo zinafika pochitika. Onani zimene zachitika.

Ndi zolimba kwambiri. Ine ndikudziwa izo zikuwoneka zolimba, abale, kunja uko. Koma ndizo. . .Baibulo linati, Yesu anati Iyemwini, “Izo zikanadzanyenga Osankhidwa omwe ngati izo zikanakhala zotheka.” Palibe njira yozungulira izo. Iwo sadzakhoza konse kuziwona Izo. Ngati izo zikanakhala zotheka, Osankhidwa omwe akanati adzanyengedwe ndi izo.

<sup>142</sup> Zindikirani, anyamata awa anawonekera pambuyo pa wodzozedwa woona wa Mulungu atatumizidwa; mwa mneneri wake woona, Mose. Ndipo pamene Mose achita chirichonse, iwo amakhoza kusanzira icho.

<sup>143</sup> Tsopano, m'bale, mlongo, ine. . .Uwu ndi mpingo wanga womwe. Ine ndiri nawo ufulu kuti ndizilalikira zimene ine ndikufuna kutero, malingana ngati ziri zochokera mu Mawu a Mulungu. Ndipo ine sindikukutsutsani inu anthu, koma

tiyeni tingofufuza izo chifukwa cha nthawi ndi ora limene ife tikukhalamo tsopano.

Moni kwa M'bale Ruddell, kwa Junior Jackson, ndi iwo kunja kuno, mipingo yathu yapaubale. Ine ndinawayiwala iwo, kanthawi kapitako. Ine ndikuganiza iwo atchera molumikiza kuno mmawa uno, nawonso, chifukwa chopanda—chopanda malo mu tchalitchi.

<sup>144</sup> Tangoganizani za izo tsopano, kwa miniti chabe. Iwo anachita zozizwitsa zomwezo zimene Mose anachita. Mose anabweretsa utitiri; iwo anatsanzira icho ndipo anabweretsa utitiri. Mwaona?

Mulungu anati, “Tsiku limene inu mudzadye icho, tsiku limenelo inu mudzafa.”

<sup>145</sup> Satana anabwera mozungulira ndipo anati, “Zedi, inu sikuti mudzafa. Inu mudzangokhala anzeruko. Inu mudzakhala nalo bungwe labwinoko, labwinoko. . .” Inu mukudziwa. “Inu mukudziwa zirizonse zidzakhala bwinoko kwa inu, mudzakhala ndi Kuwala kochulukira.” Onani, kupotoza chabe. Ayenera. . .

Ndipo kumbukirani, PAKUTI ATERO AMBUYE, malingana ndi Timoteo Wachiwiri 3:18, anati, “Mu masiku otsiriza, kuti Yane ndi Yambre awa adzakhala pa dziko lapansi.” Tsopano, ine ndikufuna inu muzindikire kuti alipo awiri a iwo, onani, otsanzira.

<sup>146</sup> Tsopano ife tipita mmbuyo ku Sodomu, patapita kanthawi, atatu awo, kukawapeza Angelo atatu awo amene anabwera uko, ndi kuwona kutsanzira, ndi zina zotero, kuwona, kuwona chimene chiri cholondola ndi cholakwika. Mwaona? Mwaona?

<sup>147</sup> Zindikirani, iwo anachita zozizwitsa zomwezo. Koma, zindikirani, iwo anatsanzira Mawu owona atadzozedwa kale, mwa mmodzi woona yemwe Mulungu anamutuma; anatsatira, mwachiwiri.

Ine ndikudabwa ngati ife tingakhoze kuganiza kwa miniti. Kumawatenga anthu mwa dzanja, osati kale litali, pafupi zaka makumi awiri zapitazo, ndipo chizindikiro chinkasonyeza. Mnyamata, panali zizindikiro zambiri ponseponse pa zinthu, ndi aliyense. . . Wina ali nacho icho mu dzanja lake lamanja; wina ali nacho icho mu dzanja lake lamanzere; mmodzi wina amachinunkhiza icho. Mukuona, mitundu yonse ya. . . Ndipo ine ndikudabwa. . . Mulungu sandilola ine kuti ndikuuzeni inu pa nthawi ino chimene chinali kwenikweni choonadi, koma tsiku lina inu mudzachipeza icho. Izo zinali chabe kuti zipangitse kupusa kwawo kuwonetseredwe. Izo sizinali zolondola, pa chiyambi. Ine ndidzakuuzani inu, tsiku lina, ngati Ambuye alola.

<sup>148</sup> Zindikirani, iwo anachita zozizwitsa zomwezo, koma iwo sanatero. . . Zindikirani, iwo sanachite izo mpaka Mawu

apachiyambi atatsogolera kaye, poyamba. Ndimo momwe Satana anachitira mmunda wa Edeni. Ndimo momwe iye wachitira nthawi zonse. Ndani yemwe ananenera poyamba? Mose? Ndani yemwe anabwera powonekera koyamba, Mose kapena Balaamu? Mose. Ndani yemwe anabwera powonekera poyamba, Yeremia kapena Hanania? Inu mukuona zimene ine ndikutanthauza? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.]

<sup>149</sup> Zindikirani, iwo ankawonera. Otsanzira achithupithupi, odzipereka, kumaganiza kuti iwo anali “akumuchitira Mulungu ntchito,” monga Davide anachitira, sabata latha, koma kutsanzira kwachithupithupi. Ine ndikungoyembekezera ka miniti. Ine ndikufuna inu kuti muganizire pakiti pa malo amenewa. Ngati ine sindinena izo, ndithudi Mzimu Woyera udzaziulula izo, makamaka kwa Osankhidwa. Mwaona?

<sup>150</sup> Chipembedzo cha Farao chikuti, “Ife tiri naye munthu yemwe angakhoze kuchita chinthu icho chomwe,” ndipo iwo anachita izo. Mwaona? Nchifukwa chiyani Farao anachita izi? Nchifukwa chiyani Mulungu analoleza izo? Nchifukwa chiyani Mulungu akanatumiza mneneri, wodzozedwa, moona kumusi uko kuti akachite chizindikiro pamaso pa Farao, ndiyeno nkulola kuwonera kwa chipembedzo kubwera pamenepo nkuwonera izo pamaso pa anthu? Nchifukwa chiyani kuti Iye akanamulola wosanzira kuwuka apa kuti azichita izo, ndi kuchita chinthu chomwecho chimodzimidzi chimene Mzimu weniweni wa Mulungu unachita? Onani, Lemba liyenera kuti likwaniritsidwe.

<sup>151</sup> Zindikirani, Iye anachita izi chotero kuti Iye akanawumitsa mtima wa Farao ndi Aigupto, kuti atsimikizire kuti Mose sanali mmodzi yekhayo amene anali nawo Mawu. Iwo akanakhoza kuchita chinthu chirichonse mofanana basi monga Mose akanakhoza kuchitira.

Ndipo nchifukwa chiyani Mulungu analola chinthu ichi chizichitika mu masiku otsiriza? Chotero, chinthu chomwecho monga mzimu wonama unanena kwa Zedekia, “Ife tikamutengera motani Ahabu kunja uko, kuti tipangitse zinthu izi kufika pokwaniritsidwa?” Iye akawatenga motani anthu awa, odalira mu mipingo yawo, kuti afike kunja kuno kuti chinthu ichi chifike pokwaniritsidwa, chimene Iye ananeneratu? Iwo, mu M’badwo wa Mpingo wa Laodikaya uwu, “Chifukwa iwe ukuti ndiwe ‘wolemara, ndipo susowa kanthu. Ine ndakhala monga mfumukazi.’ Wopanda kanthu! Sukudziwa iwe ayi kuti iwe uli womvetsachisoni, waumphawi, wakhungu? Ndipo Ine ndikukulangiza kuti ubwere udzagule kwa Ine.” Iye anati, “mafuta ndi golide.” Nchifukwa chiyani Iye anachita izo?

<sup>152</sup> Nchifukwa chiyani Iye analola kusanzira uku kuti kuwuke mu masiku otsiriza ano, pamene zinthu izi zikufika pokwaniritsidwa mwa Mawu owona a Mulungu; ndi kuwalola osanzira kubwera pamenepo ndi kumachita chinthu



chomwecho, ndi kumakana Mawu owona a Mulungu? Iye anachitira izo kwa Mose. Ndipo Farao anachita izo momutsutsa Mose; ndipo ajawa, Yane ndi Yambre, anachita izo momutsutsa Mose. Ndipo Baibulo linanena kuti izo zidzabwereza kachiwiri mu masiku otsiriza. Ndife pano. Tsopano, ngati izo siziri Lemba litakwaniritsidwa, kodi izo ziri pati?

<sup>153</sup> Kodi Mose anakangana nawo iwo ndi kunena, “Apa! Apa! Inu simungakhoze kuchita izo. Ine ndine mmodzi yekhayo yemwe wadzozedwa kuti azichita izo. Pano! Inu musiye izo, pakali pano?” Iye anangowasiya iwo azipita.

Kuwalola iwo kumapitirira nazo. Kumbukirani, Baibulo linati, “Monga kupusa kwawo kunachita kuwonetseredwa, chomwecho awa mu tsiku lotsiriza adzachita kuwonetseredwa,” pamene Mkwatibwi ali atakwatulidwa ndipo anatengedwa kupita mu mlengalenga. Zindikirani.

<sup>154</sup> Mose, Mawu owonetseredwa owona, sananene konse kanthu, anangolola izo zipite. Koma Iye anachita izo, kotero Iye akanakhoza kuwumitsa mtima wa Farao, kumunyenga Farao.

Iye anachita chinthu icho chomwe kuti Iye akanakhoza kumunyenga Ahabu. Ndipo mnyamata mmodzi wamng’ono uyo atayima pamenepo mwa iyeyekha, Mikaya wamng’ono, akuwauza iwo, “PAKUTI ATERO AMBUYE.” Apa panayima mmodzi wina, wadzozedwa, “PAKUTI ATERO AMBUYE.” Ndipo mosiyana, wina kwa mzake.

<sup>155</sup> Ife tikuyima lero ndi PAKUTI ATERO AMBUYE, kuti ubatizo wa madzi mu masiku otsiriza ndi woti ukhale mu Dzina la Yesu Khristu. Ndipo munthu wina akuyima ndi kumachita zozizwitsa, ndipo, wautatu.

Ndisonyezeni ine liwu loti *utatu* mu Baibulo. Ndisonyezeni ine pamene pali Amulungu atatu. Ndisonyezeni ine pamene pali zinthu zoterozo monga izo. Izo siziri mu Mawu a Mulungu. Palibe chinthu chotero monga aliyense kubatizidwa konse mu dzina la “Atate, Mwana, Mzimu Woyera,” kugwiritsa maudindo amenewo. Zinthu zonse izi, “O, zonse ndi zolondola, alongo. Zonse ndi zolondola, kungokhala ndi lalitali... tsitsi lanu lalifupi. Zonse ndi zolondola, inu simuyenera kumachita *izi, izo, kapena chinachake*. O, ndizo zamkhutu, wankhungu wina wokalama.”

Koma Baibulo linanena! Ndipo Iye analonjeza, “Mu masiku otsiriza, Iye akanadzatumiza Mzimu wa Eliya, ndipo akanadzawayitana anthu, ana a Mulungu, kubwerera ku Chikhulupiro chapachiyambi monga icho chinali pachiyambi, cha Mawu.” Mawu amenewo anatsimikiziridwa, Mwana wa munthu mu masiku otsiriza, mofanana monga izo zinali ku Sodomu; dzulo, lero, ndi nthawizonse. Iye analonjeza kudzachita zimenezo. Ndi lonjezo la Mulungu. Ndi PAKUTI ATERO AMBUYE.

<sup>156</sup> Zindikirani, iwo anachita chinthu chomwecho, basi monga Mose anachitira, mpaka Mulungu zinamukwana izo.

Tsopano kumbukirani, ndi PAKUTI ATERO AMBUYE, izo zidzafika pochitika mu tsiku lino. Tsopano, fufuzani pa dziko lonse; tengani mwambo uliwonse, tengani fuko lililonse, tengani munthu aliyense, tengani mpingo uliwonse! Ine ndikukulumulirani inu, mu Dzina la Khristu, kuti muchite izi, inu alaliki. Ine ndikukulumulirani inu kuti muwerenge manyuzipepala kapena kutenga kulingalira kulikonse kumene inu mukufuna kupitako, ndipo muwone ngati izo siziri pa dziko lapansi pakali pano. Mwaona? Mwaona?

Ndiye, Mateyu 24:24 akulondola chimodzimidzi. “Iwo odzozedwa, mwabodzwa adzauka mu masiku otsiriza, ndipo adzakhala aneneri abodza, ndipo adzanyenga ambiri.” Penyani izo mu zoyimira tsopano, pamene izo zikubwera tsopano, onani, “Adzanyenga ambiri.” “Aneneri,” ambiri; “aKhristu,” odzozedwa, ambiri; ambiri iwo osiyanawo, Amethodisti, inu mukudziwa, ndi Achibaptisti, ndi Achipentekoste, ndi ena otero. Mwaona?

Koma alipo mmodzi woona Khristu, Mzimu, ndipo ndiwo Mawu atapangidwa thupi monga Iye analonjezera kuti achite izo.

Tsopano ife tisuinthira patsogolo motalikira pang’ono chabe, ku Malemba enanso.

<sup>157</sup> Mpaka, Mulungu zinamukwana izo, ndiye izo zinatha. Kupusa kwawo kunachita kuwonetseredwa.

<sup>158</sup> Zindikirani. Kumbukirani, mankhusu amawoneka chimodzimidzi monga njere ya tirigu. Mwaona? Tsopano, inu simukanakhoza kunena, kumbuyo uko mu m’badwo wa Chilutera, “phesi linali tirigu,” komabe ilo linali nawo Moyo mwa ilo. Phesi ndi labwino, Moyo mu phesi unali wabwino, koma, kumbukirani, Moyo unapitirira patsogolo; unapitirira kuchokera kwa Elisha kupita kwa Eliya. Moyo ukupitirira kusunthira patsogolo. Koma, kumbukirani, iwo uli mu siteji ina. Iwo sungakhoze kukhalabe mu siteji imeneyo. Ife sitingakhoze kudya zovunda za m’badwo winawake. Ife sitingakhoze kudya zovunda za Chipentekoste, Chimethodisti, kapena Chibaptisti. Mwaona, izo zikukhala zovunda. Ife tiri nacho Chakudya chatsopano, Mawu a ora lino, zina zotero.

<sup>159</sup> Kumbukirani, mankhusu ali chimodzimidzi monga njere ya tirigu. Inu simungakhoze. . .Iye siyinkawoneka monga iyo mu masamba, iyo siyinkawoneka monga iyo mu ngayaye, koma iyo zedi inatero mu mankhusu. Iyo siyinkawoneka monga mu. . .Yesu Khristu yemweyo dzulo, mwa Lutera; siyinkawoneka monga iyo mwa Wesile; koma iyo zedi ikutero mu Pentekoste, “kuti inyenge Osankhidwa omwe ngati izo zikanakhala zotheka.” Mwaona? Ndi imeneyo mibadwo yanu.

<sup>160</sup> Koma kumbukirani, mpingo wa Chipentekoste uja, mu masiku otsiriza, unali Laodikaya; ndipo Khristu anakankhiridwa kunja, Njere, Tirigu, Iyemwini. Pamene Iye anayesa... Kumbukirani, pamene Iye anayesera kuti adziwonetsere Iyemwini mu mpingo, Iye anatengedwera kunja. Iwo unali ukadali mpingo, kumadzinenera kuti uli; odzozedwa.

Koma *pano* pali Mawu, Khristu Iyemwini, ndiwo Mawu odzozedwa amene ati adzabwere kwa Mkwatibwi Wake yense, Mkwatibwi. Wodzozedwa, wa madzi omwewo amene anatsirira tirigu, monga ife tinakamba za izo, naponso akutsirira namsongole, iwo odzozedwawo. Osankhidwa okha, kapena okonzedweratu, adzakhala okhoza kuti azindikire kusiyana pakati pa iwo. Tsopano, Aefeso 5:1 amakuuzani inu chomwecho, ndi za momwe izo zinaliri.

<sup>161</sup> Iwo ali odzozedwawo. Aliyense akuti, “Ulemerero kwa Mulungu! Ife tiri nawo ufulu kumusi kuno. Aleluya! Ife... O, aleluya! Ife timayankhula mu malirime, ndi kulumpha. Ife tiri nawo ufulu wa akazi; inu anthu mumayesa kuwayika iwo pansu pa mtundu wa zinthu izi.” Mwaona? Pitani patsogolo. Palibe kanthu kamene inu mungakhoze kuchita. Mukuti, “Chabwino, ife timayankhula mu malirime. Ife timafuula. Ife timavina mu Mzimu. Ife timalalikira Mawu.” Mwamtheradi. Palibe kanthu kotu tinene motsutsa izo. Chomwechonso anachita amuna awa kumbuyo uku mu Baibulo.

Yesu anati, “Izo zikanadzanyenga Osankhidwa omwe ngati izo zikanakhala zotheka, Osankhidwa omwe.”

<sup>162</sup> Tsopano zindikirani mankhusu. Kuchokera ku Njere yapachiyambi, Njere imene inapita mu nthaka, Iyo sikuti inali bungwe ayi. Iyo inali Njere imodzi, mwa Iyoyokha. Koma pamene iyo inatulukira, iyo siyinali Njere ayi; iyo inali bungwe, onani, masamba, chimanga.

Ndiye Iyo inapita mu siteji ina, imene inali ngayaye. Komabe iyo siyinali monga pachiyambi. Iyo inali bungwe.

Iyo inapita ku mankhusu, masamba ambiri, Chipentekoste, pafupifupi mwamawonekedwe ake tsopano. Penyani pa iyo. Iyo ikutenga mawonekedwe nthawi zonse, pafupifupi chimodzimidzi ngati zofanana, imawoneka chimodzimidzi monga Njere ya tirigu pamene inu muwona kakhungwa kakang’ono ako apo.

Koma potsiriza Iyo yawonetseredwa, ndipo popanda bungwe. Palibe zotengera zinanso. Bungwe liri chabe chotengera. Palibe zotengera zinanso; phesi liyenera kufa, mankhusu ayenera kufa, china chirichonseho chiyenera kufa, koma tirigu amakhalabe moyo. Ndilo thupi la chiwukitsiro, likubwera pansu pomwe ndi kuwanyamulira iwo mmwamba. “Iwo amene ali otsiriza kudzakhala oyamba, ndipo iwo amene ali oyamba kudzakhala otsiriza.” Mwaona, kuwanyamulira iwo

mmwamba momwe mu chiwukitsiro. Kodi inu mukutsatira izi? [Osonkhana, “Ameni.”—Mkonzi.] Chabwino. Zindikirani, njere ili. . .

<sup>163</sup> Mankhusu amawoneka chimodzimodzi monga njere. Ndipo munthu wolima munda wa tirigu, kapena chinachake chimzake, akhoza kuyang’ana ndi kunena, “Mulungu alemekezeke, ine ndiri nazo zokolola za tirigu,” pamene iye ali opanda kachidutswa kamodzi ka tirigu. Iye amawoneka chimodzimodzi basi monga tirigu, koma ndi mankhusu.

<sup>164</sup> Tsopano, amzanga, pitani mmbuyo ndi ine. Chitsisimutso choyamba chinabwera kuti, itachitika (imfa) masiku amene njere ya tirigu imayenera kugwera mu nthaka, Thupi, Mkwatibwi wa Khristu? Khristu anamukonza Mkwatibwi Wake, ndi kulondola uko, Mpingo Wake? Iye sanawupange konse Iwo bungwe; Iye anangokhazikitsa atumwi, ndi aneneri, ndi ena otero, mu Mpingo, kuti awusunge Iwo uli woyera. Koma ku Nicaea, Rome, zaka mazana atatu ndi zisanu ndi chimodzi kenako, iwo anawupanga iwo bungwe ndipo anapanga bungwe kuchokera mwa iwo. Ndi kulondola uko? Ndipo iwo unafa. Chirichonse chimene sichinagwirizane ndi mpingo umenewo chinayikidwa ku imfa. Ndipo iwo unakhalabe chigonere, kwa mazana a zaka, mu nthaka.

Koma, patapita kanthawi, pamwamba iwo unabwera mwa Lutera. Masamba oyamba aang’ono a chimanga anatulukira. Kachiwiri, iwo unaphuka kuchokera pamenepo. Iwo anapitirira patsogolo, anali ndi Zwingli ndi ena otero, ndi mabungwe ena ndi zina zotero. Ndiye, patapita kanthawi, kunabwera Achianglikani motsatira.

Ndiyeno nchiyani chinachitika? Apa panabwera Wesile motsatira ndi chitsisimutso chatsopano, ngayaye, zimene zimawoneka mochuluka pang’ono ngati Tirigu. Ndiye nchiyani chinachitika kwa iwo? Iwo unachita bungwe, ndipo unawuma ndipo unafa.

Moyo unapita mpaka mu mankhusu momwe, ndipo mankhusu anatulukira pamenepo pafupifupi angwiwo monga Tirigu. Koma, potsiriza, kupusa kwache kunachita kuwonetseredwa mu zaka zotsiriza zisanu ndi zitatu kapena khumi, makamaka mu zaka zitatu zotsiriza. Tsopano kodi iwo ukuchita chiyani? Kusololoka kuchoka kwa Tirigu.

<sup>165</sup> Tsopano nchifukwa chiyani apo sipanakhale pali bungwe litayamba mu zaka zotsiriza makumi awiri izi za chitsisimutso chachikulu ichi; aneneri odzozedwa ake, aphunzitsi odzozedwa, ena otero, koma nchifukwa chiyani palibe apo? Palibe kanthu kupitirira Njere. [M’bale Branham akugogoda pa guwa kanai—Mkonzi.] Mwaona, Iyo yabwerera, popanda bungwe. O, mai, munthu wakhungu akhoza kupenya izo. Iyo siyingakhoze kupanga bungwe; Iyo ili molimba yotsutsana nazo izo. Ndi njere

ya Tirigu, Iyoyeni. Mwana wa munthu adzakhala ali kuchita kuwonetseredwa. Njere ya Tirigu idzabwereranso kwa Iwoyokha kachiwiri, Mwana wa munthu mu masiku otsiriza.

“Ndipo apo padzabwera kusanzira, kwabodza kwa Iyo, mu masiku otsiriza, kumene pafupifupi kukanati kudzanyenge Osankhidwa ngati kukanatheka.” Penyani pa mankhusu awo a bungwe akuchokapo tsopano.

<sup>166</sup> Iwo akulola chabe Tirigu kuti adziwike, kwa Osankhidwa, amene ali gawo la Iye. Zindikirani kukongola kwake momwe izi zikubweretsedwera muno tsopano. Kokha...Zindikirani, iwo odzozedwawo kukhala okhoza; owona, Osankhidwa, okonzedweratu, Aefeso 5:1, kapena 1:5, kani, akanadzakhala okonzedwera, osankhidwa. Iwo ali okhawo amene sati adzanyengedwe.

Zindikirani, aneneri odzozedwa adzakhala ali abodza, ndipo pamenepo pakati pa iwo padzakhala pali odzozedwa mowona. Inu mudzadziwa motani izo? Ndi Mawu. Monga, ife tiri nazo izo mu mthunzi. Kodi inu mukuziona izo? Nenani, “Ameni.” [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Mwaona?

<sup>167</sup> Zindikirani, iwo odzozedwawo, Mawu okha adzawalekanitsa iwo, osati zizindikiro. O, ayi. Iwo adzachita zizindikiro zomwezo, koma Mawu ndiwo akuwalekanitsa iwo. Zedi. Iwo onse analosera. Iwo onse anachita *izi, izo*, ndi, *china*, zedi, mofanana basi. Yesu anati iwo akanadzachita chinthu chomwecho. Koma Mawu ndi amene anawalekanitsa iwo, zindikirani, osati zizindikiro.

<sup>168</sup> Kodi inu munazindikira? Yesu ananena apa, mu Mateyu 24. Iye sananene kuti, “Padzauka Ayesu abodza mu masiku otsiriza.” O, ayi, iwo sakanati ayime duu konse kwa icho. Ayi. Inu mumutenge Wachipentekoste yemwe ali Wachipentekoste weniweni, kunena, iyemwini, iye ali “Yesu”? Mwaona? Inu mumutenge Mmethodisti wabodza, kapena Mbaptisti, kapena winawake wonga choncho, kapena limodzi la mabungwe, ati, “Ife ndife Yesu”? Iwo amadziwa bwino kuposa zimenezo. Iwo sati achite izo. Koma Baibulo linati iwo adzakhala “A Khristu abodza,” osati, Ayesu, koma, “A Khristu abodza.” Iwo sakanati azindikire, kuti, “Ine ndine Yesu.” O, ayi.

<sup>169</sup> Koma iwo ali “aKhristu abodza,” ndipo sakudziwa izo, chifukwa iwo ali ochita mosiyana kwa Mawu. Ndipo Mulungu amatsimikizira zomwezo. Tsopano, ine ndikungobweretsa izi mpaka pansu ku chiwonetsero tsopano, chifukwa inu mwawona chinthu chomwecho chikuchitidwa ndi anthu amenewa chimene chakhala chitachitidwa mwenimweni. Ndipo Yesu ananena chomwecho.

<sup>170</sup> Tsopano, monga ine ndinanena, tsopano kwa inu anthu kunja pa, mu dziko la lamya uko, ine—ine sindiri kukutsutsani inu, koma uno ndi mpingo wanga ndi—ndi gulu langa limene

Mzimu Woyera unandiyika ine pa iwo, ndipo ine ndiyenera kuti ndiziwauza iwo Choonadi. Ora likufika pochedwa.

<sup>171</sup> Tsopano, iwo sadzayima kwa izo, koma, “aKhristu abodza,” abodza, iwo odzozedwawo, pafupifupi okhala ndi chizindikiro chirichonse ndi chilembo chirichonse cha Mawu. “Iwo amakhulupirira ubatizo wa Mzimu Woyera?” Mwamtheradi. “Kukhulupirira mu zonse *izi*?” Eee. “Amakhulupirira mu kuyankhula mmalirime?” Eee. “Kukhulupirira zizindikiro ndi zodabwitsa zikuwatsata, zizindikiro zidzawatsata iwo?” Eee. Awo sindiwo Amethodisti, awa sindiwo Achibaptisti. Ayi, ayi. Awa ndi Achipentekoste. Mwaona, ano ndi masiku otsiriza.

Tsopano, m’badwo woyamba wa mpingo sukanazindikira konse izo. M’badwo wa mpingo wa Methodisti sunazindikire konse izo; m’badwo wa mpingo wa Baptisti, iwo sanazindikire konse izo; m’badwo wa mpingo wa Presbateria, iwo sanazindikire konse izo. Koma, Achipentekoste, oyandikira kwambiri monga Chinthu chenicheni! Ndipo pamene, Tirigu, mankhusu ali pafupifupi monga Tirigu. Iwo sadzazindikira konse izo. Mwaona? Iwo sakanakhoza. Koma ndi masiku otsiriza, tsiku lino. Inde, bwana.

<sup>172</sup> Zindikirani, basi monga izo zinali pa chiyambi, kotero izo zidzakhala pa mapeto. Monga Eva anangotanthauzira molakwika Mawu amodzi, Satana anatero kwa Eva, ndipo iye anakhulupirira izo. Iye, osati mwamunayo; mpingo, osati Iye. Mwaona? Mpingo unali iwo umene unatenga mawu abodza. Mwaona? Osati Adamu; Eva. Osati Khristu; mpingo, mkwatibwi, odzozedwa, oyenera kukhala ali, amadzitcha yekha Mkwatibwi, onani, iye ali ndi mawu abodza.

Kodi inu simungakhoze kuwona izo? Bwanji, izo zikupotana palimodzi monga chingwe cha nsapato, monga msiza pa diso lanu. Bwanji, chirichonse chimene inu mudzatembenukireko, Baibulo, Ilo likukwapulira izo palimodzi. Eva, osati Adamu; Eva anakhulupirira izo, osati Adamu. Mkwatibwi lero, wotchedwa choncho, akukhulupirira izo; osati Khristu. Mkwatibwi ali ndi mitundu yonse, wotchedwa mkwatibwi; zizindikiro zofanana, zodabwitsa zofanana, chirichonse chofanana; koma osati Mmodzi weniweniyo. Mwaona? “Kunyenga Osankhidwa ngati izo zikanakhala zotheka.”

Tsopano mwamsanga, ngati ife tingakhoze kutsirizitsa izi mu maminiti khumi ndi asanu, ife tikhala pa nthawi. Zindikirani mwatcheru kwenikweni tsopano, kotero inu musati—inu simukhala mukumvetisa molakwika, kwa inu.

<sup>173</sup> Tsopano, ayi, iwo sakanayima kuti akhale akutchedwa “Yesu wabodza.” Iwo sakanakhala, akuyima kuti atchedwe, “Yesu.” Ndithudi ayi. Izo nzomveka kwambiri. Aliyense akanadziwa zimenezo. Aliyense akanadziwa kuti iwo sanali Yesu. Ine sindikusamala ngati iwo akanakhala ndi mafuta pa nsana wawo,

ndi magari pa manja ndi mmwamba-ndi-pansi pa maso awo, iwo akudziwabe zimenezo. . . Aliyense amene ali ndi kuganiza kwabwino, amadziwa kuti izo sizinali Yesu. Mwaona? Iwo sakanakhoza kuyimira izo. Koma iwo amadzitcha iwo okha “odzozedwa.” Ndipo iwo amachita zizindikiro ndi zodabwitsa, “pafupifupi kuti anyenge Osankhidwa.” “Koma aKhristu abodza, iwo odzozedwawo, adzauka, ndipo adzanyenga Osankhidwa ngati izo zikanakhala zotheka.”

<sup>174</sup> Tsopano penyani mwacheru. Musati muphonye neno ili, chifukwa ndi loyenera kulimvetsera.

Iye akungoyika zomata zina pa choyankhulirapo ichi pano, kuchiteteza icho kuti chingaulukepo. Ine ndakhala ndikuchita thukuta; lagwera pa tepi, inu mukuona.

<sup>175</sup> Ndipo kotero izo zidzakhala ziri basi monga Ilo, Baibulo, linati izo zikanati zidzakhale. Mwaona?

<sup>176</sup> Zindikirani, osati Ayesu abodza. “aKhristu abodza!” Iwo amakhulupirira kuti iwo ali odzozedwa, koma iwo amadziwa kuti iwo sali Yesu. Mwaona, ndizo zomveka kwambiri. Ngati munthu akanapita uko ndipo akanati, lero, “Penyani pa zipsyera mu dzanja langa. Penyani pa mphumi panga. Ine ndine Yesu.” Chabwino, tsopano, ife tikudziwa kuti izo ndi zolakwika. Ndipo, kumbukirani, Yesu sananene konse kuti anyamata amenewo akanadzawonekera. Iye anati padzawonekera “A Khristu abodza.” “A Khristu,” ambiri, zipembedzo, ndi zina zotero, *iwo odzozedwawo*; odzozedwa ndi mzimu wa chipembedzo, ndipo osati Mawu. Inu mukutsatira izo? Osati Yesu wabodza. “A Khristu abodza,” iwo odzozedwa, mwabodzawo. Mukuona? O, ndi zomveka bwanji! Motani ife. . . Zedi inu simuphonya izi!

<sup>177</sup> Tsopano, kumbukirani, ine nthawizonse ndakuuzani inu kuti pali magari atatu a anthu. Pali mitundu itatu ya anthu; Hamu, Shemu, ndi Yafeti, mitundu itatu. Magulu atatu, ndipo ine ndinati, amenewo ndi wokhulupirira, wodzipangitsa-kukhulupirira, ndi wosakhulupirira. Izo nthawizonse zakhala, nthawizonse zidzakhala ziri. Mwaona? Panali Mose, wokhulupirira; panali Yane ndi Yambre; osakhulupirira. Mwaona? Panali Balaamu; Mose. . . Nthawizonse makalasi atatu a anthu amenewo, magari atatu; wokhulupirira, wodzipangitsa-kukhulupirira, ndi wosakhulupirira.

<sup>178</sup> Tsopano kumbukirani, wosakhulupirira, mpingo wachipembedzo, sumakhulupirira mu zizindikiro zirizonse nkomwe; wozizira, wamawonekedwe, wokhuthara, mpingo mu dziko, chipembedzo. Koma wodzipangitsa-kukhulupirira ali mankhusu aja. Ndiye mnyamata amene amadzipangitsa-kukhulupirira. Ndiyeno pali wokhulupirira weniweni yemwe ali woona kwenikweni. Tsopano, apenyeni iwo pamene iwo akupita motsatira tsopano, kwa miniti chabe.

179 Ndipo zindikirani momwe aliri olimbamtima osakhulupirira awa, kapena odzipangitsa-kukhulupirira awa ndi osakhulupirira. Mai! Iwo ndi olimbamtima, penyani, ngakhale monga Satana anayima mu Kukhalapo komwe kwa Mawu owona, ndipo anati, “Izo zinalembedwa!” Ndi kulondola uko?

Nchifukwa chiyani Satana anachita zimenezo? Ndi chifukwa iye sankawadziwa Mawu a ilo. . . Iye ankadziwa kuti Mawuwo anali a ora limenelo, koma iye ankamukayikira Munthu wamng’ono wodzichepetsa uyu kukhala Mawu amenewo. “Ngati Iwe uli Mwana wa Mulungu. Ine ndikudziwa kuti Mwana wa Mulungu akubwera, chifukwa Iwo anati Iye akanadzachita izo. Ndipo izo zalembedwa, ‘Iye adzawapatsa Angelo Ake ulamuliro pa Iwe.’ Mwaona? Tsimikizira izo kwa ine! Chita chozizwitsa! Ndirole ine ndikuone Iwe ukuchita izo.” Mwaona? Mwaona?

Mwaona, wosakhulupirira, wodzipangitsa-kukhulupirira, wokopera. Tayang’anani pa Yudasi pakati pawo pomwe, nthawi yomweyo, wodzipangitsa-kukhulupirira! Mwaona? Zindikirani, ndipo apo panali Mawu owona.

180 Iwo ali olimbamtima bwanji! “Tsopano, musati mupereke tcheru chirichonse kwa zamkhutu zimenezo. Palibe kanthu kwa Izo. Musati mupite kumeneko. Ilo ndi gulu la phokoso chabe. Palibe kanthu kwa Izo. Izo ndi zopeka basi zonsezo. Ndi zimene ziri mu malingaliro anu.” Mukuona, mukuona zimene ine ndikutanthauza? Kuyima mu Kukhalapo kumene kwa Mawu ndi kumanena izo.

181 Satana anayenda mpaka mkati. Monga Baibulo linanena uku mu Yuda, “Ngakhale Mngelowamkulu, pamene ankatsutsana ndi Satana, anati, ‘Ambuye akudzuzule iwe.’” Motsutsa Mawu Iyemwini!

Ndipo pano pali wotsutsakhristu, wodzozedwa, atayima pomwe apa motsutsa Mawu owona a tsikuli, Yesu Khristu, ndipo anati, “Izo zalembedwa.”

182 Yang’anani pa masiku otsiriza, “Iyo idzakhala yoyandikira kwambiri mwakuti ikanadzanyenga Osankhidwa omwe ngati izo zikanakhala zotheka.” O, mai! Chifukwa chimene Osankhidwa sadzakhoza kunyengedwa, inu mukudziwa chifukwa chake? Ndi chifukwa iwo ali Mawu. Mwaona? Basi monga Moyo umene uli mu muzu, ine ndinanena kanthawi kapitako, Iwo sungakhoze kudzikana Wokha. Mwaona, Iwo uli Mawu ndipo mu nyengo ya Mawu. Ndiko kulondola.

183 Monga ngati Yeremia, iye ankadziwa. Ziribe kanthu zimene Hanania ananena, iye ankadziwa pamene iye anali. Ndipo ndizo chimodzimidzi monga Mose anachitira, ndi—ndi ena onse a iwo. Ndizo, iye anadziwa, ziribe kanthu zimene mneneri wabodza ananena, apo panali Mawu a Mulungu. Izo zinalembedwa.

Ndicho chifukwa Mikaya akanakhoza kunena, “Chabwino, inu mungoyembekezera ndi kuwona.”



Ahabu anati, “Ine ndikuwakhulupirira aneneri anga. Bungwe langa liri kulondola. Pamene ine nditi ndibwerereko mu mtendere...Muyikeni munthu ameneyo kuseri uko mu ndende. Ine ndidzasamalira za iye! Mupatseni iye mkate wa zowawa. Mtembenuzeni iye atuluke, musakhale ndi chiyanjano ayi ndi iye konse. Pamene ine nditi ndibwerere mu mtendere, ife tidzasamalira za munthu ameneyo.”

<sup>184</sup> Mikaya anati, “Ngati inu mukabwerera konse, Ambuye sanayankhule kwa ine.” Iye ankadziwa kuti iye anali ndi PAKUTI ATERO AMBUYE, ndipo masomphenya ake anali chimodzimidzi ndi PAKUTI ATERO AMBUYE; osati a nyengo ina yake, koma a nyengo imeneyo. Ameni! Aleluya! Nyengoyo!

<sup>185</sup> Molimba, kuimirira ndi kumatsutsana ndi Mngelowamkulu! Izo zinanenedwapo kale, kuti, “Zitsiru zimayenda ndi nsapato za gogoda pamene Angelo amawopa kuyendapo.” Ndiko kulondola.

<sup>186</sup> Chifukwa chimene Osankhidwa, Yesu anati, sadzakhoza kunyengedwa, chifukwa iwo ali Mawu amenewo. Iwo sangakhoze kukhala china chirichonse. Iwo sangakhoze kumva kanthu kena kalikonse. Iwo sakudziwa kanthu kena kalikonse. Ndiko kulondola.

Kumbukirani, Mose sanali atatengeka ndi kusanzira kwawo konseko. Anatero iye? Mose anati, “Tsopano, dikirani miniti, Farao. Inu mukudziwa chiyani? Ambuye anandiuzwa ine kuti ndichite izi, koma, ulemerero kwa Mulungu, ine ndikuwona kuti anyamata anu akhoza kuchita chinthu chomwecho. Koteru, ndikuuzani inu chimene ine nditi ndichite, ine ndilumikizana nanu inu”? A! Zimenezo sizikumveka ngati mneneri wa Mulungu. Ayi, indedi! Iye anayima molimba basi monga iye akanakhoza kuyima. Iye ankadziwa, chimodzimidzi, Mulungu akanadzasamalira izo mwanjira ina, chifukwa Iye analonjeza kutero. “Ine ndidzakhala ndi inu. Ine sindidzakusiyani inu.”

<sup>187</sup> Iye ankadziwa, koteru iye sanalumikizane nawo iwo. O, ayi. Iye anakhala molondola ndi iwo. Iye sankafuna chirichonse cha zipembedzo zawo. Iye anakhala molondola ndi Mulungu. Iye sanatengekere kutali ndi zinthu zonse zimene iwo akanakhoza kuchita. Pamene iwo anachita chinthu chimodzi...Iye anabweretsa nsabwe; iwo anabweretsa nsabwe. Iye anabweretsa magazi; iwo anabweretsa magazi. Iye anabweretsa chirichonse; iwo anamusanzira iye njira iliyonse, motsatira kumene. Iye anangoyima duu. Iye ankadziwa chimodzimidzi chiyani. Mulungu anali pa ntchito.

Inu mukumvetsa tsopano? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Inu mukutenga ziwiri ndi ziwiri, ndi kupanga zinayi? [“Ameni.”] Inu simukufuna kuwotchedwa molimba kwambiri. Koteru, koteru inu—inu mukumvetsa, mwaona.

<sup>188</sup> Chifukwa chiyani? Iwo sati adzanyengedwe ndi Izo. Wokhulupirira weniweni, iwo ali Mbewu yokonzedweratu imene ili yoti iyime mu tsikuli.

<sup>189</sup> Kungoti, ndiponso, Yesu ananena izi, “Ambiri adzabwera mu tsiku limenelo, mu Dzina Langa, ndi kunena, ‘Ambuye, kodi ine sindinatulutse ziwanda mu Dzina Lanu?’” Yesu anati, “Pa masiku otsiriza, pamene nthawi ili itatha yonse ndipo chiwukitsiro chachikulu chitabwera, kuti ambiri adzabwera ndi kudzakhala pansu mu Ufumu.” Ufumu wa Mulungu uli mwa inu.

Ambiri, maudzu adzabwera ndi kukhala basi pansu ndi Tirigu, kunena, “Tsopano, dikirani miniti, Ambuye! Ine ndinayankhula mu malirime. Ine ndinafuula. Ine ndinavina mu Mzimu. Ine ndinatulutsa ziwanda. Ine ndinayankhula ndi malirime. Ine ndinachita zinthu zonse izi.”

Kodi Iye akanadzati chiyani? Zindikirani. “Inu antchito za kusaweruzika, Ine sindinakudziweni inu nkomwe.”

<sup>190</sup> *Kusaweruzika* ndi chiyani? Mfuseni winawake. Ndicho “chinachake chimene iwe ukudziwa kuti uyenera kuti uchichite, ndipo iwe suchichita icho.” Iwo amawadziwa Mawu amenewo. Iwo amawamva Iwo. Inu mukumvetsera ku tepi iyi. Inu mukumvetsera ku Uthenga uwu. Inu mukuona Ambuye Mulungu akunena chomwecho; inu mukuwona Iye akutsimikizira izo, kuzipanga izo kukhala zoono. Ndipo inu mukudziwa Izi momveka basi momwe dzuwa likuwalira kunjja, koma inu amene muti mudzagwire ku chipembedzo chanu, kugwira ku zinthu zabodza izo; inu akuchita za kusaweruzika!

“O, inde, ine ndinali nayo misonkhano yayikulu. Ine ndinachita *izi*. Ine ndinachita *izo*.”

Anati, “Inu chokani kwa Ine, inu akuchita za kusaweruzika, ine sindinakudziweni inu konse.”

<sup>191</sup> “Chabwino, Mzimu Woyera unagwera pa ine.” Ine sindikukayika zimenezo pang’ono. “Ine ndinayankhula mu malirime. Ine ndinayimba mu Mzimu. Ine ndinachita...” Ine sindikukayika zimenezo pang’ono. Palibe funso kwa izo. O, m’bale, mlongo, ndi chikhaliidwe cha mtundu wanji!

Ino ndi nthawi yonjenjemera. Kodi ife tiri pati? Mawu awa akubwera ku Moyo tsopano. Zindikirani.

<sup>192</sup> Eya, Iye anati iwo akanadzachita zimenezo. Zindikirani, “Inu antchito za kusaweruzika.” Ine ndiri nalo Lemba ndalilemba apa. Ine sindikudziwa basi pamene izo zinali. Ine ndatenga nthawi yochuluka kwambiri. Ine ndiliyang’ana ilo, miniti chabe, ndi kuwona chimene ilo linali. Ine ndiri—ine ndiri ndi Mateyu 7:21. Ine—ine basi sindikudziwa malo ake. Ine, nthawizina ine sindimalemba kenakake ndi icho, chabwino, ine—ine kulalikirira monga chonchi, ine—ine ndikuyiwala zimene ine ndinali kulozerako pa Lemba. Mateyu 7:21.

*Osati aliyense amene anena kwa ine, Ambuye, Ambuye, ati adzalowe mu ufumu wa kumwamba; koma iye amene achita chifuniro cha Atate anga amene ali kumwamba.*

*Ambiri adzanena kwa ine mu tsiku limenelo, Ambuye, Ambuye, kodi ife sitinanenere. . .*

Aneneri, iwo odzozedwawo! Uko nkulondola? “Kodi ife sitinali aneneri? Kodi ife sitinali odzozedwa, iye wodzozedwayo? Kodi ine sindinanenere mu Dzina Lanu? Ndipo mu Dzina Lanu kodi ine sindinatulutse ziwanda?” Inu mungamachite bwanji izo, ndi kumakana kuti mubatizidwe mu Dzina la Yesu? Mwaona? O, mai! Mukuona kunyenga kwake? Mpaka pa mfundo iyo yomwe, ndiye nkugwera mmbuyo. Iwo amapita mpaka ku Mawu, ndiye nkugwera mmbuyo. Tsopano penyani izi. Ife tizitulutsa izi kunj, miniti yokha.

*Ambiri adzanena kwa ine. . . Ambuye, Ambuye, kodi ife sitinanenere, ife takhala tiri aneneri? . . .*

Eya, ine ndinayankhula za izo mu Mateyu 24:24.

*. . . ndipo mu dzina lanu. . . kutulutsa adierekezi? ndipo mu dzina lanu ndinachita zambiri zoda- . . . ntchito zambiri?*

*Ndiyeno Ine ndidzavomereza kwa iwo, ine sindinakudziweni inu nkomwe: chokani kwa ine, inu akuchita kusaweruzika.*

“Pamene Iwo anayikidwa pamaso panu pomwe ndipo inu munawawona Iwo, ndipo munawaona Iwo akusuntha, munawaona Iwo anali Mawu; ndipo chifukwa cha chipembedzo chanu, ine munakanirira kwa icho. Ine sindinakudziweni inu nkomwe. Ine sindikusamala kuti ndi adierekezi angati amene inu munawatulutsa, ndi zingati inu munachita izi ndi izo; ine sindinadziwe kanthu za inu.”

Balaamu anati, “Ine ndinanenera molondola, mu Dzina Lanu. Izo zinafika pochitika.”

<sup>193</sup> “Ndiko kulondola chimodzimidzi, koma, pamene izo zinafika ku Mawu iwe unawakana Iwo.”

O, m’bale, mukuona gawo lonyengalo? Osati “mneneri,” chimodzimidzi; koma ndi Mawu, Mawu owona, Mawu otsimikiziridwa atachita kuwonetseredwa. “Inu antchito za kusaweruzika!”

<sup>194</sup> Kuyesa, Satana wayesa mu mibadwo yonse kuti asanzire Mawu owona. Ife tikudziwa zimenezo, sichoncho ife?

<sup>195</sup> Zindikirani, kubwera mpaka ku mzere wa mmalire ndi kusiya. Penyani apa, Iye anati, mu Ahebri mutu wa 6, tsopano, ife tinali kuwerenga kanthawi kapitako. Ine ndinakuuzani inu

kuti tikamba mobwerera kwa iyo, ndipo ife titero kwa maminiti angapo otsatira. Iye anati:

...koma *minga ndi* nthula...zimene *zayandikira ku* kukanidwa; *zimene mapeto ake ali oti ziwotchedwe.* (Ammalire!)

...inu amene *mwalawa...mphatso yakumwamba...*

“Mwalawa,” mwa kuyankhula kwina, inu mwawaona Iwo! Inu simungakhoze [M’bale Branham amenyetsa milomo yake limodzi—Mkonzi.] kulawa chabe Iwo ndi kamwa yanu. Koma inu munawaona Iwo, ndipo inu munawadziwa Iwo kuti anali Choonadi. Inu munawadziwa kuti Iwo anali Choonadi. “Munalawa mphatso Yakumwamba.”

...ndipo *munapangidwa kukhala ogawana nawo za* Mzimu Woyera, pamene Iwo unagwera pa inu,

...*munalawa za mawu abwino a Mulungu...*

“Munalawa,” inu munawaona kuti Iwo anali olondola. “Ndipo Mzimu Woyera nkugwera pa inu,” udzu mmunda.

...ndiyeno nkutembenuka *kuchokako...*

“Kumukana Khristu yemwe amene anakuyeretsani inu, ndipo anakuitanani inu, ndipo anayika kudzoza kumeneko pa inu.”

...*apo pakutsala palibe nsembe inanso kwa* tchimo, ya zimenezo.

Ndi zosakhululukidwa! Ndi kosatheka kuti iwo angabwere konse ku chidziwitso cha Choonadi.”

*Pakuti izo ziri zosatheka kwa iwo amene anali... atapangidwa kukhala ogawana nawo za* Mzimu Woyera,

Unagwera pa maudzu, onani, “Zinayamba kulowamo ndi Yesu, ndipo, ‘Ambuye, ine ndikupita mopyola,’” koma pamene inu munagunda Mawu, inu munatembenukira mmbuyo. “Munapangidwa kukhala ogawana nawo za Mzimu Woyera, ndipo ngakhale munalawa, kapena munawawona Mawu Iwoeni akuwonetseredwa.” Ndiyeno kutembenuka nkuchoka kwa Iwo, “Ndi zosatheka kwathunthu kuti iwo awawone konse Iwo kapena kubwera kwa Iwo.”

Ndizo PAKUTI LITERO LEMBA. Tsopano, inu... “Miyamba ndi dziko lapansi zidzachoka, koma Iwo sadzatero.” Inu mukuona izo? “Nzosatheka kwathunthu.” Baibulo linanena choncho, ndipo Mzimu ukuchitira umboni za izo.

<sup>196</sup> Zindikirani, ndiroleni ine ndikupatseni inu chitsanzo chaching’ono. Yang’anani pa anthu awo amene anatuluka pansu pa uneneri wa Mose, kutuluka mu bungwe limenelo, ndi kutuluka ku chirichonse, pansu pa uneneri, anawona ntchito

zazikulu ndi zodabwitsa, ndi zinthu monga choncho, ndi kubwera mpaka ku mzerewammalire wa kupita mkati.

Tsopano, Lee, apo pakubwera “dzina lako pa Bukhu.” Mwaona? Iwe walikonza ilo apo. Ndipo inu amene simuli pano, ndi kunja mu—pa kulumikiza, ndi Doctor Lee Vayle wakhala pano. Iye akuyika garamala bukhu ili la Mibadwo Isanu ndi iwiri ya Mpingo. Ndipo vuto linabwerapo, kapena funso, lokhudza “dzina lako kuchotsedwamo mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa.” Mukuona, izo zimanyumwitsa atumiki ambiri. Koma dikirani mpaka inu mudzapeze bukhulo, inu mudzamvetsa izo ngati inu muli nako Kuwala kulikonse mwa inu. Mukuona?

<sup>197</sup> Zindikirani, tsopano, inu mudzatembenuzira mutu wanu ndipo osayang’ana ngakhale pa Iwo ngati inu simukufuna kuwawona Iwo. Monga mayi anga anakakonda kunena, “Iwe sungakhoze kutenga magazi kuchokera mu mpiru, chifukwa mulibe magazi mwa iwo.”

<sup>198</sup> Zindikirani, Kuwala kuyenera kuti kubwere; si kuli mu mdima. Kuwala kumabwera ku mdima, ndipo mdima sumakuzindikira Iko ayi. Zindikirani tsopano iwo odzozedwawo mu tsiku ili.

Monga Mose anawatulutsa ana a Israeli aja; ndipo iwo anamvetsera ndipo anakhala osokonezeka onse ndi fuko lalikulu lija kumeneko. Tsopano, Israeli anali wazipembedzo zosakanikirana. Iye analibe dziko, analibe kwawo. Iye anali akupita kwawo.

Ife tiri opanda mpingo. Ife sitiri. . .Ife tiri—ife tiri kupita ku Mpingo, Mpingo wa Woyambakubadwa, Mpingo umene uli mu Ulemerero; osati mpingo umene uli pa dziko lapansi, wa munthu. Mpingo umene uli mu Ulemerero, iwo otulutsidwawo, okonzedweratu ku Moyo Wamuyaya, onani, akupita Kwawo.

Ndipo pamene iwo anabwera mpaka ku malo akuti awolokerepo, iwo anawakaikira Mawu, ndipo anabwerera mmbuyo. Zitachitika kuti Yoswa ndi Kalebu ndi iwo anapita kutsidya ndipo anabweretsa pobwerera mulu wa mphesa, kuti atsimitizire kwa iwo kuti dziko linalipo kumeneko, Mawu a lonjezo la Mulungu, “Ndi dziko labwino, mkaka ndi uchi.” Ndi kuzibweretsa izo pobwerera, ku mbali iyi, kuti akatsimitizire izo kwa iwo. Ndipo iwo analawa za izo, ndipo anati, “O, o, ife sitingakhoze kuchita izo, konse.” Nchiyani chinachitika? Iwo anafera mu chipululu. Iwo anakhala apo pomwe ndipo anadzipanga okha bungwe, ndipo anafa, mmodzi aliyense wa iwo.

Koma iwo amene anapita kutsidya nakabweretsa pobwerera, Yoswa ndi Kalebu; Mose atasinthidwa. Choyimira cha kuyembekezera kwa Mpingo; ndi chiwukitsiro cha Chipangano Chakale, Chipangano Chatsopano; ndi Thupi lokwatulidwa.

Mukuona zitatu pamenepo? Muyenera kusunga maatatu amenewo mu mzere, onani, kotero, mwa wokhulupirira ndi wosakhulupirira. Mwaona?

<sup>199</sup> Zindikirani momwe izo zinaliri “kwathunthu.” Kumbukirani, Mulungu sanakhulukire konse tchimo limenelo. [M’bale Branham akugogoda pa guwa kanai—Mkonzi.] Tsopano iwo akabweramo chotani mkati? Ngati ziri minga, kuyamba ndi kuyamba, ndi minga pa mapeto. Okonzedweratu okha adzaziwona Izo.

<sup>200</sup> Zindikirani mwacheru tsopano. Monga ngati mu masiku a Marteni Woyera, isanafike kumene Mibadwo ya Mdimba; mnyamata waumulungu. Ndi angati amene anayamba awerengapo zolemba za Marteni Woyera? Ambiri a inu mwatero. Iye tinapita kumusi kuti tikapeze zolemba za Marteni Woyera; wansembe anati, “Koma iye sanali wovomeredwa.” Zedi, iye sanali; osati ndi iwo, koma iye anali ndi Mulungu. Mzimu Woyera unatiuza ife kuti timuyike iye pamenepo pa m’badwo wa mpingo wachitatu uwo. Mwaona?

<sup>201</sup> Penyani chimene mnyamata waumulungu iye anali; woyitanidwa, wokonzedweratu. Makolo ake, achikunja. Abambo ake, msirikali. Iye anachita kutsatira mzere wawo, kuti akhale msirikali. Ndipo, pamene iye anatero, ndipo nthawizonse ankakhulupirira kuti kunali Mulungu kwina kwake; munthu wa ku nkhalango, ndipo amakhoza kumuwona Mulungu. Tsiku lina iye anadutsa mu mzinda, ndipo apo panali wopempha wachikulire atagona pamenepo, akufa, akupempha winawake. . . Iye anali kuzizidwa usiku umenewo. “O,” anati, “ndipatseniko ine chinachake kuti ndidzifunditse ine; ine ndifa usikuuno.”

<sup>202</sup> Palibe akanachita izo. Ndipo Marteni anakakhala ku mbali ina ndipo ankamuyang’ana iye kwa kanthawi. Palibe akanachita izo. Iye anali ndi chikhotho chimodzi chokha. Iye akanadziwumitsa, iyemwini, iye anali pa ntchito, ngati iye—iye akanamupatsa iye chikhotho chimenecho. Kotero iye anaganiza, “Tonse a ife tiri nawo mwayi wokhala moyo ngati ine nditi ndigawane naye iye.” Kotero iye anatenga chikhotho chake chomwe, ndipo anachigawa icho pawiri ndi lupanga lake, ndipo anamukutira wopempha wachikulireyo mu icho. Iye anakuta chikhotho chake chomwe mozunguliza.

Aliyense anati, “Penyani ndi mlonda wooneka-moseketsa bwanji. Penyani ndi msirikali wooneka-moseketsa bwanji, theka la chikhotho atalikuta mozunguliza pa iye!”

<sup>203</sup> Usiku wotsatira, pamene iye anali akupuma pa ntchito ndipo atagona mu kama wake, iye anadzutsidwa. Anayang’ana, atayima pamenepo mu chipinda, ndipo apo panayima Yesu Khristu atakutidwa mu chidutswa chakale cha chovala chimene iye anamuphimba nacho pa iye. Iye anadziwa nthawi yomweyo,

“Zimene inu muchita kwa aang’ono Anga, icho inu mwachitira kwa Ine, kwa wodzozedwa Wanga,” atagona pamenepo.

Iye anali wantchito wamkulu wa Mulungu. Mpingo unamuseka iye, unamuzunza iye, unamukankhira iye kunja, ndi china chirichonse, koma iye anali mneneri wa Mulungu. Zimene iye ankanena zinkafika pochitika. Alipo ambiri amene anakhulupirira mwa iye mu m’badwo umenewo, aponso.

<sup>204</sup> Ine ndikufuna kukusonyezani inu momwe Mdierekezi aliri wonyenga. Tsiku lina iye anali atakhala mowerengera mwake. Apo panabwera mngelo wamkulu, chibakuwa pa mutu wake, atavala nsapato zagolide, chilesi chitazungulira zovala zake cha golide, ndipo anati, “Marteni, kodi iwe ukundidziwa ine?” Iye anati, “Ine ndine Ambuye wako ndi Mpulumutsi. Ine ndine Mmodzi yemwe anakupulumutsa iwe. Ndipembedze ine, Marteni.” Koma mneneri ameneyo, podziwa kuti panali chinachake chachirendo pang’ono pamenepo, iye anapitirira kuyang’ana pa iye. Iye anati, “Marteni, ine ndine Mpulumutsi wako, Yesu Khristu. Ndipembedze ine! Kodi iwe sukundidziwa ine, Marteni?”

<sup>205</sup> Marteni anapitirira kuyang’ana pa iye, Lemba likuyenda kupyola mu malingaliro ake. Iye anati, “Satana, pita kutali ndi ine.” Iye anati, “Iwe uli ndi korona pa mutu wako. Ndipo Mawu a Mulungu amati ‘oyera Ake adzamuveka Iye korona’ pa mapeto a m’badwo.”

Kodi imeneyo siyikanakhala nyambo ya Achipentekoste? Penyani Mawu amenewo, m’bale. Ndi pamene iwo amalipira.

<sup>206</sup> Tsiku lina, mobwereza, mu monasitere, iwo anali ndi woyera wachikulire kumeneko, gulu la mamonki aang’ono. Uko kunali mmodzi wa iwo wokhala ngati wonyanyuka. Penyani ichi, apa pali labwino—fanizo labwino lero. Iye ankafuna kukhala chinachake chapamwamba pa ena onse a iwo. Iye ankafuna kumadziwonetsera yekha, ulamuliro, chachikulu chinachake, chinachake chabwinoko, zapamwamba zonse, inu mukudziwa, ndi chachikulu kwambiri chinachake. Iye amayenera kukhala wodula. Nthawizonse ankafuna abale enawo osati. . . Inu mukudziwa, iye ankayenera kumakhala wosiyana. Mukuona? Iye, ziribe kanthu chimene icho chinali, iye anali wamwano kwambiri. Iye anali nsangalabwi yokhayo pa doko. Panalibe wina aliyense akanakhoza kumukhudza iye. Tsopano penyani chimene chinachitika. Iye amayenera kukhala ndi chinachake chachikulu. Iye amayenera kufanizidwa ndi—magulu aakulu. Inu mukunditsatira ine? Mwaona? Koteri, iye anati, iye analosera. Iye anati, “Ambuye andipanga ine mneneri, nanenso. Ine ndine mneneri.”

Tsopano, panali mneneri mmodzi wodziwika mu dzikolo, ndipo ameneyo anali Marteni Woyera; iye anabadwa ali mneneri.

<sup>207</sup> Koma mwana uyu anati, mnyamata wamng'ono anati, monki wamng'ono pafupi wausinkhu wa zaka makumi awiri ndi zisanu. Iye anati, "Ambuye andipanga ine mneneri, ndipo ine nditsimikizira izo kwa inu." Anati, "Usikuuno Ambuye andipatsa ine mwinjiro wawukulu, wabwino, awuyika iwo pa ine, mwinjiro woyera, ndi kundikhazika pakati panu. Ndiye nonse a inu muzikabwera kwa ine, onani, ndipo inu muzidzatenga malangizo kuchokera kwa ine."

<sup>208</sup> Tsopano fanizirani izo lero, onani, "Ine ndikhala mutu wa bungwe. Ine ndizikusamalirani inu, ena nonse a inu mamonki."

Ndipo zedi mokwanira, "Usiku umenewo, zowala zinabwera mu nyumbamo," chotero zolemba za Marteni Woyera zikunena. Kawerengeni izo. Ndipo ndi zotsimikiziridwa. Ndi mbiriyakale. Ndipo zowala zinabweramo, ndipo onse enawo anapenya, ndipo apa pakubwera... Iye anali atavala mwinjiro woyera, atayima pakati pa iwo. Iye anati, "Mukuona zimene ine ndinakuuzani inu?" Koma ndizo zosiyana ndi Mawu.

<sup>209</sup> Ndipo pamene iye anapita wopempheretsa wachikulire wa pa koleji, iye anayenda chokwera-ndi-kutsika pang'ono pokha, anati, "Mwana, izo sizikumveka bwino." Iye anati, "Pali njira imodzi yokha." Ndi iyi apa! "Pali njira imodzi yokha yoti ife tidziwire. Izo zinkawoneka zauzimu." Mnyamata, Achipentekoste akanachigwira icho, muzu, chomiza, chingwe, mbeza, ndi chinthu chirichonse! Iye anati, "Chozizwitsacho chikhoza kuwoneka chabwino, koma icho sichikuwoneka chogwirizana kwa Mawu. Tsopano, ife tiri naye munthu woteroyo, mneneri wodzozedwa, dzina lake Marteni. Bwera, tipite uko pamaso pa iye."

Munthuyo anati, "Ayi, ayi! Marteni alibe kanthu kochita ndi ichi."

<sup>210</sup> Ndipo anati, "Iwe upita, mulimonse." Ndipo iwo anamugwira iye pa mkono, kuti amutengere iye pamaso pa Marteni, ndipo mwinjirowo unamuchokera iye.

<sup>211</sup> Onani, "Kunyenga Osankhidwa ngati izo zikanakhala zotheka." Mwaona, iwo akuwadziwa iwo. Yesu anati, "Nkhosa Zanga zimawadziwa Mawu Anga."

"O," inu mukuti, "zimamva liwu Langa."

Awo ndi Mawu Ake. "Munthu sadzakhala moyo ndi mkate wokha, koma ndi Mawu onse." Mwaona? Okonzedweratu amadziwa izi. "Mawu achirendo, kapena liwu lachirendo, iwo sadzalitsatira."

Ndiyo njira yake ndi anthu awo mmbuyo umo; iwo sakanatsatira. Iwo ankadziwa kuti Marteni anali kumeneko, mneneri wa m'badwo umenewo, wozindikiritsidwa ndi Mulungu kupyolera mu Mawu, ankawadziwa Mawu. Ndipo munthu ameneyo sakanayima pamaso pa Iwo.



<sup>212</sup> Iye ananenanso kuti, “Kumene kuli Nyama,” kapena Mawu, “kumeneko, mu nyengo, mphungu zidzasonkhana.” Tsopano ndiyo Mate-...Inu mukufuna kulemba zimenezo, uyo ndi Mateyu 24:28. Pang’ono pokha tisanafike, Mateyu 24:24; ndime zinai mmusi mwa apo, onani, ngati inu mukufuna kuzipeza izo. “Kumene kuli Nyama,” Manna ali, Mawu ali, “kumeneko mphungu zikakhala zitasonkhana.”

<sup>213</sup> Tsopano ine ndiyenera kufulumira. Ine ndinayang’ana pamwamba apo ndi kuyang’ana nthawi yanji...Ndi—ndi maminiti asanu ndi awiri kapena maminiti asanu ndi atatu itapitirira thwelofu koloko. Ine ndifulumira mwamsanga ndithu, kapena ife tikhoza kutsirizitsa izi usikuuno, aliyenseyo amene akufuna kuchita zimenezo. Mmawa uno kapena usikuuno? Nha? Ndi angati amene ayenera kuti apite kwawo lero ukatha msonkhano, tiyeni tiwone dzanja lanu, onani. O, mai, kulibwino kuti ndizipitiriza!

Ine ndikupepesa powasunga anthu awo pa mafoni awo kunjira uko monga choncho, koma ine ndifulumira. Ndi za mtengo wochulukira kuposa ndalama zanu. Ine ndikukhulupirira izo ziri, kwa ine, onani. Ndalama zanu zidzawonongeka. Izi sizidzatero; Ndi Mawu. Mwaona?

<sup>214</sup> “Kumene kuli Nyama, kumeneko mphungu zidzakhala zitasonkhana.” Kumene kuli Nyama, kumene ku—ku—kupha kuli, kumeneko mphungu zidzakhala zitasonkhana. Kumene kuli Nyama yatsopano, Mawu a nyengoyo, kumeneko mphungu zidzasonkhana.

Koma iyo itatha kuvunda, ndiye miimba idzasonkhanira kwa iyo. Eya. Mukuona chimene ine ndikutanthauza? Pamene kupha kwachitika, apa pamabwera mphungu; koma itatha iyo kukhala pamenepo, ndipo itavunda, ndiye apa pamabwera miimba. Mphungu sizimakhala nako kanthu kochita ndi iyo. Mwaona?

Yesu anati, “Kumene kuli Nyama,” kumene Manna anagwa, usiku umene Manna agwa mwatsopano, “kumeneko mphungu zisonkhanira kwa Iwo.” Ndiwo Manna a tsikulo. Mwaona? Zindikirani.

<sup>215</sup> Koma atatha iwo kuvunda, mphutsi zitafika mwa iwo, ndiye apa pakubwera miimba. Iwo sangakhoze kuyinunkhita iyo mpaka iyo itavunda. Palibe zodabwitsa Yesu anaima pamenepo ndipo anati, “Yerusalemu, iwe amene unagenda mneneri aliyense!” Zindikirani puronauni yaumwini iyo, onani, “Yerusalemu, Yerusalemu, ndi mowirikiza kangati ndikanati ine...” Anali ndani Uyo? “Ndi mowirikiza kangati Ine ndikanati ndikusonkhanitse iwe monga nkukhu ikanachitira anapiye ake, iwe amene unagenda mneneri aliyense amene Ine ndinamutumizapo konse kwa iwe,” mpingo waukulu uja, Yerusalemu.

216 Yerusalemu osati wa pano pa dziko lapansi, “koma ife ndife a Yerusalemu wochokera Kumwamba uko,” kumene Mawu amachokerako, kuchokera ku kukonzedweratu, onani. Osati Yerusalemu wakale amene amawonongeka; Yerusalemu Watsopano amene sangakhoze kuwonongeka. Osati Yerusalemu wakale, womangidwa ndi munthu; koma Yerusalemu Watsopano womangidwa ndi Mulungu, mwaona, Mawu kumeneko tsopano ali pa kuwonetseredwa. “Mu nyumba ya Atate Anga muli nyumba zazikulu zambiri. Ine ndipita ndipo ndikakukonzerani inu izo,” Mlengi akupanga njira za golide, ndi zina zotero. Ndiwo Umodzi umene suwonongeka.

217 “Yerusalemu, Yerusalemu, ndi kangati kamene Ine,” kuchokera ku chiyambi cha nthawi; osati Munthu wachitatu, wina wakenso, koma, “Ine ndikanati ndikufungatire iwe monga nkukhu imachitira anapiye ake, koma iwe suli kufuna. Koma tsopano ora lako lafika.” Mwaona?

“Kumene kuli Nyama, mphungu zidzasonkhana.” Koma nyamayo itavunda kale, ndiye miimba imasonkhana. Mwaona?

218 Zindikirani. Mose, iye sanawapatse konse ana a Mulungu. . . Mose anali mphungu, ndipo iye sanawapatse konse ana a Mulungu mikute ya Nowa. Iye anali ndi Mawu atsopano a Mulungu. “Ambuye Mulungu anakomana nane mu chipululu, ndipo anatimikizira Mawu Ake, ndipo anandituma ine kumusi kuno kuti ndidzakutulutseni inu.” Ndiye apo panabwera osanzira pozungulira, kudzasanzira icho. Mwaona? Koma iye anali nawo Mawu a oralo.

Zoona, Mulungu ananena kwa Abrahamu, mmodzi yemwe anali nalo lonjezo, “Mbewu yako idzakakhala mu dziko lachirendo, zaka mazana anai, koma Ine ndidzawachezera iwo ndi kuwatulutsamo iwo ndi dzanja lamphamvu.”

219 Mose anati, “Tsopano, Ambuye Mulungu adzayankhula kwa ine ndi kundisonyeza ine, ndipo wandiuza ine choti ndichite, ndipo Ine ndikuuzani inu.” Anati, “**INE NDINE**’ wandituma ine.”

“**INE NDINE!**” Osati “Ine ndinali, kapena ndidzakhala ndiri.” **INE NDINE,**” tensi yapakalipano, Mawu tsopano. Osati Mawu amene analipo, kapena Mawu amene ati adzabwere; Mawu amene alipo tsopano. Mwaona? Inu mwamvetsa zimenezo? “**INE NDINE!**” “**INE NDINE**” ali Mawu. “Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali ndi Mulungu.” Ndi kulondola uko? “**INE NDINE.**” “Mulungu anandituma ine monga mneneri Wake, kuti ndidzatsimikizire izi kuti ziri zoona. Ine ndine yankho kwa Mawu awa, chotero, pamene Iye anabwera panso pano ndi kuchita izi.”

220 Ndipo pamene iye anachita izo, Farao anati, “Chabwino, ife tiri nawo anyamata ochuluka mu gulu lathu amene akhoza kuchita zimenezo, nawonso,” osanzira.

Yesu anati, “Tsopano, izo zidzabwereza kachiwiri mu masiku otsiriza,” onani, kumadzitcha chinthu chomwecho. Penyani yemwe anabwera apo koyamba. Penyani yemwe anakhala mwa Mawu. Ndi zimenezotu. Ndi momwe izo zimadziwikira, kotero inu mukuona.

<sup>221</sup> Ife tikuzindikira, Mose sanawapatse konse iwo chimene chinali cha nthawi ya Nowa, “Ife timanga chombo tsopano, chifukwa ndiwo Mawu, inu mukudziwa. Nowa anamanga chombo tsiku lina.” Ayi, miimba inali kudya pa izo. Ayi, ayi. Ayi, ayi.

<sup>222</sup> Awa ndi Mawu olonjezedwa. Zindikirani, chifukwa cha uthenga wake umene iye anali nawo wochokera kwa Mulungu, iye anali nawo Mawu enieni okonzedweratu a Mulungu a ora limenelo. [M’bale Branham akugogoda pa guwa kawiri—Mkonzi.]

Ngakhalenso Yesu sanawapatse iwo mikute ya Mose. Mose anali nawo Mawu a ora limenelo, koma Mose anali mneneri. Pano pali Mulungu Iyemwini, onani, Iye sanawapatse iwo ya Mose—mikute ya Mose.

Koma tangoyang’anani pa miimba pamenepo mu bungwe limenelo, anali kuzimeza izo. “Ife tikudziwa! Ife tiri naye Mose! Ife sitisowa kuti tikhale ndi Iwe.”

<sup>223</sup> Iye anati, “Ngati inu mukanamudziwa Mose, inu mukanandidziwa Ine, chifukwa Mose ankayankhula za Ine.” O, mai! Mukuona?

“Kumene Nyama ili, mphungu zidzasonkhanako.” Mphungu! Chophedwa mwatsopano cha Mawu, Mawu amene aleredwa ndi kunenepetsedwa, ndipo apangidwa kuti awonetseredwe ndi kuperekedwa ngati Chakudya kwa ana.

Tsopano, nyama yakale imene yakhala pamenepo kwa mazana a zaka, pamenepo iyo idzakhala.

Mofanana tsopano! Lutera anali nawo uthenga wa kulapa; koma inu gulu la akhungubwe Achilutera! Abaptisti anali nawo uthenga; koma, inu akhungubwe Achibaptisti! Mwaona? Achipentekoste anali nawo uthenga; tikubwera kunyumba tsopano, akhungubwe Achipentekoste!

“Koma kumene Nyama ili, kumeneko mphungu zidzasonkhana.”

<sup>224</sup> Kumbukirani, iwe sukanakhoza kuwadyetsa Chilutera, mmbuyo mu masiku amenewo (inu mukhoza tsopano), chivundi cha Katolika. Ayi, bwana. Iye anali ndi nyama yatsopano. Uwo unali m’badwo wa mpingo umenewo.

Inu simukanakhoza kuwadyetsa Amethodisti, uthenga wa Chilutera. O, ayi, iye sanafune chivundi chimenecho. Ndi zowola. Mwaona, Moyo unali utachokamo ndipo utapita ku china

chakenso. Ilo ndi phesi lakale limene linafa, kumbuyo uko. Moyo ukusunthira patsogolo.

Simukanati ngakhale inu kuti mumudyetse Mkwatibwi wa Yesu Khristu Chipentekoste. Ayi, indedi! Mabungwe ofufuma ndi-mphutsi; opanda chochita! Ayi, ayi!

Pakuti lonjezo liri, “Ndipo tsiku lalikulu ndi lowopsya ilo lisanafike, Ine ndidzakutumizirani inu Eliya mneneri. Iye adzabwezeretsa mitima ya ana kubwerera ku Chikhulupiriro cha atate kachiwiri.” “Malonjezo onse awa anali atapangidwa mu Baibulo, Ine ndidzachita izo, ndipo kumeneko mphungu zidzasonkhana.” “Onse amene Atate andipatsa Ine adzadzwa kwa Ine.” Mwaona?

<sup>225</sup> Yesu sanalawe konse zimenezo. Koma pamene Yesu anabwera, Iye anapeza khamu ilo la miimba, “Ife tiri naye Mose ndi lamulo.” Mwaona? Chabwino, uko kunali kudya kwabwino mmbuyo kutaliko pamene iyo inali itaphedwa ndi kupatsidwa kwa iwo. Mwaona, izo zinali zabwino pamenepo.

Koma ichi ndi chimene chinaneredwatu kwa Mose, iyemwini, amene anapha nsembeyo, anati, “Ambuye Mulungu wanu adzautsa pakati panu, wa abale anu omwe, Mneneri. Izo zidzafika pochitika, kuti aliyense amene sadzakangamira kwa Mneneri ameneyo ndi zimene Iye anena, adzadulidwa kumuchotsa pakati pa anthu.” Ndipo izo zinali.

<sup>226</sup> Yang’anani momwe pafupi mauneneri mazana asanu ndi limodzi osiyana anakwaniritsidwira pomwepo, a Chipangano Chakale, kwa Yesu Khristu. “Iwo anapoyza manja Anga ndi mapazi Anga.” Zokhudza, ine ndayiwala angati amene anakwaniritsidwa mu maora asanu ndi awiri otsiriza kapena maora asanu ndi atatu a Moyo Wake, aneneri onse awo ananena, mwangwiro.

<sup>227</sup> Ngati ine nditalosera lero kuti chinthu chinachake chikanachitika mu chaka kuchokera pano, mwinamwake ine ndiri ndi—ine ndiri nawo mwayi wa magawo makumi awiri pa zana kuti icho chichitike, kaya ndi cholondola kapena cholakwika. Ndipo ngati ine nditaneneratu kuti izo zikanadzachitika, ndipo ndisananene kuti ndi liti, ine ndiri nawo magawo aang’ono pa zana. Ngati ine ndikananeneratu pamene izo zikanati zidzachitike, zikundipatsa ine malire aang’ono. Ngati ine ndikananeneratu malo amene izo ziti zidzachitikire, izo zikuzipatsabe izo malire apang’ono. Ngati ine nditaneneratu...yemwe izo zikanati zidzakhalepo, ndiye ine ndiri nawobe malire apafupi zana limodzi pa zikwi za malire kuti izo zidzachitike konse, ngati siziri zoon.

Ndipo Mawu aliwonse, aleluya, amene analembedwa za Mesiya ameneyo, anakwaniritsidwa mpaka ku chilemba. Ngakhale pamene tsiku limodzi, akuwerenga Malemba, Iye anayima pakati pomwe pa chiganizo, ndipo anati,

“Mzimu wa Mulungu uli pa Ine kuti ndilalikire Uthenga, ndi kuwombola. . .” Ndipo anayima pamenepo pomwe mkati mwa chiganizo, chifukwa zina zonse za izo ziri pa Kudza Kwake kwachiwiri. Amen! “Miyamba ndi dziko lapansi zidzapita; Mawu Anga sadzatero.” Mukuona?

<sup>228</sup> Iye anali Mawu pamenepo, amene anali kuwadyetsa iwo pamenepo. Mose anawauza iwo Choonadi; koma, inu mukuona, iwo nthawizonse amapanga chipembedzo kuchokera mwa icho, kuti miimba i. . .

Pali ena a Iwo amene atsalira mphungu zitatha kudya ndipo zitapita kwawo. Ndiye iwo akuyembekezera kuti awone chinthu chinachakenso. “Mawu,” iwo akuti, “pano Iwo akuyenera kuti abwere. Ife tinali ndi mphalapala dzulo; ife tikhala ndi nkhosa mawa.” Mukuona zimene ine ndikutanthauza? “Kuli nyama ya mphalapala yaikulu kumusi uko, ili tong’o, koma ife tiri ndi nkhosa imene ikubwera lero. Ili kuti iyo?” Mukuona zimene ine ndikutanthauza? Chakudya cha Angelo! Anthu amene amadya manna tsiku limodzi, ngati iwo akanayesa kuwasungira iwo mpaka tsiku lotsatira, iwo anali kuvunda. Kodi inu simukuona zoyimira zonse, zangwirow bwanji? Nzofanana tsopano!

<sup>229</sup> Zindikirani, miimba ya tsiku la Yesu inali nayonso kutulutsa ziwanda; iwo odzozedwawo pa nyama yakale. Ndi kulondola uko? Iwo anali kutulutsa ziwanda. Yesu ananena choncho.

Ndipo kumbukirani, iwo anali nawo aneneri mu masiku amenewo, Kayafa, wansembe wamkulu, ananenera. Ndi angati akudziwa zimenezo? Kayafa ananenera. Zindikirani malo a udzu mmunda; iwo umatsiriridwa ndi kudzoza komweko. Nchifukwa chiyani Baibulo linati iye ananenera? “Chifukwa iye anali wansembe wamkulu chaka chimenecho.” Khwangwala wovunda, udzu ndi nthula, zikukhala pakati pa Tirigu; koma Mzimu unali pa izo, Mzimu Woyera weniweni wa Mulungu. Mzimu Woyera wa Mulungu unali pa iye, kuti azilalikira, kunenera, ndi kulosera kuti izo zifika pochitika; ndipo anamukana ndipo anamupachika Mawu yemwe wotsimikizidwira wa oralo.

O, chifundo, m’bale! Ndi motalika bwanji ife titi tikhale tikunena zinthu izi, onani, mochuluka bwanji kupyola mu Lemba? Ine ndifulumira. Ine ndiri ndi pafupi masamba khumi pano, a Malemba, momwe akutsimikizira zinthu zonse. “Dzuwa pa olunga ndi osalungama, mofanana.”

<sup>230</sup> Yesu anati, kuti titsimikizire izi. “Ngati Ine ndikutulutsa ziwanda ndi chala cha Mulungu, ndi ndani yemwe ana anu akutulutsa izo naye?” Tsopano, iwo anali akutulutsa ziwanda. Iwo anali akunenera. Ndi kulondola uko? Koma sanamuzindikire Iye kukhala Mawu a oralo, (chifukwa chiyani?) chifukwa Iye sanali woyanjana ndi iwo.

Tsopano tengani Mateyu 24:24, “A Khristu abodza,” iwo odzozedwawo, “adzauka, ndipo uko kudzakhala aneneri abodza akunenera izo,” onani, “ndipo adzanyenga Osankhidwa omwe ngati izo zikanakhala zotheka.” Inu mwazimvetsa izo tsopano?

<sup>231</sup> Zindikirani ana. “N’ndani amachita naye ana . . . Ngati ine ndikutulutsa ziwanda ndi Mawu a Mulungu,” chimene, Iye anali Mawu a Mulungu, “n’ndani amene ana anu achipembedzo amatulutsa izo naye?” Tsopano, ndipo Mulungu yekha akhoza kutulutsa chiwanda, ife tikudziwa zimenezo, Mulungu yekha. Pakuti, munthu wamphamvu ayenera kukhala wamphamvu kuposa yemwe ali mu nyumba yake. Iwo anali nazo mphamvu zoti achitire izo.

Inu mukudziwa, mu Chivumbulutso pamenepo, anati akanati . . .kuti wotsutsakhristu uyo awuke mu masiku otsiriza, “Anachita zizindikiro ndi zodabwitsa, zimene zinanyenga ngakhale iwo amene ankakhala pa nkhope ya dziko lapansi, ndipo ananyenga mmodzi aliyense wa iwo, Akhristu ndi onse, amene maina awo sanali atalembedwa mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa,” yankho kwa Mateyu 24:24, “amene maina awo anali asanalembedwe mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa kuchokera pa maziko adziko.”

Moyo umenewo umene unali mu muzu wa—wa mtengo weniweni wa lalanje uwo, umene unakwera mmwamba kupyolera mu zipatso za citrus zonse izo ndi china chirichonse, ndipo unapitirirabe ndipo umakayika chipatso pamwamba pa mtengo, pamwamba pa zomezanitsa zonse zachipembedzo ndi nthambi. Inu mwamvetsa izo? Ine ndifulumira. Munthu wamphamvu . . .

<sup>232</sup> Kumbukirani Davide tsopano, iye anali woonamtima, wodzipereka, akuyesa kumuchitira Mulungu ntchito, ndipo sanali wodzozedwera kuti ayichite iyo.

“Awo,” iwo odzozedwawo; koma Yesu anati, “Iwo akuphunzitsa kukhala Chiphunzitsa kutanthauzira (kwa Malemba) kwa munthu,” onani, osati Mawu a Mulungu, osati Mawu otsimikiziridwa Ake; kuphunzitsa Khristu wa mbiriyakale, onani, chinachake chimene chinalipo.

Ndipo Baibulo linati, “Iye ali.” “INE NDINE,” osati “Ine ndinali kapena ndidzakhala.” “Ine ndine pakali pano.” Iye ali Mawu amenewo amene amakhala moyo kupyolera pano.

Iye anali, pa chiyambi, Iye anali mu . . .Iye anali mu—masamba; Iye anali mu ngayaye; Iye anali mu mankhusu; koma tsopano Iye ali mu Njere.

<sup>233</sup> Tsopano, inu mupite mmbuyo ndi kukayesa kukhala moyo kachiwiri? Bwanji ngati Moyo umenewo utabwerera pansu, inu mukuganiza kuti iwo (wotsala) moyowo ukanati uyankhule konse, ukanabwereranso ku mankhusu akalewo atauma, kubwereranso konse ndi kukakhala moyo mwa iwo

kachiwiri? Iwo sukanatero konse. “Pakuti izo ndi zosatheka kwa iwo amene anaunikiridwapo kamodzi,” ndipo sanasunthire patsogolo ndi Mawu pamene ankafika pokwaniritsika, “iwo ali akufa, apita; ndipo minga ndi nthula zimene ziri pafupi kuti zikanidwe, zimene mapeto ake ali oti ziwotchedwe.” Ndi kulondola uko?

Tsopano kufulumira basi mofulumira monga ine ndingathere.

<sup>234</sup> Zindikirani Lemba tsopano. Kuphunzitsa Mulungu wambiriyakale, onani, monga momwe iwo akuyesera kukhala mu zachipiti, monga, “Chabwino, Wesile ananena *zakuti-ndi-zakuti*. Kapena, *Wakuti-ndi-wakuti* ananena *zakuti-ndi-zakuti*.” Inu mukukana Mawu olonjezedwa a tsikuli, Manna amene azindikiritsidwa momveka a tsikuli. Iwo akuyesa kuyika vinyo wawo wakale wa Chilutera, Baptisti, Wachipentekoste mu mabotolo atsopano. Izo sizikugwira ntchito. Ndipo Vinyo wathu watsopano mu mabotolo akale awo, sizigwira ntchito. Ngati iwo ayesa kuyika Vinyo watsopano uyu mu chipembedzo, kupusa kwawo kukuchita kuwonetseredwa. Iwo sangakhoze kuchita izo. Iye amawaphulitsa iwo.

<sup>235</sup> “Tsopano, m’bale, ine ndawawona Mawu a Mulungu, mwangwiro ndi Mawu!”

“Tsopano, penyani apa, Dotolo, ngati...Ife—ife sitingakhoze kukhala nawo Awo.” Ned, ine ndikuganiza inu munali nazo zina za izo posachedwapa. “Ife, ife basi sitingakhoze basi kukhala nawo Awo apa tsopano. Ine—ine kulibwino kuti inu mwina musingopitirira patsogolo.” Inu mukudziwa. Onani, izo sizigwira ntchito. Iye amawaphulitsa.

“Iwe sumaika chigamba chatsopano mu chovala chakale, chifukwa iwe upangitsa icho chonse kung’ambika.” Mwaona? Kodi Yesu sananene zimenezo? Inu simungakhoze kuyika Vinyo watsopano mu mabotolo akale. Iye amawaphulitsa iwo. Vinyo watsopano ali ndi Moyo mwa iye. Chabwino.

<sup>236</sup> Zindikirani pano chinachake, mwamsanga kwenikweni tsopano, pamene ife tikutsirizitsa...kuyankhula kwathu. Zindikirani Chivumbulutso 16:13 mpaka 14, ngati inu mukufuna kuzilemba zimenezo. Ine sindikhala nayo nthawi mwinamwake kuti ndipite ku izo. Ine ndikufuna inu kuti mukhale otsimikizira ndi kuwona izo. Tsopano zindikirani, uko ndi kuwomba pakati pa Mbale ya Chisanu ndi chimodzi ndi ya Chisanu ndi chiwiri.

<sup>237</sup> Tsopano ife ti—ife titseka mu miniti chabe, ngati inu mungakhoze chabe kupirira maminiti pang’ono motalikira. Tikutseka tsopano.

<sup>238</sup> Zindikirani Chivumbulutso 16:13 mpaka 14, pakati pa Mbale ya Chisanu ndi chimodzi ndi ya Chisanu ndi chiwiri, “Mizimu itatu yosayera yonga achule” (kodi inu munali mutazindikira zimenezo?) “inatuluka kuchokera

mkamwa mwa winawake.” Tsopano zindikirani, mwamsanga. Kodi inu mwakonzeka? Nenani, “Ameni.” [Osonkhana, “Ameni.”—Mkonzi.] Utatu wa mizimu!

<sup>239</sup> Tsopano m’bale wachipembedzo, khazikika mwabata miniti chabe. Musati muwuke ndi kuyenda kutuluka mchipinda, kumbuyo kunja uko kwa pa wailesi iyi, kulumikizana pa telefoni. Musati muzimitse tepi rekoda yanu. Khazikikani mwabata miniti chabe, ndipo mvetserani. Muli obadwa wa Mulungu, inu mutero.

<sup>240</sup> Utatu wa achule! Chule ndi nyama imene nthawizonse imayang’ana chammbuyo. Iye samayang’ana konse kumene iye akupita; iye amayang’ana kumene iye akuchokera. Mwaona? Kodi inu simukuwona? Kodi utatu unabadwira kuti? Kumbukirani, “mizimu itatu yosayera,” mizimu yapayokha. Kodi inu mukuzimva izo? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.]

<sup>241</sup> Zindikirani, iwo amayang’ana mmbuyo ku Bungwe la Nicaea kumene chiphunzitso cha utatu chinabadwirako, osati mu Baibulo. Mulibe chinthu choterocho. Iwo amayang’ana mmbuyo ku Bungwe la Nicaea ku Nicaea, Roma, kumene utatu unabadwirako.

Zindikirani kumene izo zinachokera. Zindikirani. Ndipo utatu wa achule unatuluka kuchokera mu utatu wakale, kupereka kubadwa kwa utatu watsopano, mayi wawo. Kodi iyo inabwera kuchokera kuti? Utatu, “chinjoka,” onani, “chirombo,” ndi “mneneri wabodza.” Utatu, watsopano. Pakuti ndi liti limene achule awa anatuluka? Ndi liti iwo anatero? Zindikirani, iwo anali alipo nthawi yonse, koma izo sizinali zitawonetseredwa mpaka pakati pa M’bale Yachisanu ndi chimodzi ndi Yachisanu ndi chiwiri, Zisindikizo zisanatsegulidwe kumene kuti ziulule izo.

“Pakuti mu Uthenga wa mngelo wachisanu ndi chiwiri, zinsinsi za Mulungu zidzadziwika,” zinthu zonse za utatu izi, ndi maubatizo abodza, ndipo chirichonse chinali choti chichite kuwonetseredwa. Mulungu tithandizeni ife kuti tiwone chimene chiri Choonadi! Ndipo osati aganize kuti ndi winawake akuyesa kunena chinachake kwa . . .

<sup>242</sup> Ine ndikumverera mzimu uwo ukuyipidwa ndi Chimenecho, inu mukuona. Ine sindiri kuyankhula za ndekha, m’bale. Ine ndikuyankhula za Mngelo wa Ambuye yemwe ali mu msasa. Ndizo kulondola chimodzimidzi.

<sup>243</sup> Zindikirani, utatu! “Chinjoka,” ndi angati akudziwa chimene chinjoka chinali? Icho chinali Roma. “Ndipo chinjoka chinayima pamaso pa mkazi kuti chimulikhwire mwana wake mwamsanga pamene iye anali atabadwa.” Ndiko kulondola? Kodi “chirombo” chimatanthauza chiyani mu Baibulo?



Mphamvu. Chabwino. “Mneneri wabodza, mneneri wabodza,” wabodza, iye wodzozedwayo. Mwaona?

<sup>244</sup> Zinayambira kuti? Uyu ndi “mneneri wabodza,” mmodzi. “Mneneri wabodza,” papa woyamba; ndipo kuchokera pamenepo panatuluka “hu—hule, ndipo mayi wa timahule,” chinthu chonsecho.

Utatu wabodza unali kuwuka; osati mu masiku oyambirira, sizikanati ziwonetseredwe mu masiku oyambirira, izo anapitirira mtsogolo napyola ndi izo. Koma pamene Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri zabwera, ndi kutsegula zinsinsi izo ndi kuziulula izo; ndi pamene “achule, mizimu itatu yonga achule, inatuluka kuti idziwonetsere yokha,” chiphunzitso cha utatu kutsutsana ndi Choonadi. Mwaona? Nha!

Mukuona kumene izo zinachokera? Mukuona kumene izo zikubwererako? Bungwe la Ecumenical. Iwo onse ndi abale, chonchobe; mizimu yofanana, chinthu chofanana.

Ndipo penyani. Zonyenga kwambiri, zikuchita zozizwitsa! Ndipo awa ndi adierekezi amene amapita kwa milungu yonse ya dziko lapansi, akuchita zozizwitsa, kuti akawanyenge iwo mu tsiku lotsiriza, ndipo adzapambana mu kuchita izo. Kodi Mulungu ananena chiyani zokhudza mzimu woyipa umenewo?

Unati, “Ine ndipita pansu ndi kukalowa mkamwa mwa aneneri amenewo ndi kuwapangitsa iwo kuti anenere bodza, kuti amupangitse Ahabu kuti abwere kunjja uko kuti akawonongedwe.”

<sup>245</sup> Mulungu anati, “Pita. Iwe ukapambana. Iwe ukawafikitsa iwo pokhulupirira izo. Iwo sali pa Mawu amenewo, kuyamba ndi kuyamba,” Mwaona? “Pita, pakuti iwe ukamakamiza iye. Iwe ukhala mmodzi yemwe ati akachite izo, pamene iwe ukalowa mwa aneneri abodza awo, chifukwa iye akudalira kumene mwa iwo. Ndipo iye sakudziwa kanthu za Mawu, sadzayesanso iye ngakhale kuphunzira zokhudza Iwo. Iye sangakhoze kuchita izo, chifukwa iye ndi nthula, kuyamba ndi kuyamba.” Mwaona? Mwaona? “Iwe ukapambana.”

<sup>246</sup> Penyani apa pa achule abodza awa, akuyang’ana mmbuyo, “Chifukwa chiyani, inu mukudziwa zimene iwo ananena kumbuyo uko ku Nicaea?”

Ine sindikusamala zimene iwo ananena, uko ku Nicaea. Ine ndikunena zimene iwo ananena kuno ku Mpandowachifumu wa Mulungu; chimene chikanati chikhale, osati chimene chinali; chimene chiti chidzakhale, pakuti Iye ali “INE NDINE.” Mwaona?

“Abodza.” Penyani pa izo. Nha! Zindikirani kumene iwo anachokera.

<sup>247</sup> Tsopano mvetserani mwatcheru. Ife tikuwona mwapoyera, Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri zitatsegulidwa kale, ndizo zoti

ziulule chinsinsi chimenecho. Utatu umenewo ndi chiyani? Mwaona? Ndi pati pamene izo zinayamba zatchedwa utatu? Mukuona? Ndi pati mu Baibulo pamene Ilo linayankhula nkomwe mawu a utatu? Ndi pati pamene pakanakhoza kukhala Amulungu atatu, pamene ife tikupembedza Amulungu atatu nkusakhala achikunja?

Iwo angakhoze bwanji kukhala olekana, pamene Iye anati, “Ine ndi Atate Anga ndife Mmodzi?” “Kupatula inu mutakhulupirira kuti Ine ndine Iye, inu mudzafa mu tchimo lanu, mwaona, kusakhulupirira kwanu.” Tchimo ndi kusakhulupirira. “Inu mudzawonongekera mu kusakhulupirira kwanu.”

O, inu mukuti ndine Yani, mukuti Ine ndinachokera kuti,  
O, kodi inu mukuwadziwa Atate Anga, kapena kodi inu mungakhoze kutchula Dzina Lawo?  
INE NDINE Duwa la ku Sharoni, Nyenyezi Yowala ya Mmawa.

Kodi inu mungakhoze kundiiza ine Yemwe Iye ali?

INE NDINE yemwe anayankhula ndi Mose mu chisamba choyaka Moto,  
INE NDINE Mulungu wa Abrahamu, Nyenyezi Yowala ya Mmawa.  
INE NDINE Duwa la ku Sharoni, o, inu mukuti Ine ndinachokera kuti;  
O, kodi inu mukuwadziwa Atate Anga, kapena mungakhoze kutchula Dzina Lawo? (Ameni!)  
INE NDINE Alpha, Omega, Chiyambi kuchokera ku Mapeto;  
INE NDINE chirengedwe chonse, ndipo Yesu ndilo Dzina Lake.

<sup>248</sup> Ndiko kulondola. Osati utatu! Ayi, bwana. Ndicho chinthu chabodza.

Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri, zikutsegula zinsinsi zimenezo zimene “ziyenera kuti zitsirizidwe,” kuzisonyeza izo. Chisindikizo kutsegulidwa; kuyalutsa, kuziwonetsa, kupangitsa kumveka Zoonadi zobisika zimene Zisindikiro zinali zitabisa zaka zonse izi, kupyola mu mipingo yonse iyo ndi zipembedzo.

“Hule lalikulu,” la Chivumbulutso seveni-...Iye anali ndani? Koma iye ndi “MAYI WA TIMAHULE,” nayenso. Mwaona?

<sup>249</sup> “Tsopano, inu munawatcha iwo ‘miimba,’” inu mukutero, “M’bale Branham.” Ndiko kulondola.

Koma, kumbukirani, muimba ndi mbalame. Iyo ndi yodzozedwa kuti iziuluka, nayenso. “Mizimu iwiriyo idzakhala yofanana kwambiri ikanati idzanyenge Osankhidwa.” Muimba

ndi wamkulu monga—monga mphungu. Iye akhoza kuwuluka monga mphungu iyo; ndipo iye ndi wodzozedwa kuti aziuluka, kapena kulalikirira, kapena kunenera, zindikirani, mofanana monga mphungu. Koma iye sangakhoze kuyitsatira mphungu mu utali. Ayi, ayi. Ngati iye ayesera kuti ayitsatire mphungu, kupusa kwake kudzachita kuwonetseredwa. Inde, bwana. Iye sangakhoze kuitsatira mphungu.

O, iye akhoza kunena, “Ine ndimakhulupirira mwa Yesu Khristu kukhala Mwana wa Mulungu. Ine ndikukhulupirira Mulungu Atate, Wamphamvuzonse, Mlengi wa miyamba ndi dziko lapansi; Yesu Khristu Mwana Wake, ndi zina zotero.” O, zedi, iwo akhoza kuchita zimenezo. Koma bwanji za Iye kukhala yemweyo dzulo, lero, ndi nthawizonse? Mwaona?

<sup>250</sup> Mphungu ndi mbalame yomangidwa-mwapadera. Palibe kanthu konga iyo, pa dziko lapansi. Mwaona? Iye—iye... Ngati khungubwe ayesa kumutsaita iye, kapena mbalame ina iliyonse, iyo ikhoza kuphwasuka. Kupusa kwake kudzachita kuwonetseredwa, zedi mokwanira. Iye akanaphulika pamene iye akanayesa kuyika Vinyo watsopano mu botolo lakale. Onani, iye akanaphulika, Iye akanaphwasuka. Iye sanapangidwe, iye sali...Thupi lake silinaikidwe palimodzi ndi chimango choti chizimugwira iye mmwamba umo. Pamene iye afika mu milengalenga yaikulu iyo mmwamba kutali, ngati iye sanali atapangidwa, wodzozedwa, kukonzedweratu, kudbadwa ali mphungu, iye akanaphulika mu zidutswa. Mwaona? Nthenga zikanathothoka kuchoka mu mapiko ake, ndipo iye akanagwera pa dziko lapansi. Zedi. Iye sangakhoze kuitsatira mphungu, mu utali. Ngati iye ayesa kutero, kupusa kwache kuchita kuwonetseredwa. Ndiko kulondola. Iwe sungakhoze.

<sup>251</sup> Chifukwa chiyani? Iye sangakhoze kupenya monga mphungu. Ndi ubwino wANJI zikanachita kuti alumphire mmwamba kwenikweni, ndi osamakhoza kupenya pamene iwe uli pamene iwe uli mmwamba umo? Ndipo ngati iye atati ayesere, ngakhale kuyesa kuti asanzire mphungu iyi, mu utali, iye amakhala wakhungu kwambiri iye samadziwa chimene iye amachitira khama. Ndiko kulondola. Iye akukuwa ndi kufuula, ndi kumapitiriza; koma ingoyankhulani Mawu kwa iye, mnyamata, pamenepo kupusa kwake kumachita kudziwika.

Kuyankhula kwa iye zokhudza ubatizo mu Dzina la Yesu Khristu, kapena, Iye kukhala yemweyo dzulo, lero, ndi zonse, zonse—zonse monga chomwecho, ndi kumuuza iye. “Bwanji, o, tsopano dikirani miniti chabe!” Mwaona? O, eya, pamenepo nthenga zake zikuthothoka. Mwaona, iye walumphya yense, ndi kunenera, ndi kutulutsa ziwanda, ndi kuyankhula mmalirime, ndi kufuula, ndi kumapitiriza, kuthamanga chokwera-ndi-chotsika pansi. Koma asayese kutsatira mmwamba Umo; bwanji, iye zedi adzachita kudziwika.

Komabe, iye ndi wokhazikitsidwa. Iye ndi wodzozedwa. Iye akhoza kuuluka. Iye akhoza kudziyandamitsa iyeyekha, kufika mmwamba umo, koma osati. . . patali chomwecho. Mwaona, iye akhoza kudya zovunda, koma iye sangakhoze kudya Nyama yatsopano imene ikuchokera ku Mpandowachifumu.

Iye ndi wakhungu. Iye ndi wochita khama, koma iye sakudziwa chimene iye akuchitira khama. Mukuona, Mzimu womwewo umene unagwera pa iye, monga mvula, kuti umupange iye tirigu; iye sali tirigu kuyamba ndi kuyamba. Iye amaphulika. “O, ine sindingakhoze kupitira zina. . . O, ayi, bwana! Ine ndikudziwa Doctor Yonasi anati. . .” Chabwino, zipitani patsogolo. Mwaona? Pitani patsogolo, ngati inu mukufuna kutero.

<sup>252</sup> Ayi, zindikirani, iye sanabadwe, kapena kumangidwa, kapena kukonzedweratu, kuti akakhale mbalame ya mtundu umenewo. Iye akhoza. . . Iye ali. . . likhoza kukhala ndimu likumera pa mtengo wa lalanje, koma ilo silinabwere kuchokera ku mizu. Ilo ndi chinachake chimene chachita kuwonjezedwapo. Ndipo pamene iwo anafika pamwamba kwambiri mu zipembedzo zawo mwakuti iwo sangakhoze kupenya Mawu okonzedweratu a Mulungu akutsimikiziridwa, ndiye kupusa kwawo kumachita kudziwika. “O, chinthu chimenecho, Mlangali pamwamba pa mutu, ndi zonse, o, Ndizo zamkhutu.” Mwaona? Achita kudziwika.

<sup>253</sup> Iye sanapangidwe kuti aziyang’ana patali chotero. Iye angakhoze kokha kupenya kutali kwa monga momwe magalasi achipembedzo angati amulolere iye kuti apenye. Koma, zikatha zimenezo, iye ndi wakhungu monga mleme. Ndi pamenepo kupusa kwake kumachita kudziwika. Mwaona? Ndi pamene mphungu yona imakhala pansu kuti izidya. Inde, bwana. Ndi pamene mphungu zoonza, zosankhidwa, zimapenya chimene iye ali. Pamene iye sangakhoze kuwatenga Mawu amenewo, iwo amadziwa pomwepo kuti iye ndi muimba wa chipembedzo.

<sup>254</sup> Bwanji, nchifukwa chiyani iye sangakhoze kuuluka? Chifukwa, taonani pa zimene iye wakhala akudya. Iye wakhala akudya pa mtambo wovunda wa zachipembedzo. Zimenezo siziti—izo sizipangitsa thupi lake kukhala lauzimu, sizimuyika iye mu kukwanira kwauzimu, mwakuyankhula kwina, kuti zimunyamulire iye mmwamba pamwamba pa kusiyana kwa zazipembedzo. Mwaona? Onani, iye wangodyetsedwa zinthu zovunda; thupi lake liri lopangidwa kuchokera kwa zimenezo. Iye sangakhoze kupita kumeneko kumene Nyama yatsopano iyo imamunyamula mphungu ameneyo. Iye sangakhoze basi kuchita zimenezo. Mwaona?

<sup>255</sup> Zimenezo zikukwaniritsa Mateyu 24:24. Iye akuuluka, kulumphira mmwamba mu mlengalenga, kutambasula mapiko ake, koma iye basi sangakhoze kufika mmwamba mokwanira.

Mwaona? Ndiko kulondola. Onani, iye sangakhoze kupita, iye sangakhoze kufikira mmwamba mokwanira kuti akatenge Manna atsopano amenewo. Iye akhoza kudya manna akale amene ali pansi pano pa nthaka, akalulu akale akufa amene anagundidwa sabata lapitalo, ndi mwezi wapitawo, kapena zaka makumi anai zapitazo, chivundi. Iye akhoza kudya zimenezo, ndi kugalika pa izo, ndi kuyimba ndi kufuula, ndi kumapitiriza, kulumphama mmwamba ndi kuuluka monga mphungu ina. Iye ndi wodzozedwa, monga mbalame yina.

Ndipo iye ali choyimira cha mphungu, muimba ali. Ife tikudziwa zimenezo. Iye zedi ali, koma iye sangakhoze kutsatira mphungu yeniyeni iyo. Mwaona? Iye sangakhoze basi kuchita zimenezo. Ayi, bwana. Thupi lake silinapangidwe; iye wakhala akudya pa zovunda zosiyana, onani, ndipo izo sizidzakhala ziri... iyo siyikhala—iyo siyikhala Nyama yatsopano, Manna atsopano. Ichu chikhala chinachake chimene Lutera ananena, Wesile ananena, kapena Dokotala *Wakuti-ndi-wakuti* ananena. Izo sizikhala pa zimene Yesu ananena kwa ora ili.

<sup>256</sup> Tiyeni tipite tsopano, potseka. Iwo odzozedwawo, “A Khristu,” mu masiku otsiriza, koma “aphunzitsi abodza ndi mneneri wabodza.” Zindikirani kukhudza kwake! Tsopano ine ndikufuna inu kuti mufanizitse izi; ife tiribe nthawi yoti tiziwerengere izo apa, Mateyu 24:24 ndi Timoteo Wachiwiri 3:8.

Mateyu 24:24 anati, mu masiku otsiriza, onani, “Pamenepo adzabwera aKhristu abodza,” iwo odzozedwa, mwabodzawo, “aneneri abodza, ndipo adzasonyeza zizindikiro ndi zodabwitsa,” chimodzimodzi monga Mmodzi weniweniyo—Mmodzi weniweniyo, “ndipo adzatero—ndipo pafupifupi adzanyenga Osankhidwa omwe.” Tsopano zindikirani, ameneyo anali Yesu akuyankhula.

<sup>257</sup> Apa pakubwera Paulo, pambuyo pa Iye pomwe, ndipo anati, “Tsopano, mu masiku otsiriza, padzabwera anthu achipembedzo, onani, okhala nawo mawonekedwe aumulungu. Ndi kutsogolera akazi opusa, otengeka ndi mitundu yonse ya kusilira kwa chidziko.”

Ndipo iwo amadabwa, kumati, “Nchifukwa chiyani iwe umawatola akazi awo?” O, chifukwa chaubwino... Iwo samaziwona basi Zimenezo.

“Kutsogolera akazi opusa, olemedwa ndi zilakolako zosiyana,” kutali ndi zinthu monga pa... za... Mwaona, “Ndipo monga Yane ndi Yambre...”

Mateyu 24:24, “A Khristu abodza,” odzozedwa, mwabodza, kumachita zizindikiro ndi zodabwitsa kuti awanyenge Osankhidwa.

“Tsopano monga Yane ndi Yambre anamutsutsa Mose, chotero adzachita osokonezeka awa; a malingaliro osokonezeka

pazokhudza Chikhulupiriro.” Osati “ka” chikhulupiriro. “Chikhulupiriro!”

“Chikhulupiriro chimodzi, Ambuye mmodzi, umodzi uba-...” Inu simungakhoze kukhala ndi “Chikhulupiriro chimodzi” popanda kukhulupirira mwa “Ambuye mmodzi.” Inu simungakhoze kukhala ndi maubatizo awiri, ndipo osati umodzi wa Atate, ndi Mwana, Mzimu Woyera. “Ubatizo umodzi,” Yesu Khristu. Ndiko kulondola. Mwaona, ubatizo wabodza!

<sup>258</sup> Zindikirani, kazifanizireni izo palimodzi tsopano pamene inu mukafika kunyumba. Zindikirani Mateyu 24:24, Yesu akuyankhula; Paulo, Timoteo Wachiwiri 3:8; ena ambiri. Ndipo tsopano fanizitsani izo.

<sup>259</sup> Ndiyeno kuyikapo Lemba lina, Luka 17:30, Malaki 4.

“Monga Yane ndi Yambre anamutsutsa Mose,” Mawu odzozedwa a ora, “chomwecho adzakhala anthu awa,” osati munthu, “anthu,” iwo odzozedwawo, “kutsutsa Choonadi.”

<sup>260</sup> “Mu tsiku lomwelo limene Mwana wa munthu ali kuululidwa.” Chivumbulutso 10:1 mpaka 7, kawerengeni izo pamene inu mukafika kunyumba, “Uthenga wa mngelo wachisanu ndi chiwiri, kutsegula Zisindikizo.” Nchiyani chimenecho? Osati mngelo ndiye Mwana wa munthu; koma mtumiki akuulula Mwana wa munthu. Kodi inu mungakhoze kutengera izo pozilekanitsa tsopano? Ndi pamene zikuwoneka kukhala zolimba kwambiri kwa inu, inu mukuona. Osati Mwana wa munthu, Iyemwini; koma mngelo wachisanu ndi chiwiri, mtumiki wa chisanu ndi chiwiri, ali kuulula kwa anthu Mwana wa munthu, chifukwa Izo zachoka ku mankhusu. Iye sangakhoze kupanga bungwe Izo. Ndi Njere, Iyoyomwe, kachiwiri.

“Ndipo mu tsiku limenelo, Yane ndi Yambre adzatsutsa,” iwo odzozedwawo (odzipangitsa-kukhulupirira ndi osakhulupirira, mpingo mwamaonekedwe ndi Achipentekoste) akuyima motsutsa Njere yowona, “koma asiyeni iwo okha; kupusa kwawo kudzachita kuwonetseredwa, monga kwawo kunaliri.” Mwaona? Inu mukumvetsa tsopano? [Osonkhana, “Ameni.”—Mkonzi.]

<sup>261</sup> Chivumbulutso 10, anati, “Mu masiku a kuwomba kwa mngelo wachisanu ndi chiwiri.” Tsopano kumbukirani, wachisanu ndi chiwiri, M’badwo wa Mpingo wa Laodikaya. “Kuomba kwa mngelo ameneyo,” pamene m’badwo wa mpingo umenewo wachita kale chipembedzo ndi kukhala m’badwo wa mpingo, pamene izo zachitika mu bungwe lake la Chipentekoste; pamene mtumiki kwa umenewo. . .

Kodi mtumiki aliyense anali chiyani? Kodi Marteni Lutera anali chiyani? Chitsutso kwa Akatolika. Kodi Wesile anali chiyani? Chitsutso kwa Achilutera awo. Kodi Achipentekoste anali chiyani? Chitsutso kwa iwo enawo. Kodi Moyo wapita kuti tsopano? Kutali kuchoka ku bungwe. Palibenso mankhusu; ndi

Njere. Ndi chiyani chimenecho? Chitsutso kwa Achipentekoste, onani, kuti akakwaniritse Lemba la ora lino. Mwaona?

<sup>262</sup> Zindikirani, tsiku lomwelo pamene mtumiki uyu... Osati pamene iye akuyamba, koma pamene iye akuyamba kufalitsa Uthenga wake. Mwaona? Chikoka Choyamba, machiritso; Chikoka Chachiwiri, kunenera; Chikoka Chachitatu, kutsegula kwa Mawu, zinsinsi kuululidwa. Palibe zinanso, palibe dongosolo linanso lapamwamba loti liulule Mawu, kuposa aneneri. Koma njira yokha imene mneneri angati atsimikiziridwe ndi mwa Mawu. Ndipo, kumbukirani, Chikoka Chachitatu chinali kutsegula kwa Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri zija, kuti ziulule Choonadi chobisika chimene chasindikizidwa mu Mawu. Kodi inu muzikuona izo? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi.]

Ndi pamenepo, mu tsiku limenelo pamene chinthu ichi chiti chidzachitike, kuti Yane ndi Yambre, osanzira, ati adzaonekere kachiwiri. Monga momwe iwo anachitira pamene Mose anawonekera ndi Mawu apachiyambi, kuti awanene Iwo; iwo akuwonekera, kuti awasanzire Iwo. Chimodzimodzi basi molondola. Tsopano inu mukuona chimene Mateyu 24:24 ali? Onani, iwo odzozedwawo!

<sup>263</sup> Tsopano apo pali zinthu zitatu zimene ife titi tinene ife tisanati titseke. Izi ndi izo. Ine ndikufuna inu kuti mumvetsere mwatcheru kwenikweni tsopano pamene ife tikutseka. Zinthu zitatu, kumbukirani, zinthu zitatu zakwaniritsidwa kale. Zinthu zitatu zagona patsogolo panu pakali pano.

<sup>264</sup> Choyamba. Dziko liri mu chikhalidwe cha Sodomu. Yesu anati izo zikanadzachitika. Tayang'anani pa kusokoneza; akazi athu akuyesera kumachita monga amuna athu; amuna athu akuyesa kumachita monga akazi, achikazi; ovunda, auve, otsika-pansi, ogwidwa-ziwanda, ndipo sakudziwa izo. Baibulo linanena kuti izo zikanadzachitika, ndipo ndi pamene izo ziri.

<sup>265</sup> Chachiwiri. Ndi mu ora limenelo, malingana ndi Lemba apa, kuti Yane ndi Yambre akuwonekera. Chachiwiri.

<sup>266</sup> Chachitatu. Ziri mu ora lomwelo pamene Mwana wa munthu ati adzaululidwe.

<sup>267</sup> Apo pali wokhulupirira wanu, wodzipangitsa-kukhulupirira wanu, ndi wosakhulupirira wanu. Apo pali Mawu enieni atayima apo, otsimikiziridwa; apo pali wodzipangitsa-kukhulupirira akuwatsanzira Iwo; ndipo apo pali wosakhulupirira akukana chinthu chonsecho.

Koma kudzakhala Kuwala cha nthawi yamadzulo,  
Njira yaku Ulemerero inu mudzaipezadi  
(Kulondola uko?)

Mafuko akusweka, Israeli akuwuka,  
Zizindikiro Baibulo linalosera;  
Masiku a Amitundu akwanira (Sodomu), ndi  
zowopsya zachuluka.

Bwererani, O omwazika, kwanu.

Tsiku la chiwombolo layandikira,  
Mitima ya amuna ikulephera, mwa mantha;  
Dzazidwani ndi Mzimu wa Mulungu, konzani  
nyali zanu ziwale, (kuti inu mukhoze  
kumawona Mawu a orali,)

Yang'anani mmwamba, chiwombolo chanu  
chayandikira!

Aneneri abodza akunama, (iwo anati iwo  
adzakhalapo kuno; iwo odzozedwawo),  
Choonadi cha Mulungu akuchikana,  
Kuti Yesu Khristu ndi Mulungu wathu.

Ndicho, iwo sakuchikhulupirira Icho. Baibulo linati  
kudzakhala chinthu chimenecho kuno. Ndi ichi apa!

Koma tiziyenda kumene atumwi anayenda  
(Kuwala komweko! “Ndi kubwezeretsa  
Chikhulupiro cha atate kwa ana.”)

Tsiku la chiwombolo layandikira, pafupi  
kwambiri,

Mitima ya amuna ikulephera mwa mantha,  
(dziko lapansi likugwera mkati);

O, dzazidwani ndi Mzimu wa Mulungu,  
konzani nyali zanu ziwale.

Yang'anani mmwamba, chiwombolo chanu  
chayandikira.

Inu mukukhulupirira zimenezo? [Osonkhana akuti,  
“Ameni.”—Mkonzi.] Tiyeni ife tiweramitse mitu yathu ndiye.

<sup>268</sup> Kunja mu dziko kumene Uthenga uwu ukupita, kuchokera  
ku Chigwa cha Kummawa mpaka Kumadzulo, kuchokera ku  
California mpaka ku New York, kutsika mpaka Kummwera,  
kukwera mpaka Kumpoto, kunja mpaka ku mamishoni, ndi  
kulikonse kumene Iwo akupita, ndi mu Kachisi uyu. Ife ndife  
osauka. Ife tiribe zinthu zopambana izi, zazikulu, zamaluwa, ndi  
zowonetsa pa televizioni. Ife tikungoyesera kuchita chopambana  
chimene ife tingakhoze. “Koma onse amene Atate andipatsa Ine  
adzadza.”

<sup>269</sup> Tsopano, ine ndikufuna inu mudziwe kuti izi ndi  
zotsimikizika, ndi inu amene mukumvetsera ku tepi iyi. Inu  
mukanakhoza kuti munaganiza lero kuti ine ndinali kuyesa  
kunena izo zokhudza inemwini, pokhala kuti ine ndinali  
kunyamula Uthenga uwu. Ine ndiribe kenanso kochita nawo  
Iwo kuposa kalikonse, osati zoposa liwu chabe. Ndipo, liwu  
langa, ngakhale motsutsana ndi kuweruza kwanga kwabwino;



ine ndinkafuna kuti ndikhale mlenje. Koma ndi chifuniro cha Atate anga chimene ine ndikulengeza kuti ndizichita, ndipo ndatsimikiza kuti ndizichita.

Ine sindinali Mmodzi yemwe anawonekera kumusi pa mtsinje; ine ndinali kokha kuyima pamenepo pamene Iye anawonekera. Ine sindine Mmodzi yemwe amachita zinthu izi ndi kulosera zinthu izi zomwe zimachitika mwangwirowo momwe izo ziriri; ndine kokha mmodzi yemwe ndimakhala pafupi pamene Iye akuchita izo. Ine ndinali kokha liwuu limene Iye analigwiritsa ntchito, kuti azinene Izo. Izo sizinali Zimene ine ndinkazidziwa; ndi chimene ine ndinangodziperekako ndekha, chimene Iye anayankhulira kupyoleramo. Icho sindicho ine, uyo sanali mngelo wachisanu ndi chiwiri, o, ayi; iko kunali kuwonetseredwa kwa Mwana wa munthu. Uyo sanali mngelo, uthenga wake; icho chinali chinsinsi chimene Mulungu anachifutukula. Ameneyo si munthu; ndi Mulungu. Mngeloyo sanali Mwana wa munthu; iye anali mtumiki wochokera kwa Mwana wa munthu. Mwana wa munthu ndi Khristu; Iye ali Mmodzi yemwe inu mukudyapo. Inu simukudya pa munthu; munthu, mawu ake adzalephera. Koma inu mukudya pa Thupi la Mawu osalephera la Mwana wa munthu.

<sup>270</sup> Ngati inu simunadye mokwanira pa Mawu aliwonse, kuti mudzipatse nokha nyonga kuti mukauluke pamwamba pa zipembedzo zonse izi ndi zinthu za mdziko, kodi inu pa nthawi ino mungachite izo, pamene ife tikupemphera?

<sup>271</sup> Atate Wokondedwa, ichi ndi chinthu cholimba. Si chiri chophweka kuti wachivundi achite ichi. Inu mukudziwa zinthu zonse. Ndipo ine ndikukupemphani Inu, Mulungu Wokondedwa, kuti izo zisati zikhale zosamvetsedwa bwino. Koma, mwa Kuwala kwa Mawu Anu, mulole anthu aziyenda.

<sup>272</sup> Ndipo, Atate Mulungu, ine sindikudziwa yemwe Wosankhidwayo ali; Inu mukumudziwa. Ine sindikudziwa pamene Kudza Kwanu kuli. Koma ine ndikungodziwa kuti Inu munati pamene izi ziti zizidzachitika, iwo odzozedwawo, mwabodza awa; osati pamene iwo anayamba kumene.

Mose anangowasiya iwo okha, pakuti iye sakanakhoza kuchita chinanso za izo. Iye akanakhoza kokha kunena zimene Inu munali kunena. Inu munamuuza iye kuti aitane utitiri; ndiye iwo anayitananso izo. Inu munamuuza iye kuti asandutse madzi kukhala magazi; ndiye iwo anachita izo. Mose ankangochita kokha, Mawu ndi Mawu, monga Inu munanenera, koma ndiye Inu munali Mmodzi Yemwe munachititsa kupusa kuwonetseredwa.

<sup>273</sup> Tsopano, Atate, Ndinu Mulungu, panobe. Mawu omwewo ananena kuti izi zikanadzachitika mu masiku otsiriza. Anthu ambiri owonamtima, monga ife tinanena Lamlungu lapita, akuyika dzanja lawo pa Likasa ilo liri pa ngolo yatsopano, ndipo

osati mapewa a Alevi, amene agwa nafa, “akufa mu tchimo ndi zolakwika,” akutsutsa mokangana ndi chikumbuntima chawo chomwe.

<sup>274</sup> Atumiki ambiri atakhala mowerenga mwawo, amawerenga Mawu amenewo, ndi kusintha pa tsambalo mwamsanga; kuwopa kuti angakhale ndi kuphulitsidwa pamenepo, kudziwa kuti angataye kuyima kwawo kwachitukuko ndi anthu, ndi mpingo wake ndi chipembedzo chake. Mulungu mutithandize ife kusachita konse izo!

<sup>275</sup> Yeretsani mtima wathu, Ambuye, kuchokera ku zonyansa zonse za mdziko. Ambuye, ine ndikuyima wokonzekera kutsukidwa. Ine ndikuima wokonzeka, ndi mpingo uwu ndi onse amene akumvetsera izi, ndi aliyense amene ati adzamvetsere kwa tepi iyi. Ine ndikuyima, Ambuye, ndikupempha kutsuka. Ambuye, nditengereni ine kunyumba ya woumba ndipo kandisweni ine uko, ndiwumbeni ine wantchito yemwe Inu mungamfune.

Pakuti, Ambuye Yesu, “Ine ndine munthu wa milomo yosayera,” monga Yesaya analirira, “ndimakhala ndi anthu a milomo yosayera; ndipo watsoka ndi ine, pakuti ine ndikuwona vumbulutso la Mulungu akuchita kuwonetseredwa,” monga Yesaya anawaona Angelo mu Kachisi. Ine ndikuona nthawi yotsiriza, Ambuye, ndipo watsoka ndi ine ndi banja langa; watsoka ndi ine ndi anthu anga. O Mulungu wamuyaya, chitirani chifundo pa ife. Ine ndikudzichonderera kwa ndekha ndi anthu. Musalole ife kuti tiwonongeke ndi iwo amene sali kukhulupirira, koma mulole ife tikhale ndi okhulupirira.

<sup>276</sup> Chipembedzo chirichonse, Ambuye, mwamuna aliyense kapena mkazi...ine sindingakhoze kukufunsani Inu kuti mudalitse chipembedzo, pamene ine ndikudziwa kuti Inu ndinu wotsutsana nacho icho. Koma ine ndingakhoze kunena kokha kuti, Ambuye, ngati Inu muli nayo iliyonse ya nkhosa Zanu kunja pakati pa iwo, mulole iwo ayimve tepi iyi. Mulole iwo ayimve Iyo, Ambuye, ndi kuyimvetsa Iyo ndi kumvetsa kumene Inu muti mudzawapatse iwo, ndipo mulole iwo akatulukemo ndi kukulandirani Inu. Mulole iwo asati akhale onyengedwa ndi khungu ndi mwambo wa tsiku lino. Musalole iwo kuti akayesere kudya chinachake chimene...kapena imene inali nyama mu tsiku lina. Mulole iwo atenge Mawu.

Ndimomomwe Afarisi anakupachikirani Inu, Ambuye. Iwo anali akutenga mtembo wa tsiku la Mose, ndi kumaumeza iwo; mutatha Inu kupereka choyimira, mu chipululu, cha manna atsopano usiku uliwonse, kutanthauza m’badwo uliwonse. Ndi pamene iwo analepherera. Icho chinawadyetsa iwo chiphe. Icho chinawapha iwo, kudya chakuyda chovunda chimenecho.

Ndipo, mwauzimu, icho chikuchita chinthu chomwecho lero; kuwapha iwo, mwauzimu, ndi chipembedzo.

Tithandizeni ife, Mulungu Wokonededwa. Izo zonse ziri mmanja Anu tsopano. Mu Dzina la Yesu Khristu.

<sup>277</sup> Ndi mitu yathu yoweramitsidwa, ife tikuti tiyimbe ija pamene inu mukupanga lingaliro lanu. Kodi inu mupita njira yonse?

Ndikukhoza kumumva Mpulu... (ndipo Iye ali Mawu)...-mutsi wanga akuitana, Ndikukhoza kumumva...

“O, ine ndalowerera nthawi yaitali, koma, kwenikweni, pakali pano ine ndikumumva Iye, ‘Bwerani kwa Ine, nonse inu amene mukupwaira konseko.’ Mverani, ‘tengani mtanda wanu nditsateni Ine tsiku ndi tsiku.’ ‘Eya, ngakhale ine ndingayende kupyola m’chigwa cha mthunzi wa imfa, ine sindidzawopa choyipa ayi; mmusi kupyola mu msipu wobiriwira wa mu mthunzi, ndi mmbali mwa madzi odikha.’”

Ndipo kumene Iye anditsogolera ine...

“Ambuye, ine ndikuwona kupusa kwa utatu uwo. Ine ndikuwona dziko lonse likufesedweramo; maudzu akumera paliponse. Koma kumene Inu munditsogolera ine tsopano, Ambuye, ine ndidzakhala monga ajawa mu Machitidwe 19. ‘Pamene iwo anamva Ichi, iwo anabatizidwanso mu Dzina la Yesu Khristu.’”

...tsatira, (“ine ndapita gawo la njirayo, Ambuye, kokwanira kuti ndikulandireni Inu.”)

Tsopano ndidzapita ndi Iye njira yonse.

[M’bale Branham ayamba kung’ung’uza *Kumene Iye Anditsogolera Ine*—Mkonzi.]

<sup>278</sup> Mulungu Wokonededwa, ine ndikudalira kuti izo zikubwera kuchokera mu mtima wanga. Ine ndikudalira kuti izo zikubwera kuchokera mu mtima wa aliyense yemwe akuyima pa nthawi ino, mwinamwake ambiri omwe ati adzamve tepi iyi, amene palibe pano kapena amene sali kumva izi tsopano. Mulole ife tikhale lolera, Ambuye, mosalabadira mtengo wake. Munati, “Monga munthu wopita kukakomana ndi ankhondo ena, msilikari, mfumu; choyamba iye amakhala pansu ndi kuwerengera, kodi iye ali wokhoza kuti achite izo, kodi iye angakhoze kuzisiya zinthu za mdziko? Kodi inu mungakhoze kuzisiya, kulowa mu ankhondo a Mawu olembedwa a Mulungu; kumaguba ndi asilikari Ake, kumauluka ndi mphungu Zake?” Perekani izo, Ambuye, mu Dzina la Yesu.

<sup>279</sup> Inu mukukhulupirira? Kodi inu mukumuvomereza Iye? Chabwino. Ife tidzakuonani inu kuno kachiwiri, usikuuno, Ambuye akalola. Kodi inu mukukhulupirira izo kukhala Choonadi? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Kodi izo ndi zomveka mokwanira? [“Ameni.”]

Tenga Dzina la Yesu nawe,  
Mwana wosauka ndi watsoka;  
Ilo lidzakusangalatsa ndi kukutonhoza,  
Litenge ilo kuli- . . .

Tsopano, gwiranani chanza ndi winawake wapafupi nanu tsopano.

Dzina lofunika, O lokoma bwanji!  
Chiyembekezo cha padziko, chiyembekezo cha  
padziko, chimwemwe cha Kumwamba;  
Dzina lofunika, O lokoma bwanji!  
Chiyembekezo cha padziko ndi chimwemwe  
cha Kumwamba.

Pa Dzina la Yesu kugwada,  
Kugwera pa mapazi Ake,  
Mfumumu ya mafumu Kumwamba tidzamuveka  
korona . . . (Iye ndi Mulungu, ndiye)  
Ulendo wathu ukadzatha.

Dzina lofunika, Dzina lofunika, O lokoma  
bwanji! O lokoma bwanji!  
Chiyembekezo cha padziko ndi chimwemwe  
cha Kumwamba;  
Dzina lofunika, O lokoma bwanji!  
Chiyembekezo cha padziko ndi chimwemwe  
cha Kumwamba.

<sup>280</sup> Ine ndikuganiza kuti atumiki onse anadziwidwa mmawawu, kuzindikiridwa.

Pamene munthu wapemphera sabata lonse, kudabwa nchiyani, powona Malemba awa, iwo akuyima kumene pamaso pako. “Tsoka kwa ine,” anatero Paulo, “ngati ine sindilalikira Uthenga.” Pa mapeto a ulendo wake, iye anati, “Ine sindinazembe kufotokoza kwa inu Uphungu wonse wa Mulungu monga Iwo unapatsidwa kwa ine.”

<sup>281</sup> Ine ndimayiwala nthawizina kuzindikira zinthu, kuwapereka, kuti tiwadalitse ana.

Billy ananena, tsiku lina, mwamuna anabwera, anati, “Ine ndakhala ndikubwera kuno kwa zaka ziwiri, kuti ndidzamudalitsitse mwana wanga.”

Billy anati, “Musati muziganiza moyipa za izo. Ine ndiri ndi mwana, wa usinkhu wa chaka, ndipo iye sanadalitsidwe, panobe. Kotero ine ndingoyembekezera mpaka iye atakula mokwanira kuti adzayende kupita apo yekha, ine ndikuganiza.”

<sup>282</sup> Kotero ife timapeza m’bale, mlongo, sindizo—sindizo, onani, ine. . . Chinthu chimodzi, ife tiyenera kumawadalitsitsa ana athu.

Ife tiyenera kumabatiza wina aliyense. Apo pali dziwe; pano pali madzi. Ngati inu simunateropo, nchiyani

chikukulepheretsani inu? Pano pali madzi. Bwerani pakali pano. Musati muyembekezere mpaka usikuuno; bwerani pakali pano. Pali munthu amene wayima apa ati abatize aliyense yemwe walapa ndi kupanga kuvomereza. Ngati inu mwabatizidwapo ka khumi ndi kawiri, iwo akubatzani inu mu Dzina la Yesu Khristu kwa chikhululukiro cha tchimo. Mwaona? Ife tiri nazo izo.

<sup>283</sup> Koma, onani, Uthenga uli pa mtima wanga. Ine ndiyenera kuwutulutsa Iwo. Ndicho cholinga changa chokhacho, mosalabadira zimene akazi anga anena, ana anga anena, abusa anga anena, changa chirichonse chimene chinena. Ndi Ambuye wanga. Ine ndiyenera ndiwukulutsira Iwo kunjja. Ndicho cholinga changa chokhacho.

<sup>284</sup> Ndipo tsopano, nthawi zambiri, ine ndimayiwala kuwazindikira atumiki. Ine ndikuganiza mwinamwake... m'bale wathu, M'bale Neville, munthu wofunika. Abale ena awa pano, ife tiri okondwa kukhala nanu.

<sup>285</sup> Osati kuti ife timatsutsana nanu inu, m'bale, kuti tikhale osiyana. Ena a inu pano mukhoza kukhala alaliki autatu. Ife sitikufuna kukhala okwiya ndi inu. Ife timakukondani inu. Ngati ife tikanati tisanatero, ngati ine ndikanati ndisamakulupirire zimenezo, ine sindikanachoka pa mpingo uno mpaka ine nditafika pansi apo pa maondo anga ndi kuti, "Mulungu, ndipangeni ine mokhoza."

Ine sindikufuna mzimu wamwano uwo, wodzikonda kuti usanganikirane ndi wanga. Ine ndikufuna mzimu wanga kuti ukhale wangwiro ndi woyera, chikondi cha pa abale, woyera ndi Mzimu Woyera. Tsopano, ngati winawake achita chirichonse cholakwika kwa ine, zonsezo nzabwino. Ndipo ngati ine ndingakhale nawo ufulu kuti ndibwezere pa iwo, ine sindikufuna izo mu mtima wanga. Ayi, ine—ine ndikufuna kukhala ndi chikondi. Ine ndikufuna kukhala wokonzeka kukonza ndi chikondi, ndi chikondi chimene mwamtheradi chimayankhira kunjja uko kwa icho.

<sup>286</sup> Ine sindikutanthauza kukhala wosiyana. Amethodisti, Abaptisti, Akatolika, Apresbateria, yense yemwe inu muli, ine sindikunena zinthu izi kuti ndikhale wosiyana, kukhala wamwano ndi inu. Ngati ine ndikanatero, ndine wachinyengo ndipo ndiyenera kukhala pansi apa pa guwa ili, ndikupemphera mopyola kwa Mulungu.

Koma ine ndikunena izo, ndi chifukwa cha chikondi, ndipo ine ndikuwona kumene inu mukupita. Tsopano, ine sindikunena izi mwa ndekha, ndi kunena kuti ine ndikupenekera. Ine ndikukupatsani inu PAKUTI ATERO AMBUYE. Ichu ndi Chionazi. Ndipo ine ndikukondani inu chifukwa cha zinthu zimenezo. Mulungu akudalitseni inu.

<sup>287</sup> Tsopano pamene ife tikuyimba ndime yina ya nyimbo iyi, tiyeni, ife tisanapite. Ife tikufuna inu mudzakhale pano

usikuuno, ngati inu mungathe. Ngati inu simungathe, Mulungu akhale ndi inu kufikira titadzawonananso. Ife tingopemphera kuti Mulungu a—akudalitseni inu ndi kukupatsani inu zopambana za dziko Lake, mwaona.

Tenga Dzina la Yesu . . .



*IWO ODZOZEDWAWO PA NTHAWI YOTSIRIZA* CHA65-0725M  
(The Anointed Ones At The End Time)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham wolalikiidwa mu Chingelezi pa Lamlungu mmawa, Julaye 25, 1965, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingelezi. Kumasulira uku kwa Chichewa kunadindidwa mchaka cha 1996 ndi Voice of God Recordings.

CHICHEWA

©1996 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)